

***KAFUKUFUKA***  
***WA***  
***CHIPANGANO CHATSOPANO***

**HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

@Harvestime International Institute

**ZAMKATI MWA BUKULI**

## ZAMKATI MWA BUKULI

Kagwiritsidwe Ntchito Ka Bukuli.....	3
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu.....	4
Mau Oyamba.....	5
Zolinga za Maphunzirowa.....	6

### CHIPANGANO CHATSOPANO

Mau Oyamba a Mauthenga Abwino.....	7
1. Mateyu.....	8
2. Marko.....	20
3. Luka.....	26
4. Yohane.....	33
Mawu Oyamba a buku la Mbiri.....	46
5. Machitidwe.....	47
Mawu Oyamba a Makalata.....	63
6. Aroma.....	66
7. I ndi II Akorinto.....	81
8. Agalatiya.....	105
9. Aefeso.....	113
10. Afilipi.....	124
11. Akolose.....	131
12. I ndi II Atesalonika.....	142
13. I ndi II Timoteo.....	154
14. Tito.....	171
15. Filemoni.....	178
16. Ahebri.....	182
17. Yakobo.....	190
18. I ndi II Petro.....	199
19. I, II, ndi III Yohane.....	210
20. Yuda.....	220
Mawu Oyamba a Buku La Uneneri.....	226
21. Chibvumbulutso.....	227
Mayankho a Mafunso Odziyetsa Nokha.....	236

## **KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKULI**

### **KAKONZEDWE KA BUKULI**

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga:** Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welangani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo:** Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulemamba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

### **ZOWERENGA ZINA ZOFUNIKA POPHUNZIRA PHUNZIROLI**

Mudzafunikira Buku Lopatulika

## NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

### MKUMANO WOYAMBA

**Kutsekulira:** Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Nchito Yoyamba.** Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

### MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira:** Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipereze okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina ali yense ali ndi buku laphunziroli.

## **PHUNZIRO: KAFUKUFUKU WA BAIBULO**

### **MAWU OYAMBA**

Mau ambiri a mu Chipangano Chakale amene Ambuye adawalankhula munthawi ya utumiki wawo wa pansi pano anaonetsera kufunikira kwa chimene Malemba akufotokoza. Pachifukwa chokhachi chotsindika kufunikira kwa Mau a Mulungu kwa ophunzira ake, Harvestime International yabwera ndi phunziro lokuti, “Kafukufuku wa Baibulo,” ngati dongosolo la maphunziro okonzekeretsa atumiki kuti akathe kufikira anthu amitundu yonse ndi Mau a Mulungu.

Gawo loyamba la “Kawuniwuni wa Baibulo” akuonetsera Baibulo ndi matanthauzidwe ake mu malembedwe osiyanasiyana. Akupereka chithunzithunzi cha mbiri ya Mbaibulo, malo ndi moyo wake mmene unalili munthawi imene kunali Baibulo. Komanso kawuniwuniyi akuphunzitsa magawo a maluso ndi magawo a mabuku onse opezeka Mchipangano Chakale.

Buku ili, limene ndi gawo lachiwiri, likupitiliza phunziroli poona mndandanda wa buku lililonse la Mchipangano Chatsopano. Zina mwa nkhani zomwe zikupezeka za olemba buku, anthu mwe amawalemberea, cholinga chomwe amalemberea buku, ndime zikuluzikulu, mndandanda wa anthu omwe alimo ndi magawo a zopezeka mkatimo.

Moyo ndi Mfundo za utumiki pa buku lililonse zalembedwanso. Mfundo zimenezi ndi choonadi chotheratu pa kukula kwa Mkhrisitu ndi utumiki zimene muyenera kuzilondola ndi kuzikhazikitsa mmoyo wanu.

“Kawuniwuni wa Baibulo ndi phunziro limene limagwirizana ndi phunziro la “Njira zatsopano zophunzirira Baibulo” zimene zimaphunzitsa njira zambiri zophunzirira Baibulo. Maphunziro onsewa akonzedwa ndi cholinga mwayi wapaderadera wophunzira Mawu a Mulungu.

## ZOLINGA ZA PHUNZIROLI

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kupanga ndi kutambasula magawo a mabuku a Chipangano Chatsopano.
- Kutchula mu buku lililonse
  - Wolemba buku
  - Kwa amene amawalemba
  - Nthawi yomwe linalembedwa
  - Cholinga cha buku
  - Vesi lotsogolera
  - Moyo ndi Mfundo ya utumiki
- Kupitiliza kuphunzira Mawu a Mulungu mwatsatanetsatane mukamaliza phunziroli.

## MAWU OYAMBA A MAUTHENGA ABWINO

Mabuku oyambirira anayi Mchipangano Chatsopano ndi mauthenga. Mabuku amenewa ali ndi mbiri ya kubadwa, moyo, utumuki, ziphunzitso, imfa ndi kuuka kwa Yesu Khristu. Njira za buku lililonse ndi zosiyana:

**Mateyu:** Bukuli limamutchula Yesu ngati mfumu ya a Yuda. Ndipo koyamba ndi mndandanda wa makolo ake a Yesu. Ndipo mathero ake akuonetsa Yesu ngati mfumu akutuma ophunzira.

**Marko:** Bukuli limamutchula Yesu ngati mtumiki wa Mulungu kwa anthu amtundu wa Chiroma. Bukuli silikambapo za mndandanda wa makolo a Yesu chifukwa chakuti Yesu akuonetseredwa ngati mtumiki wa Mulungu ndipo palibe amene anaonetsa chidwi pa mbiri ya ubwino wake ngati mtumiki.

**Luka:** Mubuku ili Yesu akuonetseredwa ngati “Mwana wa Munthu” munthu wangwiro ndi mpulumutsi wa anthu ochimwa. Ndime 3 ya Luka akukamba za makolo a Yesu kuchokera kwa Adamu. Ndipo bukuli likumalizira ndi munthu wangwiro ameneyi, Yesu akukwera Kumwamba kwa Atate wake.

**Yohane:** Amakamba za Yesu ngati Mwana wa Mulungu monga mwa ulamuliro wake. Bukuli limayamba kufotokoza za Yesu ngati Mawu a Mulungu ovumbulutsidwa. Ndipo ndime yomaliza ya bukuli imaonetsa kuti dziko silikanakwanitsa kudziwa zonse za utumiki wake wa padziko lapansi. Uwu ndi umboni wapadera kuti analidi Mwana wa Mulungu.

## MAGULU A CHIYUDA

A Yuda omwe analipo munthawi ya Chipangano Chatsopano anali mmagulu osiyana. Magulu awa ndi amene akupezeka mmabuku a Mauthenga:

**Afalisi:** Awa chipembedzo chawo chinakhazikika pa kumvera lamulo limene linanthauzidwa, kutambasulidwa, ndi kulimbikitsidwa kuti litsatidwe. Iwowa samatsatira malalamulo olembedwa okha komanso amatsatira miyambo ya tsiku ndi tsiku imene imaphunzitsidwa kufikira mibado mibado. A Yuda ambiri anali Afalisi ndipo ochitachita. Iwowa amakhulupirira za kuukakwa akufa.

**Asaduki:** Ili linali gulu la ulamuliro limene silimakhulupirira za kuuka kwa akufa. Amakhulupirira ziphunzitso zolembedwa mchilamulo osati zongolankhulidwa. Iwowa anali mbali imodzi ya ulamuliro wa Chiloma umene umalamulira Isalayeli munthawi ya Yesu.

**Esenisi:** Ili lidali gulu lina la Chiyuda limene la malamulo ndipo limayembekezera kuti a Mesiya abwera awiri. Gulu

**Zelote:** Gulu ili limavomereza ziwawa pofuna kubweretsa mtendere munthawi ya ulamuliro wa Chiroma.

## CHAPUTALA CHA 1

### MATEYU

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Mateyu.
- Kuzindikira omwe wolemba buku la Mateyu amawalemba.
- Kutchula cholinga cha buku la Mateyu.
- Kulemba ndime zikuluzikulu za buku la Mateyu.
- Kutchula moyo ndi mfundo za utumiki za buku la Mateyu.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Mateyu

**OMWE AMAWALEMBERA:** Kwa onse okhulupirira, ngakhale oyambirira anali a Yuda amene anawaonetsera Yesu ngati Mesiya, Mwana wa Davide.

**CHOLINGA:** Kuonetsa utumiki was Yesu, potsindika za ntchito yake ngati Mfumu ya a Yuda.

**VESI LOTSOGOLERA:** Mateyu 28: 19-20

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Lamulo lotsiliza la Yesu kwa ophunzira linali kulalikira uthenga kwa anthu amitundu yonse.

**ANTHU OPEZEKA M'BUKULI:** Yesu, ophunzira khumi ndi awiri.

### MAGAWO

#### Gawo Loyamba: Mndandanda wa makolo a Mfumu 1:1-17

- I. Mawu oyamba 1:1
- II. Mndandanda wa anthu 1:2-16
- III. Dongosolo la mndandanda 1:17

#### Gawo Lachiwiri: Kubadwa kwa Mfumu 1:18-2:23

- I. Kutenga pakati: 1:18-23
- II. Kubadwa: 1:24-25
- III. Zomwe zinzchitika kutsatira kubadwa: 2:1-23
  - A. Kuyenderedwa ndi amnzeru akummawa ndi chiwembu cha Herode: 2:1-12



- B. Kuthawira ku Aigupto: 2:13-15
- C. Chipongwe cha Herodi: 2:16-18
- D. Kubwerera kwawo ku Nazareti: 2:19-23

**Gawo Lachitatu: Kukonzekera 3:1-4:11**

- I. Kukonzekera kubwera kwa Mfumu: 3: 1-17
  - A. Utumiki ndi uthenga wa Yohane Mbatizi: 3:1-12
  - B. Ubatizo wa Mfumu: 3:13-17
- II. Kukonzekera kwa Mfumu: 4:1-11
  - A. Satana alimbana ndi umunthu wake: 4:1-4
  - B. Satana alimbana ndi umulungu wake: 4:5-7
  - C. Satana alimbana ndi umbuye wake: 4:8-11

**Gawo Lachinayi: Utumiki wa Mfumu ku Galileya 4:12-13:58**

- I. Kulapa machimo: 4:12-17
- II. Asodzi anayi ayitanidwa kukhala ophunzira: 4:18-22
- III. Chipambano ndi kutchuka koyamba: 4:23-25
- IV. Makhalidwe oyenera a mbadwa mu Ufumu: 5:1-7:28
  - A. Kaganizidwe ka mbadwa mu Ufumu: 5:1-12
  - B. Umboni wa mbadwa za Ufumu: Kuunika ndi mchere: 5:13-16
  - C. Mfundo za Ufumu mogwirizana ndi chilamulo ndi aneneri: 5:17-48
    - 1. Malamulo a Mulungu: 5:17-20
    - 2. Lamulo latsopano: 5:21-48
      - a. Kupha: 5:21-26
      - b. Chigololo: 5:27-30
      - c. Kulekana: 5:31-32
      - d. Malumbiro: 5:33-37
      - e. Makhalidwe ndi anthu ena: 5:38-48
  - D. Kaganizidwe katatu ka mu Ufumu: 6:1-18
    - 1. Kupereka: Maonekedwe akunja: 6:1-4
    - 2. Kupemphera: Maonekedwe a mmwamba: 6:5-15
    - 3. Kusala kudya: Maonekedwe amkati: 6:16-18
  - E. Zinthu zoyambirira za mbadwa za Ufumu: 6:19-33
    - 1. Mogwirizana ndi mtengo wake: 6:19-21
    - 2. Mogwirizana ndi ntchito yake: 6:22-24
    - 3. Mogwirizana ndi zofuna za kuthupi: 6:25-34
    - 4. Chofunikira chapamwamba: Ufumu: 6:33
  - F. Makhalidwe oyenera a mbadwa za Ufumu: 7:1-29

1. Kuweruza: 7:1-5
  2. Kusamalira choyera: 7:6
  3. Pemphero: 7:7-12
    - a. Mitundu itatu ya pemphero: kupempha, kufuna, kugogoda: 7:7-8
    - b. Kusiyana kwa mayankho a pakati pa atate a kudziko ndi Atate a Kumwamba: 7:9-11
- G. Malangizo apadera a mbadwa za Ufumu: 7:13-29
1. Zipata ziwiri: 7:13-14
  2. Aneneri onyenga: 7:15-20
  3. Chizindikiro cha munthu wa Mulungu: kuchita chifuniro Chake: 7:21-23
  4. Kusiyana pakati pa ochenjera ndi opusa: 7:24-27
- H. Kudabwitsa kwa chiphunzitso cha Yesu: 7:28-29
- V. Ulamuliro wa Mfumu: 8:1-9:38
- A. Ulamuliro pa nthenda: 8:1-17
    1. Kuchiritsidwa kwa wodwala khate: 8:1-4
    2. Kuchiritsidwa kwa kapolo wa Kenturiyo: 8:5-13
    3. Kuchiritsidwa kwa mpongozi wake wa Petro: 8:14-15
    4. Kuchiritsa matenda osiyanasiyana: 8:16-17
  - B. Ulamuliro pa ophunzira ake: 8:18-22
  - C. Ulamuliro pa zinthu za chilengedwe: 8:23-27
  - D. Ulamuliro pa ziwanda: 8:28-34
  - E. Ulamuliro pa tchimo: 9:1-8
  - F. Ulamuliro pa anthu: 9:9-17
    1. Kuitanidwa kwa Mateyu: 9:9
    2. Kudya ndi ochimwa: 9:10-13
    3. Kuyankha chinthu chovuta: 9:14-17
  - G. Ulamuliro pa imfa: Mwana wa mkazi wa Yairo: 9:18-19,23-26
  - H. Ulamuliro pa zokhuza thupi la munthu: 9:20-38
    1. Mzimayi wa nthenda ya mwazi: 9:20-22
    2. Khungu: 9:27-31
    3. Kusamva ndi kudzazidwa ndi ziwanda: 9:32-34
    4. Chifundo cha Yesu: 9:35-38
- VI. Kutumidwa ndi mfumu: 10:1-42
- A. Ulamuliro wa ophunzira khumi ndi awiri: 10:1-4
  - B. Malangizo a paulendo: 10:5-42

1. Komwe akuyenera kupita: 10:5-6
2. Utumiki: 10:7-8
3. Malangizo a katundu: 10:9-15
4. Malangizo a uzimu: 10:16-42

VII. Malingaliro pa Ufumu: 11:1-30

- A. Kusamvetsetsa Ufumu: 11:1-11
- B. Kusokonezedwa kwa Ufumu: 11:12-19
- C. Kukanidwa kwa Ufumu: 11:20-24
- D. Kulandiridwa kwa Ufumu: 11:25-30

VIII. Mikangano ndi Afalisi: 12:1-14

- A. Kukolola la Sabata: 12:1-8
- B. Kuchiritsa la Sabata: 12:9-13
- C. Zotsatira zake: 12:14-21

IX. Tchimo losakhululikidwa: 12:22-37

X. Yankho la Yesu ku mafunso a Afalisi: 12:38-45

XI. Kufunikira kwa za uzimu kuposa za thupi mu ufumu: 12:46-50

XII. Mafanizo a Ufumu: 13:1-53

- A. Fanizo la ofesa: 13:1-9
- B. Chifukwa chogwiritsa ntchito mafanizo: 13:10-17
- C. Tanthauzo la fanizo la ofesa: 13:18-23
- D. Fanizo la nansongole: 13:24-30
- E. Fanizo la kambewu ka mpiru: 13:31-32
- F. Fanizo la chotupisa mkate: 13:33
- G. Chidule cha mafanizo: 13:34-35
- H. Tanthauzo la fanizo la nansongole: 13:36-43
- I. Fanizo la chuma chobisika mmunda: 13:44
- J. Fanizo la ngale za mtengo wapatali: 13:45-46
- K. Fanizo la khoka loponyedwa mnyanja: 13:47-50
- L. Mawu omaliza okhuza mafanizo: 13:51-52

XIII. Kulandiridwa kwa Mfumu mdera la kwawo: 13:53-58

**Gawo lachisanu: Utumiki mmagawo oyandikana ndi Galileya 14:1-18:35**

- I. Imfa ya Yohane Mbatizi: 14:1-12

II. kuchoka kwa Yesu kupita kuchipululu: 14:13-15:20

- A. Kudyetsa anthu zikwi zisanu: 14:13-21
- B. Kutsatira mkate ndi nsomba: 14:22-23
- C. Kuyenda pa Nyanja: 14:24-33
- D. Utumiki ku Genesareti: 14:34-36
- E. Kukangana ndi Afalisi ndi Alembi: 15:1-20

- III. Yesu achoka ku Turo ndi Sidoni: 15:21-28
- A. Azimayi aku Turo ndi Sidoni: 15:21-28

- IV. Yesu achoka ku dera la Dekapolisi: 15:29-38
- A. Utumiki wochiritsa mphepete mwa Nyanja ya Galileya: 15:20-31
  - B. Kudyetsa anthu zikwi zinayi: 15:32-38

- V. Utumiki ku dera la Magadani: 15:39-16:4

- VI. Awachenjeza ophunzira za Afalisi ndi Asaduki: 16:5-12

- A. Kufunafuna chizindikiro: 16:1-4
- B. Awachenjeza za chiphunzitso: 16:5-12

- VII. Kuchoka ku Kayesareya wa Filipo: 16:13-17:21
- A. Kuyesa ophunzira: 16:13-20
  - B. Kulengeza za imfa, kuuka ndi kubweranso: 16:21-28
  - C. Mawalitsidwe a paphiri: 17:1-13
  - D. Kuchiritsa wodwala khunyu: 17:14-20

- VIII. Kupita ku Galileya: 17:22-18:35
- A. Kukumbutsa za imfa ndi kuuka: 17:22-23
  - B. Kupereka nsonkho: 17:24-27
  - C. Phunziro la wamkulu: 18:1-6
  - D. Machenjezo pa zolakwitsa: 18:7-9
  - E. Fanizo la nkhosa yosochera: 18:10-14
  - F. Kuthetsa mikangano pakati pa mbadwa za Ufumu: 18:15-35
    - 1. Mathetsedwe a mikangano: 18:15-17
    - 2. Udindo ndi mwayi wa mbadwa za Ufumu: 18:18-20

3. Funso la kukhulukira: 18:21-22
4. Mfumu ndi angongole ake: 18:23-35

**Gawo lachisanu ndi chimodzi: Utumiki wa Mfumu yak u Pereya: 19:1-20:34**

- I. Kuchiritsa makamu ku Yudeya: 19:1-2
- II. Funso lokhuzana ndi zakulekana: 19:3-12
- III Yesu adalitsa tiwana: 19:13-15
- IV. Kucheza ndi mwini chuma: 19:16-22
- V. Zotsamwiza za chuma: 19:23-30
- VI. Fanizo la mwini nyumba: 20:1-16
- VII. Za imfa ndi kuuka kwake: 20:17-19
- VIII Pempho la mzimayi wozikonda: 20:20-28
- XI Akhungu awiri achiritsidwa ku Yeriko: 20:29-34

**Gawo Lachisanu ndi chiwiri: Sabata yomaliza ya Mfumu 21:1-27:31**

- I. Yesu alowa mu Yerusalemu: 21:1-11
- II. Kuyetsedwa kwa Kachisi: 21:12-17
- III. Mtengo wa mkuyu utembereredwa: 21:18-22
- IV. Afunsa za ulamuliro wake: 21:23-32
- V. Fanizo la olima munda wa mpesa: 21:33-46
- VI. Fanizo la phwando la ukwati: 22:1-14
- VII. Mafunso ofuna kupepusa Yesu: 22:15-45
  - A. Za kupereka msonkho kwa Kayesala: 22:15-22
  - B. Za kuuka kwa akufa: 22:23-33
  - C. Za lamulo lalikulu loposa onse: 22:34-40
  - D. Za zokhuza Yesu mwini: 22:41-46
- VIII. Kukambirana zokhuza Afalisi ndi Asaduki: 23:1-39

- A. Amanamizira ulamuliro pa chimpembedzo: 23:1-3
- B. Amasenzetsa katundu olemera: 23:4
- C. Amapempha matamando: 23:5-7
- D. Malangizo kwa ophunzira ake: 23:8-12
- E. Tsoka kwa Alembi ndi Afalisi: 23:13-36
- F. Kulilira Yerusalemu: 23:37-39

IX. Tsogolo la Ufumu: 24:1-25:46

- A. Kuonongeka kwa kachisi: 24:1-2
- B. Zizindikiro za masiku otsiriza: 23:3-14
- C. Nthawi ya chisautso: 24:15-22
- D. Kubweranso kwa Yesu: 24:23-31
- E. Fanizo la mtengo wamkuyu: 24:32-35
- F. Tsiku la Ambuye: 24:36-40
- G. Lamulo la kudikira: 24:42-51
- H. Mafanizo a masiku otsiriza: 25:1-46
  - 1. Anamwali khumi: 25:1-13
  - 2. Matalente: 25:14-30
  - 3. Nkhosa ndi mbuzi: 25:31-46

X. Zochitika asanapachikidwe: 26:1-27:31

- A. Kulengeza za imfa yake: 26:1-2
- B. Upo wofuna kupha Yesu: 26:3-5
- C. Kudzodzedwa kuti amuike mmanda: 26:6-13
- D. Yudasi avomereza zompereka Yesu: 26:14-16
- E. Mgonero wotsiriza: 26:17-19
  - 1. Kukonzekera Pasaka: 26:20-29
  - 2. Mgonero otsiriza: 26:20-29
  - 3. Yesu amuchenjeza Petulo pa kudzitamandira: 26:30-35
- F. Mgetsemane: 26:36-46
- G. Kuperekedwa ndi kumangidwa kwa Yesu: 26:47-56
- H. Kuyesedwa kwa Yesu: 26:57-27:26

**Gawo Lachisanu ndi chitatu: Imfa ndi Chigonjetso cha Mfumu 27:27-28:20**

- I. Kupachikidwa ndi kuikidwa mmanda: 27:27-66

- A. Kunyoza kwa asilikali: 27:27-31
- B. Ulendo wokafa ndi kupachikidwa pa mtanda: 27:32-54
- C. Azimayi okhulupirika, kuikidwa mmanda ndi alonda akumanda: 27:55-66

II. Chiukitso: 28:1-15

III. Kutumidwa: 28:16-20

### MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Mateyu ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga cha buku la Mateyu.

---

---

---

3. Kodi Mateyu amalemba ndani?

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki mu buku la Mateyu.

---

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Mateyu kuchokera pa mtima.

---

---

---

**(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa chaputala chomaliza cha bukhu lino).**

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Buku la Mateyu likhonza kuonedwa mmagawo atatu a zochitika khumi. Chiphunzitso cha pa phiri chimene chili ndi mfundo khumi (ndime 5-6). Ndime zotsatira (8-10) zimakamba za zozidwa khumi. Gawo lotsatira la la ndime (11-18) pamene amakamba zotsatira khumi za anthu omwe amamtsata Yesu. Liwerengeni bukuli pogwiritsa ntchito magawowa.
2. Werengani moyo wa Mateyu. Iyeyu anali wodulitsa misonkho (Mateyu 5:3). Ndipo anakhala wophunzira wa Yesu (Mateyu 9:9). Kumapeto kwake anasankhidwa kukhala mtumwi (Mateyu 10:13) ndipo ndi amene analemba Uthengawu mu dzina lake.
3. Werengani mayesero a Yesu mu Mateyu 4 ndipo gwiritsani ntchito tchati loti likuthandizeni kumvetsesa nkhani ya mayesero:

### Mayesero a Khristu

<b>Mayesero</b>	<b>Mtundu wa Mayesero</b>	<b>“Ngati”</b>	<b>Mayankho a Yesu Mmalemba</b>
Miyala	Njala ya Kuthupi	Ngati muli mwana wa Mulungu	Deuteronomo 8:3
Pamwamba Pa kachisi	La uzimu	Ngati muli mwana wa Mulungu	Masalmo 91:11-12 Deuteronomo 6:16
Mafumu a Dziko lapansi	Lokhuza zinthu	Ngati mundigwadira ine	Deuteronomo 6:13

4. Mu buku la Mateyu chaputala 1 ndi 2 muli mawu amene atchulidwa koma ndi ochokera mu chipangano chakale monga:  
Mateyu 1:23 Yesaya 7:14  
Mateyu 2:2 Yeremiya 23:5; Zekaliya 9:9  
Mateyu 2:6 Milika 5:2  
Mateyu 2:15 Hoseya 11:1; Eksodo 4:22  
Mateyu 2:18 Yeremiya 31:15  
Mateyu 2:23 Yesaya 11:1
5. Lembani makhalidwe a ophunzira a Yesu kuchokera mu Mateyu chaputala cha 10.
6. Werengani Mateyu 20:17-28. Ndipo lembani kusiyana kwa atsogoleri a kudziko ndi utsogoleri wa Yesu.



7. Werengani Mateyu 23 ndipo lembani malamulo khumi oyenera atsogoleri a chikhristu.
8. Werengani mawu awa amene akuchokera mu chipangano chakale amenenso akufana ndi Mateyu 21:1-17; Zakaliya 9:9; II Mafumu 9:13; Eksodo 30:13; Masalmo 118:26; Levitiko 1:14; Yesaya 56:7; Yeremiya 7:11; Masalmo 8:2
9. Werengani mawu ofunikira awa mu buku la Mateyu: Ufumu, Kumwamba, Ufumu wa Kumwamba.

10. Phunzirani mapemphero a Yesu kuchokera mmabuku awa:

-Pa ubatizo:	Luka 3:21
-Malo obisika:	Marko 1:35
-Mu chipululu:	Luka 5:16
-Usiku wonse asanasankhe ophunzira ake:	Luka 6:12
-Asanaitanidwe, "Idzani kwa Ine":	Mateyu 11:25-27
-Akudyetsa anthu 5,000:	Yohane 6:11
-Atadyetsa anthu 5,000:	Mateyu 14:23
-Atapereka pemphero la Ambuye:	Luka 11:1-4
-Ku Kaesareya wa Filipo:	Luka 9:18
-Asanawalitsidwe:	Luka 9:28-29
-Kwa tiwana:	Mateyu 19:13
-Asanaukitse Lazaro kwa akufa:	Yohane 11:41-42
-Mu kachisi:	Yohane 12:27-28
-Pa mgonero:	Mateyu 26:26-27
-Kwa Petro:	Luka 22:32
-Kwa ophunzira ake ndi amene adzamtsatira:	Yohane 17
-Mu Getsemane:	Mateyu 26:36,39,42,44
-Pa mtanda:	Luka 23:24
-Ku Emau:	Luka 24:30

11. Phunzirani zozizwa zimene Yesu adachita:

	<b>Mateyu</b>	<b>Marko</b>	<b>Luka</b>	<b>Yohane</b>
Wakhate	8:2-3	1:40-42	5:12-13	
Kapolo wa Kenturiyo	8:5-13		7:1-10	
Mpongozi wa Petro	8:14-15	1:30-31		4:38-39
Awiri a ku Gadara	8:28-34	5:1-15	8:27-35	
Munthu wopuwala	9:2-7	2:3-12	5:18-25	

Mkazi wa mwazi	9:20-22	5:25-29	8:43-48	
Akhungu awiri	9:27-31			
Munthu wosalankhula	9:32-33			
Dzanja lopuwala	12:10-13	3:1-5	6:6-10	
Munthu wogwida chiwanda	12:22		11:14	
Mkazi wa kukanani	15:21-28	7:24-30		
Wodwala khunyu	17:14-18	9:17-29	9:38-43	
Anthu akhungu	20:29-34	10:46-52	18:35-43	
Wosalankhula		7:31-37		
Munthu waziwanda mkachisi		1:23-26	4:33-35	
Wakhungu ku Betsaida		8:22-26		
Mkazi wopeteka			13:11-13	
Munthu wodwala mbulu			14:1-4	
Akhate khumi			17:11-19	
Khutu la kapolo			22:50-51	
Mwana wa wamkulu				4:46-54
Wodwala ku Betsaida				5:1-9
Wosaona chibadwire				9:1-7
Aletsa namondwe	8:23-27	4:37-41	8:22-25	
Kuyenda panyanja	14:25	6:48-51		
Adyetsa anthu 5,000	14:15-21	6:35-44	9:12-17	6:5-13
Adyetsa anthu 4,000	15:32-38	8:1-9		
Ndalama mu nsomba	17:24-27			
Mkuyu wouma	21:18-22	11:12-26		
Kupha nsomba			5:1-11	
Madzi akhala vinyo				2:1-11
Kupha nsomba			21:1-11	
Mwana wa Yairo	9:18-25	5:22-42	8:41-56	
Mwana wa mkazi wamasiye				7:11-15
Lazaro				11:1-44

12. Mphunzirani mafanizo amene Ambuye Yesu adagwiritsa ntchito pophunzitsa:

	<b>Mateyu</b>	<b>Marko</b>	<b>Luka</b>
Nyali mu mbiya	5:14-15	4:21-22	8:16; 11:33
Nyumba pa thanthwe	7:24-27		6:47-49
Chovala chatsopano	9:16	2:21	5:36
Vinyo watsopano	9:17	2:22	5:37-38
Wofesa ndi nthaka	13:3-8	4:3-8	8:5-8

Mbewu ya mpiru	13:31-32	4:30-32	13:18-19
Nansongole	13:24-30		
Chotupitsa	13:33		13:20-21
Chuma chobisika	13:44		
Fanizo la ngale	13:45-46		
Fanizo la nkhoka	13:47-48		
Nkhoza yosochera	18:12-13		15:4-6
Amangawa awiri	18:23-24		
Antchito a mmunda	20:1-16		
Ana awiri	21:28-31		
Olima munda wampesa	21:33-41	12:1-9	20:9-16
Phwando la ukwati	22:2-14		
Mtengo wamkuyu	24:32-33	13:28-29	21:29-32
Anamwali khumi	25:1-13		
Matalente	25:14-30		19:12-27
Nkhosa ndi mbuzi	25:31-36		
Mbewu		4:26-29	
Wokongola ndi wokongoletsa			7:41-43
Msamaliya wachifundo			10:30-37
Bwenzi la usiku			11:5-8
Mwini chuma wopusa			12:16-21
Kapolo wochezera			12:35-40
Mdindo okhulupirika			12:42-48
Mkuyu wosabala			13:6-9
Malo a ulemu			14:7-14
Phwando lalikulu			14:16-24
Mtengo womtsata Iye			14:28-33
Ndalama yotaika			15:8-10
Mwana wolowelera			15:11-32
Mdindo onyenga			16:1-8
Lazaro ndi wa chuma			16:19-31
Mbuye ndi akapolo ake			17:7-10
Mkazi wamasiye			18:2-5
Mfalisi ndi wamisonkho			18:10-14

## CHAPUTALA CHA 2

### MARKO

#### ZOLINGA:

Pakutha ma mutu uwu muyenera:

- Kutchula wolembe buku la Marko.
- Kuzindikira amene Marko amawalemba.
- Kutchula cholinga cha buku la Marko.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Marko kuchokera pa mtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya utumiki la buku la Marko.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Marko

**KOMWE AMALEMBERA:** Kwa onse okhulupirira, koma makamaka kwa Achiroma amene amafuna kuwaonetsera Yesu ngati kapolo.

**CHOLINGA:** Kuonetsa utumiki wa Yesu, potsindika za ntchito yake ngati kapolo ndi mwana wa munthu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Marko 10:45

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Tikuyenera kutumikira osati kutumikilidwa

**ANTHU OPEZEKA M'BUKULI:** Yesu, akuphunzira khumi

### MAGAWO

I. Nthawi yokonzekera: 1:1-13

- A. Chiyambi cha uthenga: 1:1-3
- B. Utumiki wa Yohane Mbatizi: 1:4-8
- C. Ubatizo wa Yesu: 1:9-11
- D. Mayesero a Yesu: 1:12-13

II. Utumiki wa ku Galileya: 1:14-6:30

- A. Chiyambi cha utumiki wa Yesu: 1:14-15
- B. Kuitanidwa kwa asodzi anayi: 1:16-20
- C. Kuchiritsidwa kwa munthu wodzazidwa ziwanda: 1:21-28
- D. Kuchiritsidwa kwa mpongozi wake wa Petulo: 1:29-31
- E. Kutchuka kwa utumiki: 1:32-34
- F. Nthawi ya chete: 1:35-37
- G. Maulendo anayi aku Galileya: 1:38-39
- H. Kuchiritsa wakhate: 1:40-45
- I. Kuchiritsa munthu wopuwala: 2:1-12
- J. Kuitanidwa kwa Mateyu: 2:13-14
- K. Chisangalalo, chitsutso ndi yankho: 2:15-22
- L. Kusamvetsetsana pa Sabata: 2:23-3:6
- M. Utumiki mbali mwa Nyanja: 3:7-12
- N. Kusankhidwa kwa ophunzira khumi ndi awiri: 3:13-19
- O. Changu cha Yesu: 3:20-21
- P. Tchimo losakhulukidwa: 3:31-35
- Q. Ubale weniweni ndi Yesu: 3:31-35
- R. Mitundu ya mafanizo: 4:1-34
  - 1. Fanizo la wofesa: 4:1-20
  - 2. Fanizo la nyali: 4:21-25
  - 3. Fanizo la mbewu: 4:26-29
  - 4. Fanizo la mbewu yampiru: 4:30-34
- S. Namondwe pa Nyanja: 4:35-41
- T. Machiritso a wogwida ndi wonyasa: 5:1-20
- U. Mwana wa Yairo ndi mzimayi wa vuto la mwazi: 5:21-43
- V. Kukanidwa ku Nazareti: 6:1-6
- W. Ntchito ya ophunzira khumi ndi awiri: 6:7-13
- X. Imfa ya Yohane Mbatizi: 6:14-29
- Y. Mmene adayendera khumi ndi awiriwo: 6:30

### III. Nthawi ya kudzikana: 6:31-9:50

- A. Kudyetsa anthu zikwi zisanu: 6:31-46
- B. Kuyenda pamadzi: 6:47-52
- C. Utumiki ku Genesareti: 6:53-56
- D. Kudzudzulidwa kwa Afalisi: 7:1-23
- E. Mkazi wa ku Suro-Fonika: 7:24-30

- F. Kuchiritsa munthu wosalankhula: 7:31-37
- G. Kudyetsa anthu zikwi zinayi: 8:1-9
- H. Kufuna chizindikiro: 8:10-13
- I. Langizo la chotupitsa: 8:14-21
- J. Kuchiritsa munthu wakhungu: 8:22-26
- K. Funso ndi phunziro la ku Kayesareya wa Filipo: 8:27-9:1
- L. Mawalitsidwe a Yesu: 9:2-10
- M. Vuto la Eliya: 9:11-13
- N. Kuchiritsa mnyamata wa chiwanda: 9:14-29
- O. Chiphunzitso chotsiriza ku Galiyela: 9:30-50

IV. Utumiki wa ku Pereya ndi Yudeya: 10:1-52

- A. Phunziro lokhuza kulekana: 10:1-12
- B. Mdalitso wa tiwana: 10:13-16
- C. Mnyamata mwini chuma: 10:17-22
- D. Malangizo a zotsamwisa za chuma: 10:23-27
- E. Zokambirana zokhuza mphoto: 10:28-31
- F. Anenelatu za imfa Yake: 10:32-34
- G. Pempho lofuna malo apamwamba: 10:35-45
- H. Machiritso a Bartimeyu wakhungu: 10:46-52

V. Zochitika mu Sabata yotsiriza: 11:1-15:47

- A. Kulowa mwachifumu ku Yerusalemu: 11:1-11
- B. Kutemberera mtengo wamkuyu wosabala: 11:12-14
- C. Kuyeretsa kachisi: 11:15-19
- D. Phunziro la chikhulupiriro: 11:20-26
- E. Kulimbana ndi ulamuliro wa Yesu: 11:27-33
- F. Fanizo la osungira munda: 12:1-12
- G. Za kupereka msonkho: 12:13-17
- H. Za kuuka kwa akufa: 12:18-27
- I. Funso la lamulo lalikulu loposa onse: 12:28-34
- J. Funso lokhuza Yesu mwini: 12:35-37
- K. Chenjezo lokhuzana ndi Alembi: 12:38-40
- L. Mphatso ya mkazi wamasiye: 12:41-44
- M. Chikhulupiriro cha mtsogolo: 13:1-37
- N. Chiwembu cha Ansembe akulu: 14:1-2
- O. Phwando la ku Betaniya: 14:3-9

- P. Chiwembu cha Yudasi: 14:10-11
  - Q. Pasaka: 14:22-26
  - R. Mgonero otsiriza: 14:22-26
  - S. Aneneratu zoti Petulo azamkana Yesu: 14:27-31
  - T. Pemphero la mu Getsemani: 14:32-42
  - U. Kuperekedwa ndi kumangidwa: 14:43-52
  - V. Chiweruzo cha Ayuda: 14:53-65
  - W. Petulo akana Yesu: 14:66-72
  - X. Chiweruzo cha Pilato: 15:1-21
  - Y. Kupachikidwa kwa Yesu: 15:22-41
  - Z. Kuikidwa mmanda kwa Yesu: 15:42-47
- VI. Chiukitso cha Yesu: 16:1-8
- A. Kumanda kuja: 16:1-3
  - B. Manda opanda kanthu: 16:4-6
  - C. Kutumidwa kulalikira uthenga wa chiukitso: 16:7-8
- VII. Kuonekera kwa Yesu: 16:9-14
- A. Kwa Maliya wa Magadala: 16:9-11
  - B. Kwa ophunzira awiri: 16:12-13
  - C. Kwa khumi ndi mmodzi: 16:14
- VIII. Kutumidwa kwakukulu: 16:15-18
- IX. Kukwera kwa Yesu kupita kumwamba: 16:19
- X. Kukwaniritsa kutumidwa: 16:20

### **MAYESO ODZIYESA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Marko ndi ndani?

---

---

2. Tchulani cholinga cha buku la Marko.

---

---

---

3. Kodi wolembe buku la Marko amalemba ndani?

---

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya utumiki mu buku la Marko.

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Marko kuchokera pa mtima.

---

---

---

**(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa chaputala chomaliza cha bukhu lino).**



## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Phunzirani mawu ofunikira omwe akupezeka mu buku la Marko: Mwachindunji, osachedwa ndi mwachangu.
2. Phunzirani moyo wa Marko wolemba buku amene limene limadziwikanso ndi dzina lake. Onani: Machitdwe 12:12,25; 13:5,13; 15:37-39; Akolose 4:10; Filemoni 23-24; ndi I Petro 5:13.
3. Yesu anaonekera kwa nthawi yaitali atangoukitsidwa, ndi cholinga chofuna kutsimikiza kuti anaukadi mmanda. Motero anaonekera kwa anthu awa:
  - Maliya wa Magadala: Marko 16:9-10
  - Akazi ena: Mateyu 28:9-10
  - Ophunzira awiri panjira yak u Emau: Marko 16:12-13; Luka 24:13-32
  - Petro: Luka 24:34
  - Ophunzira opandapo Tomasi: Marko 16:14; Luka 24:36; Yohane 29:19
  - Ophunzira ndi Tomasi: Yohane 20:26-31
  - Asanu ndi awiri mbali mwa Nyanja ya Galileya: Yohane 21
  - Ophunzira ku Galileya: Mateyu 28:16-20
  - Yakobo: I Akorinto 15:7
  - Iwo amene anali ndi Iye paphiri: Marko 16:19; Luka 24:44; Machitidwe 1:3
  - Paulo: I Akorinto 15:5-8
4. Yesu ananamizilidwa zambiri kuchokera kwa adani ake. Werengani Marko 2:1-3:6 ndipo malizitsani tchatili:

**2:1-12**

**2:13-17**

**2:18-22**

**2:23-28**

**3:1-6**

---

Mmene zinachitikira

---

Omwe amamutsutsa

---

Chimene amamutsuta

---

Amalankhula kwa ndani

---

Mmene anawayankhira Yesu

---

Zotsatira zake

---

## CHAPUTALA CHA 3

### LUKA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula wolembe buku la Luka.
- Kudziwa amene Luka amawalemba.
- Kutchula cholinga cha buku la Luka.
- Kulemba vesi lotsogolera la Luka kuchokera pa mtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya utumiki ya buku la Luka.

### GAWO LOYAMBA

**WOLEMBA:** Luka

**KULEMBERA:** Okhulupirira onse, koma makamaka kwa a Helene amene amafuna awaonetsere Yesu ngati munthu wangwiro. Komanso amalemba wokhulupirira wina wotchedwa Teofilo.

**CHOLINGA:** Kulongosola za mbiri za utumiki wa Yesu (Luka 1:1-4).

**VESI LOTSOGOLERA:** Luka 19:10

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Ntchito yathu ndi yofanana ndi Yesu. Ndiko kufikira onse otaika ndi uthenga wabwino.

### MAGAWO

#### Gawo loyamba: Kukonzekera 1:1-2:52

I. Mawu oyamba:

- A. Kalata kwa Teofilo: 1:1-4
- B. Masomphenya a Zakaliya: 1:5-25
- C. Masomphenya a Maliya: 1:26-38
- D. Maliya azonda Elizabeti: 1:39-56
- E. Kubadwa kwa Yohane Mbatizi: 1:57-80

II. Kubadwa ndi umwana wa Yesu:

- A. Kubadwa kwa Yesu: 2:1-7
- B. Abusa azonda Yesu: 2:8-20
- C. Mdulidwe ndi kutchulidwa dzina kwa Yesu: 2:21
- D. Kuperekedwa kwa Yesu: 2:22-40
- E. Kupezeka kwa Yesu Mkachisi: 2:41-52

**Gawo Lachiwiri: Chiyambi cha Utumiki wa Yesu 3:1-4:3**

- I. Utumiki wa Yohane Mbatizi: 3:1-20
- II. Ubatizo wa Yesu: 3:21-22
- III. Makolo a Yesu: 3:23-38
- IV. Mayesero a Yesu: 4:1-13

**Gawo Lachitatu: Yesu ku Galileya 4:14-9:62**

- I. Kukanidwa kwa Yesu ku Nazareti: 4:14-30
- II. Munthu wa ziwanda mu Sunagoge ku Kaparnao: 4:31-37
- III. Kuchiritsidwa kwa mpongozi wa Petulo: 4:38-39
- IV. Zozizwa zina ndi kulalikira: 4:40-44
- V. Kupha nsomba modabwitsa ndi kuitanidwa kwa Petulo, Yakobo ndi Yohane: 5:1-11
- VI. Kuyeretsewa kwa wa khate: 5:12-16
- VII. Kukhululukidwa ndi kuchiritsidwa kwa munthu wamanjenje: 5:17-26
- VIII. Kuitanidwa kwa Mateyu: 5:27-28
- IX. Kuchita phwando ndi amisonkho: 5:29-32
- X. Zokhudza kusala kudya: 5:33-39
- XI. Kudula ndi kudya tirigu pa tsiku la Sabata: 6:1-5
- XII. Kuchiritsa munthu wa dzanja lopuwala: 6:6-11
- XIII. Kusankha khumi ndi awiri: 6:12-16
- XIV. Chiphunzitso cha pa phiri: 6:17-49
- XV. Kuchiritsa kapolo wa Kenturiyo: 7:1-10
- XVI. Kuukitsidwa kwa akufa kwa mwana wa mkazi wamasiye: 7:11-17
- XVII. Mafunso okhuza Yohane Mbatizi: 7:18-35
- XVIII. Mafuta ndi chikhululukiro a mkazi Wochimwa: 7:36-50
- XIX. Kulalikira mothandizana ndi azimayi ena: 8:1-3
- XX. Fanizo la mbewu ndi dothi: 8:4-15
- XXI. Fanizo la nyali: 8:16-18
- XXII. Ubale wa kuuzimu: 8:19-21
- XXIII. Kuletsa namondwe: 8:22-25
- XXIV. Kuchiritsa wa ziwanda: 8:26-40
- XXV. Kuchiritsa mkazi wa vuto la mwazi ndi kuukitsa mwana wa mkazi wa Yairo: 8:40-56
- XXVI. Utumiki wa khumi ndi awiriwo: 9:1-6

- XXVII. Imfa ya Yohane Mbatizi: 9:7-9
- XXVIII. Kudyetsa anthu zikwi zisanu: 9:10-17
- XXIX. Chivomerzo cha Petulo: 9:18-21
- XXX. Aneneratu za imfa yake: 9:22
- XXXI. Kuitanidwa kukhala ophunzira: 9:23-27
- XXXII. Mawalitsidwe: 9:28-36
- XXXIII. Mamasulidwe a mnyamata wa ziwanda: 9:37-45
- XXXIV. Phunziro la wamkulu: 9:46-48
- XXXV. Zokhuzana ndi kulolerana: 9:49-50

**Gawo Lachinayi: Yesu pa ulendo wa ku Yerusalemu 10:1-19:48**

- I. Kutsimikizika kupita ku Yerusalemu ndi kukanidwa ndi mudzi wa a Samaliya: 9:51-56
- II. Zokhuza ophunzira: 9:57-62
- III. Utumiki wa ophunzira makumi asanu ndi awiri: 10:1-24
- IV. Fanizo la Msamaliya wachifundo: 10:25-37
- V. Mgonero wa pakati pa Maliya ndi Malita: 10:38-42
- VI. Kuphunzitsa za pemphero: 11:1-13
- VII. Chitetezo pa machenjerero a mphamvu ya Satana: 11:14-26
- VIII. Kufunika kosunga Mau a Mulungu: 11:27-28
- IX. Kufunafuna chizindikiro: 11:29-36
- X. Kuyaluka kwa Afalisi ndi Alembi: 11:37-54
- XI. Machenjezo: 12:1-59
  - A. Okhuza chinyengo: 12:1-12
  - B. Okhuza kusilira: 12:13-2
  - C. Okhuza nkhawa: 12:22-34
  - D. Okhuza zakudikira mbuye: 12:35-48
  - E. Okhuza kumvetsetsa utumiki wa Yesu: 12:49-59
- XII. Kulapa machimo: 13:1-9
- XIII. Kuchiritsa mkazi wa mzimu wonyasa: 13:10-17
- XIV. Mafanizo: 13:18-30
  - A. Mbewu ya mpiru: 13:18-19
  - B. Chotupisa: 13:20-21
  - C. Khomo lopapatiza: 13:22-30
- XV. Uthenga wochokera ndi opita kwa Herodi: 13:31-33
- XVI. Kulilira Yerusalemu: 13:34-35

XVII. Kuchiritsa munthu wodwala mbulu: 14:1-6

XVIII. Mafanizo:

- A. Chikondwerero cha mmbanja: 14:7-14
- B. Phwando lalikulu: 14:15-24
- C. Womanga nyumba: 14:25-30
- D. Mfumu yopita ku nkondo: 14:31-35
- E. Nkhosa yotaika: 15:1-7
- F. Ndalama yotaika: 15:8-10
- G. Mwana wolowerela: 15:11-32
- H. Fanizo la kapitawo wonyenga ndi zokhuza Afalisi: 16:1-18
- I. Mwini chuma ndi Lazaro waumphawi: 16:19-31

XIX. Zolakwitsa: 17:1-4

XX. Kukuza chikhulupiriro: 17:5-10

XXI. Machiritso a wodwala khate: 17:11-19

XXII. Ufumu wa Mulungu wa kutsogolo: 17:20-37

XXIII. Fanizo la mkazi wa masiye ndi woweruza wosalungama: 18:1-8

XXIV. Fanizo la Mfalisi ndi wokhomesa misonkho: 18:9-14

XXV. Kulandira tiwana: 18:15-17

XXVI. Mnyamata mwini chuma: 18:18-30

XXVII. Kulojera za imfa ndi kuuka kwa Yesu: 18:31-34

XXVIII. Kuchiritsa wa khungu ku Yeriko: 18:35-43

XXIX. Kutembenuka kwa Zakeyu: 19:1-10

XXX. Fanizo la ndalama: 19:11-27

### **Gawo Lachisanu: Yesu ku Yerusalemu 19:28-24:53**

I. Zochitika Yesu asanape: 19:28-23:25

A. Kulowa mu Yerusalemu: 19:28-48

B. Kusemphana kukachisi: 20:1-47

- 1. Funso lokhuza ulamuliro: 20:1-8
- 2. Fanizo la olima munda osakhulupirika: 20:9-18
- 3. Funso la kupereka msonkho kwa Kayesala: 20:19-26
- 4. Funso lokhuza kuuka kwa akufa: 20:27-40
- 5. Funso ndi chenjezo: 20:41-47

C. Ziphunzitsa za mkachisi: 21:1-38

- 1. Chopereka cha mkazi wamasiye: 21:1-4
- 2. Zakutsogolo: 21:5-28

3. Awachenjeza za kudikira: 21:29-38

D. Pasaka ndi usiku wotsiriza: 22:1-71

1. Chiwembu chofuna kupha Yesu: 22:1-6
2. Kukonzekera Pasaka: 22:7-13
3. Mgonero wotsiriza: 22:14-23
4. Wamkulu weniweni: 22:24-30
5. Chenjezo kwa Petulo: 22:31-34
6. Chenjezo kwa ophunzora: 22:35-38
7. Pemphero la mmunda wa Getsemane: 22:39-46
8. Kumangidwa kwa Yesu: 22:47-53
9. Petulo akana Yesu: 22:54-62
10. Kuyesedwa kwa Yesu: 22:63-71
  - a. Chipongwe cha asilikali: 22:63-65
  - b. Chiweruzo cha akuluakulu: 22:66-71
  - c. Kumva mlandu pamso pa Herodi: 23:1-12
  - d. Kumva mlandu pamaso pa Pilato: 23:13-25

II. Imfa ya Yesu: 23:26-56

A. Kupachikidwa: 23:26-49

1. Panjira yaku Gologota: 23:26-31
2. Kupachikidwa ndi kunyozedwa kwa Yesu: 23:32-38
3. Kulapa kwa Zigawenga: 23:39-43
4. Imfa ya Yesu: 23:44-49
5. Kuikidwa mmunda kwa Yesu: 23:50-56

III. Kuukitsidwa kwa Yesu: 24:1-12

IV. Utumiki pambuyo chiukitso: 24:13-49

- A. Panjira yak u Emau: 24:13-35
- B. Kuonekera ku Yerusalemu: 24:36-49
- C. Kutuma komaliza: 24:44-49
- D. Kukwera kwa Yesu kupita kumwamba: 24:50-53

## **MAFUNSO ODZIYESA NOKHA**

1. Kodi adalemba buku la Luka ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene Luka analemba buku.

---

---

---

3. Kodi wolemba buku la Luka amalemba ndani?

---

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Luka.

---

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Luka kuchokera pa mtima.

**(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino).**

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

1. Luka yemwe analemba uthengawu, ndi iye amenenso analemba Machitidwe Atumwi. Choncho muzaphunzira Machitidwe Atumwi kutsogolo kwa maphunziriwa.
2. Phunzirani moyo wa Luka, amene ndi olemba bukuli. Nkhani yake ikupezeka mmabuku anayi a mauthenga komanso mu buku la Machitidwe Atumwi.
3. Phunzirani tchati ili la ophunzira a Yesu:

**Dzina**

**Zimene  
amachita**

**Mbali ya utumiki**

Petro

Msodzi

Mtsogoleri wa mpingo

Yakobo mwana wa Zebedayo	Msodzi	Yudeya
Yohane	Msodzi	Yerusalemu, Efeso, anawachotsa ku Patmo
Andreya	Msodzi	m'Asiya
Filipo	Chotsadziwika	Frugiya
Bartumeyu	Chotsadziwika	Armeniya Irani
Tomasi	Chotsadzikika	Pafiya, Peresiya, Indiya
Mateyu	Wokhometsa misonkho	Aitiopiya
Yakobo	Chotsadziwika	Palestine, Aigupto
Yudasi	Chotsadziwika	



## CHAPUTALA CHA 4

### YOHANE

#### ZOLINGA:

Pakutha pa mutu uwu muyenera:

- Kutchula wolembe buku la Yohane.
- Kudziwa amene Yohane amawalemba.
- Kutchula cholinga chomwe Yohane amalemba buku.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Yohane.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki za buku la Yohane.

#### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yohane

**KULEBERA:** Okhulupirira onse amene Yohane anawaonetsera kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu

**CHOLINGA:** kutsimikizira kuti Yesu anali Mesiya, Mwana wa Mulungu ndi wotsogolera anthu ku moyo osatha.

**VESI LOTSOGOLERA:** Yohane 20:31

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Yesu ndiye Khristu, Mwana wa Mulungu wa moyo, mwini chipulumutso and njira ya moyo wosatha.

**ANTHU OPEZEKA:** Yesu, Yohane Mbatizi, ophunzira khumi ndi awiri.

### MAGAWO

#### Gawo Loyamba: Mawu Oyamba 1:1-51

I. Kuonetsera Yesu amene ndi Mkhristu: 1:1-18

A. Yesu amene ndi Mawu analiko: 1:1-3

1. Kuchokera pa chiyambi: 1:1
2. Ndi Mulungu: 1:1
3. Anali Mulungu: 1:1
4. Mawu olenga: 1:2-3

B. Yesu, Moyo ndi Kuunika: 1:4-13

1. Moyo ndi Kuunika kwa anthu: 1:4
2. Kuwala kumene kunawala mumdima: 1:5
3. Kuwala kumene Yohane Mbatizi anachitira umboni: 1:6-8
4. Kuwala kwenikweni kwa munthu: 1:9
5. Sanalandilidwe ndi ambiri: 1:10-11
6. Analandilidwa ndi ena: 1:12-13

C. Yesu mu thupi: 1:14-18

1. Wobadwa mwa Mulungu: 1:14
2. Mawu anasandulika thupi nakhala pakati pathu: 1:14
3. Yohane Mbatizi anachita umboni za Mau osandulika thupi: 1:15

D. Yesu, wodzala ndi chisomo cha Mulungu: 1:16-18

II. Umboni wa Yohane Mbatizi: 1:19-34

A. Yesu amene ndi Mesiya: 1:19-28

1. Mafunso: 1:19-22
2. Mayankho: 1:23
3. Wofunsa: 1:24
4. Kufunsa mochuluka: 1:25
5. Yankho: 1:26-27
6. Malo ochitikira macheza: 1:28

B. Yesu mwana wa nkhosa ndi Mwana: 1:29-36

1. Ubatizo: 1:29-34
2. Chivomerezo: 1:35-36

III. Ophunzira oyamba: 1:35-51

- A. Andreyu: 1:34-40
- B. Simoni Petro: 1:40-42
- C. Filipo: 1:43-44
- D. Natanateli: 1:45-51

**Gawo Lachiwiri: Utumiki 2:1-12:50**

I. Kusandutsa madzi kukhala vinyo: 2:1-10

- A. Malo: 2:1
- B. Anthu oyitanidwa: 2:2
- C. Vuto: 2:3-5
- D. Yankho la chozizwa: 2:6-11

II. Ulamuliro pa kachisi: 2:12-25

- A. Kupita ku Yerusalemu: 2:12-13
- B. Kuyereza kachisi: 2:14-22
  - 1. Kuyereza: 2:14-16
  - 2. Kukumbukira kwa ophunzira: 2:17
  - 3. Uneneri: 2:18-21
  - 4. Kukumbukira kwa ophunzira: 2:22
- C. Zotsatira za kuyereza: 2:23-25

III. Kucheza ndi Nikodemu: 3:1-21

- A. Malo ake: 3:1-2
- B. Chilengezo: 3:2
- C. Yankho: 3:3
- D. Funso loyamba: 3:4
- E. Yankho: 3:5-8
- F. Funso lachiwiri: 3:9
- G. Yankho: 3:10-21

IV. Chitsimikizo cha Yesu ndi Yohane Mbatizi: 3:22-36

- A. Malo: 3:22-24
- B. Funso: 3:25-26
- C. Yankho: 3:27-36

V. Utumik pakati pa Asamaliya: 4:1-42

- A. Mmene malo analili ku Samaliya: 4:1-6
- B. Umboni kwa Mkazi: 4:7-26
- C. Kudadwa kwa ophunzira: 4:27
- D. Umboni wa Mkazi ku Samaliya: 4:28-30
- E. Masomphenya a akuphunzira: 4:31-38
- F. Zotsatira za utumiki wa ku Samaliya: 4:39-42

VI. Chozizwa ku Galileya: 4:43-54

- A. Kupita ku Galileya: 4:43-45
- B. Kuchiritsa mwana wa Wamkulu: 4:46-54

VII. Kuchiritsa moyo pa tsiku la Sabata: 5:1-47

- A. Machiritso pa tsiku la Sabata: 5:1-9
- B. Ayuda ndi munthu wochiritsidwa: 5:10-13
- C. Yesu ndi munthu wochiritsidwa: 5:14
- D. Ayuda ndi munthu wochiritsidwa: 5:15-18
- E. Chiphunzitso cha kuchiritsidwa: 5:19-47
  - 1. Yesu alengeza za Umulungu wake: 5:19-29
    - a. Muntchito: 5:19-21
    - b. Muchiukitso: 5:21
    - c. Muchiweruzo: 5:22-29
    - d. Mu ulemu: 5:23
  - 2. Umboni ku Umulungu wake wa Yesu: 5:30-40
    - a. Umboni wa Iye mwini: 5:30-32
    - b. Yohane Mbatizi: 5:33-35
    - c. Ntchito za Yesu: 5:36
    - d. Atate: 5:37-38
    - e. Malemba: 5:39
  - 3. Kudzudzula kusakhulupirira: 5:40-47

VIII. Yesu Mkate wa Moyo: 6:1-15

- A. Malo ake: 6:1-4
- B. Vuto: 6:5-7
- C. Kudyetsa anthu zikwi zisanu: 6:8-13
- D. Zotsatira zohkumudwitsa: 6:14-15

IX. Mantha mchikhulupiriro pakatikati pa mafunde: 6:25-34

X. Zotsatira za kudyetsa anthu zikwi zisanu: 6:22-71

- A. kusonkhana kwa anthu zikwi zisanu: 6:22-24
- B. Macheza pa za Mkate wa Moyo: 6:25-71
  - 1. Mkate wa Mose kufanizidwa ndi wa Yesu: 6:25-34
  - 2. Mkate umene umapatsa Moyo Wosatha: 6:35-40
  - 3. Mkate wamoyo wotsika kumwamba: 6:41-51
  - 4. Mkate wa imfa ya Yesu: 6:52-59
- C. Zotsatira za macheza: 6:60-71
  - 1. Ambiri anabwerera mmbuyo: 6:60-66
  - 2. Khumi ndi awiriwo anatsala: 6:67-71

XI. Yesu pa phwando ku Yerusalemu: 7:1-53

- A. Ulendo wa ku Yerusalemu: 7:1-10
- B. Yesu ku Yerusalemu. Mafunso ambiri okhuza Iye: 7:11-13
- C. Kukaikitsa kwa otsutsana ndi Yesu: 7:14-24
- D. Yesu ngati wokaikitsa: 7:25-36
- E. Kulalikira za Yesu: 7:37-39
- F. Gulu logawanika: 7:40-44
- G. Akuluakulu ogawanika: 7:45-53

XII. Chiphunzitso mkachisi: 8:1-59

- A. Mkazi wachigololo: 8:1-8:11
- B. Yesu kuunika kwa dziko: 8:12-20
- C. Chithunzithunzi cha mtanda ndi zotsatira za khamu: 8:21-30
- D. Ayuda ndi kukhala ophunzira: 8:31-59
  - 1. Ufulu pa kudziwa choonadi: 8:31-36
  - 2. Ana a Abrahamu: 8:37-40
  - 3. Ana a Satana: 8:41-47
  - 4. Zokhuzana ndi kudzadzidwa ndi ziwanda: 8:48-52

E. Zotsatira za chiphunzitso pakati pa Yesu ndi Abrahamu: 8:52-59

XIII. Yesu achiritsa munthu wakhungu: 9:1-41

- A. Munthu wosapenya chibadwire achiritsidwa: 9:1-7
- B. Zimene anachita abale a munthu wosapenya: 9:8-12
- C. Zimene anachita Afalisi: 9:13-34
  - 1. Kukambirana ndi munthu wosapenya: 9:13-17
  - 2. Kukambirana ndi makolo ake: 9:18-23
  - 3. Kukambirana kwachiwiri ndi munthu wosapenya: 9:24-34
- D. Kumapeto kwa zonse Yesu, wosapenya ndi Afalisi: 9:35-41

XIV. Macheza A ubusa: 10:1-42

- A. Mbusa wenweni wa nkhosa: 10:1-6
- B. Khomo lolowera nkhosa: 10:7-10
- C. Mbusa wabwino wa nkhosa: 10:11-18

XV. Kuutsa udani ndi Yesu: 10:19-42

- A. Kusemphana pa Kukhala ndi ziwanda: 10:19-21
- B. Kufuna zolankhula zopanda pake: 10:22-24
- C. Yankho la Yesu: 10:25-30
- D. Kuthawa chilango cha kuchita mwano: 10:31-39
- E. Kupeza malo kupitilira Yorodano: 10:40-42

XVI. Imfa isandulika moyo: 11:1-44

- A. Malo ake: 11:1-6
- B. Dongosolo: 11:7-16
- C. Macheza pa zochitika zofunika za kutsogolo: 11:17-27
- D. Chikaikitso cha imfa: 11:28-39
- E. Kuukitsidwa kwa Lazaro: 11:40-44
- F. Zotsatira za chozizwacho: 11:45-12:11
  - 1. Zimene ena osakhulupirira adachita: 11:45
  - 2. Zimene akuluakulu adachita: 11:46-53
  - 3. Zimene zidachitika pa chitetezo cha Yesu: 11:54-57
  - 4. Kudzodzedwa chifukwa cha imfa yake: 12:1-8
  - 5. Machitachita osiyanasiyana: 12:9-11

XVII. Yesu Mfumu: 12:12-50

- A. Kutchuka kwa Mfumu kuchuluka: 12:12-19
- B. A Helene azonda Mfumu: 12:20-22
- C. Imfa ya Mfumu: 12:23-50
  - 1. Kulosera imfa ya Mfumu: 12:23-27
  - 2. Chitsimikizo cha Atate kwa Mfumu: 12:28-30
  - 3. Umboni wa Mfumu: 12:30-36
  - 4. Kusakhulupirira Mfumu: 12:37-43
  - 5. Chikhulupiriro mwa Mfumu: 12:44-50

**Gawo Lachitatu: Utumiki wa chinsinsi 13:1-17:26**

I. Mgonero wotsiriza: 13:1-38

- A. Kutengapo phunziro: Kusambitsa mapazi: 13:1-11
  - 1. Zomwe zinachitika: 13:1-3
  - 2. Chochitikacho: 13:4-5
  - 3. Tanthauzo la chochitikacho: 13:6-17
- B. Kubwera poyera kwa Yudasi: 13:18-30
- C. Kulosera za kuchoka kwa Yesu: 13:31-35
- D. Kulosera kuti Petulo azamkana Yesu: 13:36-38

II. Uthenga wa chikonzekero ndi chithonhozo: 14:1-27

- A. Chikonzekero: 14:1-4
- B. Njira: 14:5-15
- C. Mthonhozi: 14:16-21,26
- D. Kudzionetsera kwa ake ake: 14:22-31

III. Umodzi wa pamwamba ndi Yesu: 15:1-27

- A. Umodzi ndi mpesa: 15:1-8
- B. Umodzi mchikondi: 15:9-17
- C. Kusemphana ndi dziko: 15:18-25
- D. Umodzi ndi mthonhozi: 15:26-27

IV. Chithunzithunzi cha tsogolo: 16:1-33

- A. Aneneratu za chizunzo chilimkudza: 16:1-6
- B. Mtonthozi yemwe akubwera: 16:7-16
- C. Uneneri wa kubwerera kwa Yesu kupita kumwamba: 16:16
- D. Ophunzira okhala kakasi: 16:17-19
- E. Kusanduliza chisoni kukhala chimwemwe: 16:20-30
- F. Chikhulupiriro cha mtsogolo: 16:31-33

V. Pemphero la Yesu: 17:1-26

- A. Kwa Iye Yekha: 17:1-8
- B. Kwa akuphunzira ake: 17:9-19
- C. Kwa omtsatira akutsogolo: 17:20-26

**Gawo Lachinayi: Masiku otsiriza 18:1-19:42**

I. Kugwidwa: 18:1-14

- A. Mkumano wa ku Munda: 18:1
- B. Kumpereka kwa Yudasi: 18:2-3
- C. Kusaletseka kwa Yesu: 18:4-9
- D. Chiwawa cha Yesu: 18:10-11
- E. Ulendo wopita kwa Anasi: 18:12-14

II. Petulo amkana Yesu koyamba: 18:15-18

III. Kumva mlandu pamaso pa Anasi: 18:19-24

- A. Umboni wodzitetzeza: 18:19-21
- B. Chiweruzo cha Anasi: 18:22-24

IV. Petulo amkana Yesu kachiwiri: 18:25-26

V. Petulo amkana Yesu kachitatu: 18:26-27

VI. Kumva mlandu pamaso pa Pilato: 18:28-19:16

- A. Kumva mlandu pamaso pa gulu lonse: 18:28-32
- B. Kumva Mlandu mseri: 18:33-38
- C. Barabasi: 18:38-40



- D. Kuchitidwa chipongwe ndi Aroma: 19:1-3
- E. Afuna zoti aphedwe: 19:4-8
- F. Chikhululukiro chikanidwa: 19:9-16

VII. Imfa ya Yesu: 19:17-30

- A. Kupachikidwa: 19:17-18
- B. Dzina lokamba za imfa yake: 19:19-22
- C. Kuonetsa kusakhuzidwa: 19:23-24
- D. Osiyidwa: 19:25-27
- E. Imfa ya Yesu: 19:28-30

VIII. Kuikidwa mmanda: 19:31-42

- A. Kuzonda mtembo: 19:31-37
- B. Kuikidwa mmanda: 19:38-42

**Gawo Lachisanu: Kuukitsidwa ndi Kuonekera 20:1-21:23**

I. Chiukitso cha Yesu: 20:1-31

- A. Mmanda mopanda kanthu: 20:1-10
- B. Umboni wa aminthenga awiri: 20:11-13
- C. Umboni wa Ambuye woukayo: 20:14-29
  - 1. Kwa Maliya wa Magadala: 20:14-18
  - 2. Kwa ophunzira koma popanda Tomasi: 20:19-25
  - 3. Kwa ophunzira kuphatikizapo Tomasi: 20:26-29
- D. Mawu otsiriza: 20:30-31

II. Mkumano wa mmbali mwa nyanja: 21:1-23

- A. Usiku wolephera kupha nsomba: 21:1-3
- B. Yankho la katakwe wa asodzi Yesu: 21:4-6
- C. Kufisula ndi Yesu: 21:7-14
- D. Kutsimikizika kwa Petulo kwachiwiri: 21:15-19
- E. Chiyambi cha Munthu wotchuka: Kuti Wophunzira Ngati Yohane sadzafa: 21:20-23

**Mawu Omaliza 21:24-25**

I. Yohane ndi wophunzira wochitira umboni ndi wolembe: 21:24

II. Pali zinthu zina zambiri Yesu adachita zimene Yohane sadalembe: 21:25

### **MAFUNSO ODZIYESA NOKHA**

1. Kodi ndi ndani amene analemba buku la Yohane?

---

2. Tchulani cholinga chomwe wolembe analemba bukuli.

---

---

---

3. Kodi bukuli analemba ndani?

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Yohane.

---

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Yohane kuchokera pantima.

---

---

---

**(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino.)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Yesu adalankhula mawu ambiri okhuza Iye mwini mu buku la Yohane. Mawu amenewa amayamba ndi mawu okutu “Ine ndine” ... Werengani zitsanzo zotsatirazi:

-Ine ndiye amene (Mesiya):	4:26; 8:24,28; 13:19; 18:5,6,8
-Ine ndine mkate wamoyo:	6:35,41,48,51
-Ine ndine kuunikakwa dziko lapansi:	8:12
-Ine ndine khomo:	10:7,9
-Ine ndine mbusa wabwino:	10:11,14
-Ine ndine kuuka ndi moyo:	11:25
-Ine ndine njira, choonadi ndi moyo:	14:6
-Ine ndine mpesa:	15:1,5
-Kulibe Abrahamu, NDILI:	8:58

2. Werengani ubale wa Yesu ndi Mulungu:

-Mkugwira ntchito: 5:19	-Mu ulemu: 5:23
-Mu chidziwitso: 5:20	-Mu kubadwitsa: 5:24-25
-Mu chiukitso: 5:28-29	-Mu kukhalapo: 5:26

3. Yohane akutiuzza michezo yokwana isanu ndi itatu imene Yesu anali nayo ndi anthu komanso magulu osiyanasiyana:

-Petro ndi Nataniele:	1:35-51
-Nikodemo:	3:1-21
-Mkazi wa ku Samariya:	4:6-26
-Munthu wosaona chibadwire:	10:35-51
-Malita ndi Mariya:	11:1-57
-Atumwi:	13:1-16:33
-Mariya wa ku Magadala:	20:1-18
-Petro:	21:15-23

4. Mu buku la Yohane muli maumboni asanu ndi awiri a anthu amene analengeza kuti Yesu anali Mesiya:

-Yohane Mbatizi: 1:34	-Tomasi: 20:28
-Nataniele: 1:49	-Yohane: 20:31
-Petro: 6:69	-Yesu Mwini: 10:36
-Malita: 11:27	

5. Phunzirani moyo wa Yohane Mbatizi:

-Ntchito yake:	Yohane 1:6-18
----------------	---------------

-Zovala ndi zakudya zake:	Mateyu 3:4
-Uthenga wake:	Mateyu 3:2-10; Luka 3:3-6,13-14; Yohane 1:29
-Kuloseredwa ndi:	Yesaya (40:3-5) ndi Malaki (3:1)
-Umboni wake:	Yohane 1:20,23,27; 3:29-30
-Kuloserera kwake:	Yohane 3:34-35; Luka 3:16
-Chitsimikizo kuti Yesu anali Mesiya:	Mateyu 11:2-6
-Ulemu wa Yesu kwa Yohane:	Mateyu 11:7-11

6. Yohane ndi wophunzira amene analemba uthengawu, analembanso I, II ndi III Yohane ndi buku la Chibvumbulutso. Muphunzira zimenezi kutsogoloku mphunziroli.
  
7. Phunzirani mayina a Mzimu Woyera amene agwiritsidwa ntchito ndi Yohane:
  - Wokhala naye: 14:16-17
  - Mphunzitsi: 14:25-26
  - Mboni: 15:26
  - Wotsutsa machimo: 16:7-11
  - Wotsogolera: 16:13-15
  
8. Yohane akumuonetsa Yesu ngati Mwana wa Mulungu (Umulungu wake) komanso ngati Mwana wa Munthu (Umunthu wake). Werengani ma vesi awa:
 

Mwana wa Mulungu: 1:34,49; 3:18; 5:25; 10:36; 11:4,27; 19:7, 20:31

Mwana wa Munthu: 1:51; 3:13-14; 5:27; 6:27,53,62; 8:28; 9:35; 12:23-24
  
9. Pakuonjedzera dzina la Yesu ngati “Mwana wa Mulungu” pofuna kutsindikira Umulungu wake, Yohane anagwiritsa ntchito mawu ena pofuna kutsimikiza Umulungu wake. Umulungu wa Yesu umatchulidwa kamodzi mu chaputala chilichonse cha buku la Yohane: 1:49; 2:11; 3:16; 4:26; 5:25; 6:33; 7:29; 8:58; 9:37; 10:30; 11:27; 12:32; 13:13; 14:11; 15:1; 16:28; 17:1; 18:11; 19:7; 20:28; 21:14
  
10. Phunzirani moyo wa Yohane amene analemba bukuli:
  - Banja lake: Yohane 21:2, 19:25; Mateyu 27:56; Marko 15:40
  - Ntchito imene amagwira: Marko 1:19-20
  - Utsogoleri wake mu mpingo woyamba: Machitidwe 4:1-22; 8:14-15; Agalatiya 2:9
  - Ukapolo wake: Chibvumbulutso 1:1,4,9
  
11. Onani mitsutso yochuluka imene inamuukira Yesu. Malizitsani tchatili:

Mavesi ake Gwero la mtsutso	Mtundu wa mtsutso	Chifukwa chomtsutsira
5:16		
18		
43		
6:41		
52		
61,66		
70		
7:1		
5		
11		
12		
20		
27,30		
32		
41,44		
45		
47		
8:6		
13		
48,53,59		
9:16		
22		
24		
10:19		
24,31		
39		
11:46		
53		
56-57		
12:4		
10		
19		

## **MAWU OYAMBA A BUKU LA MBIRI**

Buku la Machitidwe ndi buku lokhalo la mbiri mu Chipangano Chatsopano. Limakamba za zinthu zinthu zimene zinachitika pamene Ambuye Yesu atangokwera kupita kumwamba ndi za pa tsiku la Pentekosite, kuonjezera apo limakambaso za kubwadwa ndi mbiri ya mpingo woyamba.

## CHAPUTALA CHA 5

### MACHITIDWE

#### ZOLINGA:

Pakutha pa mutu umenewu muyenera:

- Kutchula wolembe buku la Machitidwe.
- Kuzindikira amene amawalemba.
- Kutchula cholinga cha buku la Machitidwe.
- Kulemba vesi lotsogoloera la buku la Machitidwe.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Machitidwe.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Luka

**KULEMBERA:** Okhulupirira onse ngakhale akulemba kwa munthu wotchedwa Tiofelo.

**CHOLINGA:** Bukuli limakamba za zimene Yesu adapitiriza kuchita ndi kuphunzitsa atangopita kumwamba mu thupi lake la ulemerero, mpingo (Machitidwe 1:1-2).

**VESI LOTSOGOLERA:** Machitidwe 1:8

**MOYO NDO MFUNDO YA UTUMIKI:** Umboni weniweni wa Mzimu Woyera ndiwo mphamvu: Mphamvu yokhala mboni yofalitsa Uthenga kudziko lonse lapansi.

**ANTHU OPEZEKA:** Yohane, Petulo, Paulo, Sila, Banaba, Yohane Marko, Filipo, Stefano, Hananiya ndi Safira, Dorika, Koneliyo, Felike, Agripa.

### MAGAWO

(Dziwani: Gawo ili limatsatira lamulo la Ambuye lopezeka pa Machitidwe 1:8 kuti Uthenga ulalikidwe kuchokera ku Yerusalem, Yudeya, Samaliya ndi malekezere onse a dziko lapansi).

#### Mawu oyamba

Machitidwe 1:1-11

I. Mawu oyamba: 1:1-2

A. Kwa: Teofelo: 1:1

B. Okhuzana: Zimene Yesu adapitiliza kuchita ndi kuphunzitsa atangopita kumwamba mu thupi lake la ulemerero, Mpingo: 1:1-2

II. Utumiki wa Yesu atatha kuukitsidwa: 1:3

A. Masiku ake: Makumi anayi: 1:3

B. Cholinga chake: Zitsikimizo zosakaikitsa: 1:3

C. Uthenga wake: Ufumu wa Mulungu: 1:3

III. Mkumano wotsiiriza wa Yesu ndi akuphunzira ake: 1:4-8

A. Lamulo la ophunzira: 1:4-5

B. Funso la ophunzira: 1:6

C. Chenjezo kwa ophunzira: 1:7

D. Kutuma ophunzira: 1:8

IV. Kukwera kwa Yesu kupita kumwamba: 1:9-11

A. Kulongosola za kukwerako: 1:9

B. Kulengeza za kubwera kwake kwachiwiri: 1:10-11

**Gawo Loyamba:  
Kupanga mboni ku Yerusalemu  
Machitidwe 1:12-7**

I. Kukonzekeretsa mboni: 1:12-2:4

A. Ophunzira aYesu kudikirira ku Yerusalemu: 1:12-26

1. Kusonkhana kwa ophunzira: 1:12-15

a. Malo awo okumaniranapo: 1:12-13

b. Chiwerengero chawo ndi mayina awo: 1:13-15

c. Cholinga chawo: 1:14



2. Chilimbikitso chopita kwa ophunzira: 1:15-22
  - a. Wolankhula: Petulo: 1:15
  - b. Uthenga 1:16-22
    - (1) Chiyambi: 1:16-20
    - (2) Malangizo: 1:21-22
3. Yankho la akuphunzira: 1:23-26
  - a. Maina oti asankhidwe: 1:23
  - b. Pemphero: 1:24-25
  - c. Maere: 1:26
- B. Ubatizo mwa Mzimu Woyera: 2:1-4
  1. Mmene zinakhaira: 2:1
  2. Anthu: 2:1
  3. Malo ake: 2:1
  4. Chochitikacho: 2:2-4
    - a. Mphepo: 2:2
    - b. Malilime a moto: 2:3
    - c. SKulankhula: 2:4

**Gawo Lachiwiri: Ntchito yochitira umbini ku Yerusalemu  
Machitdwe 2:5-7**

I. Mboni zoyamba: 2:4-40

- A. Mmene umboni unaperekedwera: 2:4-6
- B. Zotsatira za umboni: 2:7-13
- C. Ulaliki wa Petulo: 2:14-36
  1. Uneneri wokhuzana ndi nthawi: 2:17
  2. Uneneri wokhuzana ndi mzimu: 2: 17-18
  3. Uneneri wokhuzana ndi chochitikacho: 2:19-20
  4. Uneneri wokhuzana ndi chipulumutso: 2:21
  5. Ntchito ya Yesu: 2:22-36
    - a. Yesu adatsimikizidwa ndi Mulungu: 2:22
    - b. Yesu adapachikidwa: 2:23
    - c. Yesu adauka kwa akufa: 2:24-32
    - d. Yesu adakwezedwa pa dzanja lamanja la Mulungu: 2:33-35
    - e. Yesu ndi Mbuye ndi Khristu: 2:36
- D. Zotsatira atamva uthenga: 2:37-40
  1. Kutsutsika: 2:37

2. Kufunsa: 2:37
3. Langizo: 2:38
4. Malonjezo: 2:38-39
5. Chilimbikitso: 2:40

## II. Mpingo woyamba: 2:41-47

- A. Chiwerengero cha anthu mu mpingo woyamba: 2:41
  1. Chizindikiro chawo: Iwo amene adalandira Mawu.
  2. Chiwerengero chinali: Zikwi zitatu 3,000
- B. Makhaliidwe a Uzimu a mpingo woyamba: 2:42
  1. Chiphunzitsa cha atumwi.
  2. Chiyanjano cha oyera mtima.
  3. Mgonero.
  4. Pemphero.
- C. Chikhalidwe cha mpingo woyamba: 2:44-46
  1. Machitidwe awo a moyo watsiku ndi tsiku: 2:44-45
  2. Kulambira ndi kuchitira umboni tsiku ndi tsiku: 2:46
  3. Kuchita chiyanjano mmanyumba: 2:46
  4. Umodzi: 2:46
- D. Umboni wa mpingo watsopano: 2:46-47
  1. Chikhalidwe cha umboni: 2:46-47
  2. Zotsatira za umboni: 2:47

## III. Chozizwa choyamba: 3:1-26

- A. Mmene chozizwa chinalili: 3:1-11
  1. Malo ake: 3:1
  2. Munthu ndi chosowa chake: 3:2-3
  3. Uthenga: 3:4-6
  4. Chozizwa: 3:7-8
  5. Zimene khamu linachita: 3:9-11
- B. Kulongosola chozizwa: 3:12-18
  1. Munthuyo sanachiritsidwe ndi mphamvu ya atumwi: 3:12
  2. Munthuyo anachiritsidwa ndi Mulungu kuti apereke ulemmerero kwa Yesu: 3:13-15
  3. Munthuyo anachiritsidwa mwa chikhulupiriro mdzina la Yesu: 3:16
  4. Munthuyo anachiritsidwa kuti akaonetse kukwaniritsidwa kwa uneneri: 3:17-18

C. Uthenga wa Petulo: 3:19-26

1. Lonjezo limene Petulo adalinena: 3:19-21
  - a. Chimene Mulungu adatsimikizira Israyeli kuchita: 3:19
  - b. Chimene Mulungu adalonjeza kuchita: 3:19-21
2. Uneneri wa aneneri: 3:22-26
  - a. Uneneri wa Mose ndi aneneri: 3:22-24
  - b. Lonjezo la pangano: 3:25
  - c. Dongosolo la Mesiya: 3:26

IV. Chitsutso choyamba: 4:1-31

A. Kumangidwa: 4:1-4

1. Choyambitsa chitsutso: 4:1
2. Cholinga cha chitsutso: 4:2
3. Mtundu wa chitsutso: 4:3

B. Kuyesedwa: 4:5-14

1. Kubwalo la milandu: 4:5-6
2. Mafunso akubwalo la minlandu: 4:7
3. Mawu a Petulo: 4:8-12
  - a. Maziko a yankho lake: 4:8
  - b. Yankho lake: 4:9-10
  - c. Umboni wake wa Yesu: 4:10-12
  - d. Chilengezo chake cha chipulumutso: 4:12
4. Umboni wa oweruza milandu: 4:13-14
  - a. Chikhalidwe cha umboni: 4:13
  - b. Umboni wa munthu amene anachiritsidwa: 4:14
5. Chisankho: 4:15-22
  - a. Kufuna uphungu: 4:15-17
  - b. Chisankho: 4:17-18
  - c. Yankho la Petulo ndi Yohane: 4:19-20
  - d. Kumasulidwa: 4:21-22
6. Zimene adachita: 4:21-31
  - a. Pemphero la mpingo: 4:23-30
  - b. Ntchito ya mpingo: 4:31

V. Mwambo oyamba wa tchimo: 4:32-5:16

A. Dongosolo la mpingo: 4:32-37

1. Chiyanjano chake: 4:32
2. Umboni wake: 4:33
3. Chuma chake: 4:32-37

B. Tchimo loyamba ndilo loononga chiyanjano: 5:1-10

1. Tchimo: 5:1-2
2. Kuonekera poyera kwa tchimo: 5:3-4
3. Mwambo wake wa tchimo: 5:5-10

C. Zotsatira za mwambo: Umboni wobala chipatso wa chiyanjano: 5:11-16

1. Malingaliro a mantha a mamembala: 5:11
2. Umodzi: 5:12
3. Zozizwa: 5:12, 15-16
4. Zomwe anthu adachita: 5:12-14

VI. Chizunzo choyamba: 5:17-43

A. Maziko a chitsutso: 5:17

B. Zotsatira za chitsutso: 5:18

C. Chiombolo cha Mulungu: 5:19-26

1. Ntchito Zake: 5:19
2. Lamulo Lake: 5:20
3. Zomwe adachita ndi lamulo Lake: 5:21
4. Kuzindikira ntchito zake: 5:21-23
5. Zotsatira za ntchito Zake: 5:24-26

D. Kuyesedwa: 5:27-40

1. Lamulo la akuluakulu: 5:27-28
2. Chozitchinjiriza cha Petulo: 5:29-32
3. Kusanthula kwa akuluakulu: 5:33-39
4. Chisankho chosalungama cha akuluakulu: 5:40

E. Zotsatira za chizunzocho: 5:41-42

1. Chikondwerero: 5:41
2. Umodzi: Kukumana tsiku ndi tsiku limodzi: 5:42
3. Kuchitira umboni: Kuphunzitsa ndi Kulalikira: 5:42

VII. Atumiki oyamba: 6:1-7

- A. Kufunikira kwa atumikiwo: 6:1
- B. Atumikiwo anasankhidwa: 6:2-4
  - 1. Maziko a kusankhidwako: 6:2
  - 2. Cholinga cha kus: 6:2 ankhidwako
  - 3. Chisankhocho: 6:3
  - 4. Kufunikira kwa kusankhidwako: 6:4
- C. Atumiki akhazikitsidwa: 6:5-6
  - 1. Njira zomwe zidatsatidwa: 6:5-6
  - 2. Amuna anasankhidwa: 6:5
  - 3. Kuzozedwa kwao: 6:6
- D. Zotsatira za atumikwo: 6:7
  - 1. Mawu anachulukitsidwa: 6:7
  - 2. Ophunzira anachuluka: 6:7
  - 3. Kumvera ku chikhulupiriro: 6:7

VIII. Wophedwa woyamba kamba ka chikhulupiriro: 6:8-8:1

- A. Mmene analili Stefano: 6:3-15
  - 1. Mmodzi wa asanu ndi awiri: 6:3,5
  - 2. Wozazidwa ndi Mzimu Woyera: 6:5
  - 3. Munthu wa mbiri yabwino: 6:3
  - 4. Munthu wa chikhulupirio: 6:5
  - 5. Munthu wa nzeru: 6:3, 10
  - 6. Munthu wa mphmvu: 6:8
  - 7. Mboni yadalilika: 6:9-10
- B. Chizunzo cha Stefano: 6:11-15
- C. Uthenga wa Stefano: 7:1-53
  - 1. Abrahamu: 7:1-8
  - 2. Makolo a Mchipangano chakale: 7:9-16
  - 3. Mose: 7:17-43
    - a. Ku Aigupto: 7:17-28
    - b. Muchipululu: 7:29-43
  - 4. Chihema: 7:44-50
    - a. Cha Mose: 7:44
    - b. Cha Yoswa: 7:45
    - c. Cha Davide: 7:45-46
    - d. Cha Solomoni: 7:47-50
    - e. Cha Mulungu: 7:48-50
  - 5. Aneneri: 7:51-53

- D. Umboni wa Stefano: 7:54-8:1
  - 1. Malingaliro a akuluakulu: 7:54
  - 2. Chilengezo cha Stefano: 7:55-56
  - 3. Zomwe akuluakulu anachita: 7:57-59
  - 4. Imfa ya Stefano: 7:59-8:1

**Gawo Lachitatu: Umboni wa ku Yudeya ndi ku Samariya  
Machitidwe 8-12**

I. Kusintha: Zotsatira za imfa ya Stephano: 8:1-4

- A. Chizunzo: 8:1,3
- B. Kuikidwa mmanda kwa Stefano: 8:2
- C. Umboni wopitirira wa mpingo: 8:4

II. Umboni wa Filipo: 8:5-40

A. Utumiki wa ku Samariya: 8:5-25

- 1. Umboni wa Filipo: 8:5-13
  - a. Ntchito ya Filipo: 8:5-7, 12
  - b. Zimene a Samaliya adachita: 8:6-12
  - c. Simoni wa nyanga: 8:9-13

2. Ntchito ya Petulo ndi Yohane: 8:14-17

- a. Kubwera kwa Petulo ndi Yohane: 8:14
- b. Kubwera kea Mzimu Woyera: 8:15-17
- c. Zimene Simoni adachita: 8:18-19
- d. Chenjezo la Simoni: 8:20-24

B. Utumiki wa ku Aitiyopiya: 8:26-40

- 1. Kukonzekera: 8:26-28
- 2. Umboni: 8:29-35
- 3. Zomwe adachita: 8:36-38

C. Kusintha kupita ku Azotu: 8:39-40

III. Umboni wa Saulo: 9:1-31

A. Kusanthulika mtima kwa Saulo: 9:1-9

- 1. Cholinga chake: 9:1-2

2. Masomphenya ake: 9:3-9
3. Mawu ake: 9:4-7
4. Kuchita khungu: 9:8-9
- B. Kutumidwa kwa Saulo kudzera kwa Hananiya: 9:10-19
  1. Maitanidwe: 9:10-16
  2. Kutumidwa: 9:17-19
- C. Ntchito ya Saulo: 9:20-31
  1. Saulo ku Damasiko: 9:20-25
    - a. Umboni wake: 9:20-22
    - b. Zimene adachita: 9:21-23
    - c. Kuthawa kwake: 9:23-25
  2. Saulo ku Yerusalemu: 9:26-30
    - a. Kulandiridwa kwake: 9:26-28
    - b. Ntchito yake: 9:28-29
    - c. Kuchoka kwake: 9:29-30
- D. Kusintha: Mpukulo mu mpingo: 9:31

#### IV. Umboni wa Petulo: 9:32-12:35

- A. Ku Luda: 9:32-35
  1. Okhulupirira: 9:32
  2. Munthu wodwala: 9:33
  3. Kuchiritsidwa kwa munthu wodwala: 9:34
  4. Zomwe adachita: 9:35
- B. Ku Yopa: 9:36-43
  1. Imfa ya Dorika: 9:36-37
  2. Kuitanidwa kwa Petulo: 9:38-39
  3. Utumiki wa Petulo: 9:40-41
  4. Zotsatira za utumiki: 9:42-43
- C. Ku Kaisareya: 10:1-48
  1. Masomphenya a Koneriyo: 10:1-8
    - a. Koneriyo: 10:1-2
    - b. Masomphenya a Koneriyo: 10:3-6
    - c. Zomwe adachita Koneriyo: 10:7-8
  2. Masomphenya a Petulo: 10:9-22
    - a. Msomphenya: 10:9-12
    - b. Kulankhula: 10:13-16
  3. Kufika kwa otumidwa: 10:17-22
  4. Kufika kunyumba ya Koneriyo: 10:23-48

- a. Ulendo: 10:23
  - b. Kulandiridwa: 10:24-27
  - c. Chilongosolo: 10:27-28
  - d. Funso: 10:29
  - e. Yankho: 10:30-33
  - f. Ulaliki osamalizitsa: 10:34-43
    - (1) Mulungu opanda tsankhu: 10:34-35
    - (2) Kufalikira kwa Uthenga wabwino: 10:36-37
    - (3) Uthenga wa uthenga wabwino: 10:38-43
  - g. Zimene Koneriyo adachita: 8:44-48
- D. Ku Yerusalemu: 11:1-12:25
- 1. Vuto lobwera kamba ka kusandulika kwa a mitundu: 11:1-18
    - a. Vuto lake: 11:1-3
    - b. Kulongosola ntchito ya Mulungu pakati a mitundu: 11:4-17
      - (1) Masomphenya: 11:4-10
      - (2) Alendo: 11:11
      - (3) Ulendo: 11:12-16
    - c. Chisankho: 4:18

V. Mpingo wa ku Antiokeya ku Asuri: 11:19-30

- A. Chitsitsimutso cha ku Antiokeya: 11:19-21
- B. Kufika kwa Banaba: 11:22-24
- C. Saulo asankhidwa ngati mbusa wophunzitsa: 11:25-26
- D. Zimene Agabo anaulula: 11:27-30

VI. Chizunzo cha Herode: 12:1-25

- A. Kuphedwa kwa Yakobo: 12:1-2
- B. Kumangidwa kwa Petulo: 12:3-4
- C. Kumasulidwa kwa Petulo 12:5-19
- D. Imfa ya Herode: 12:20-23

VII. Kulalikidwa kwa Mawu: 12:24-25

**Gawo Lachinayi: Umboni ku dziko lonse lapansi  
Machitidwe 13-28**



I. Ulendo woyamba wochita utumiki: 13:1-14:28

- A. Kuitanidwa ku utumiki: 13:1-3
- B. Utumiki ku Pafo wa ku Ku: 13:4-12
- C. Utumiki ku Antiokeya wa Mpisidiya: 13:13-50
  - 1. Kupita ku Pisidiya: 13:13-16
  - 2. Uthenga: 13:17-37
    - a. Chipulumutso cha mu Eksodo: 13:17
    - b. Ulendo wa mu Chipululu: 13:18
    - c. Kugonjetsa Kanani: 13:19
    - d. Ulamuliro wa Saulo ndi Davide: 13:20-23
    - e. Utumiki wa Yohane Mbatizi: 13:24-25
    - f. Kupachikidwa ndi kuuka Kwa Yesu: 13:26-37
    - g. Kuitanidwa: 13:38-41
  - 3. Mmene adayankhira kuitanako: 13:42-50
- D. Utumiki ku Ikoniyo: 13:51-14:5
- E. Utumikiku Lustra: 14:6-25
- F. Utumiki ku Antiokeya: 14:26-28

II. Mkumano wa akuluakulu ku Yerusalemu: 15:1-35

- A. Vuto lake: 15:1-3
- B. Mkumano wa akuluakulu: 15:4-21
  - 1. Mkumano woyamba: 15:4-5
  - 2. Mkumano wa mseli wa atumwi ndi akuluakulu: 15:6
  - 3. Mkumano wachiwiri: 15:7-21
    - a. Uthenga wa Petulo: 15:7-11
    - b. Uthenga wa Paulo ndi Banaba: 15:12
    - c. Uthenga wa Yakobo: 15:13-21
- C. Chisankho: 15:19-21
- D. Makalata: 15:22-35

III. Ulendo wachiwiri wa utumiki: 15:36-18:22

- A. Kutsutsana: 15:36-41
- B. Utumiki wa ku Lustra: 16:1-5
- C. Utukiwa wa ku Trowa: 16:6-10
- D. Utumiki wa ku Filipo: 16:11-40

- E. Utumiki wa ku Tesalonika: 17:1-9
- F. Utumiki wa ku Bereya: 17:10-14
- G. Utumiki wa ku Atene: 17:15-34
- H. Utumiki wa ku Korinto: 18:1-18
- I. Utumiki wa ku Efeso: 18:19-21
- J. Yerusalemu ndi Antioki: 18:22

#### IV. Ulendo wachitatu wa utumiki: 18:23-21:14

- A. Ku Galatiya: 18:23
- B. Utumiki wa ku Efeso: 18:24-19:41
  - 1. Apolosi: 18:24-28
  - 2. Ophunzira a Yohane: 19:1-7
  - 3. Sukulu ya ku Turano: 19:8-12
  - 4. Ana a Skeva: 19:13-17
  - 5. Kupereke otembenuka: 19:18-20
  - 6. Chisankho: 19:21
  - 7. Otchinjiriza Demetriyo: 19:23-41
- C. Utumiki wa ku Makedoniya ndi ku Helene: 20:1-5
- D. Utumiki wa ku trowa: 20:6-12
- E. Utumiki wa ku Mitilene: 20:13-38
  - 1. Ulendo: 20:13-16
  - 2. Mkumano ndi akuluakulu a ku Efeso: 20:17-35
    - a. Kuunika utumiki wake: 20:17-21
    - b. Kuona za kutsogolo: 20:22-24
    - c. Chikumbumtima cha Paulo: 20:25-27
    - d. Chenjezo 20:28-31
    - e. Kuvomerezeka kwa Mulungu: 20:32
    - f. Chitsanzo cha Paulo mu mtsautso: 20:33-35
  - 3. Kusanzikana: 20:36-38
- F. Utumiki wa ku Turo: 21:1-6
- G. Utumiki wa ku Ptolemai: 21:7
- H. Utumiki wa ku Kaesareya: 21:8-14

#### V. Ulendo wotsiriza wa ku Yerusalemu ndi kwa Aroma: 21:15-28:31

- A. Yerusalemu: 21:15-23:32
  - 1. Kusintha kupita ku Yerusalemu: 21:15-17

2. Mphekesera zosutsana ndi Paulo: 21:18-30
    - a. Kuti anaphwanya chilamulo cha Mose: 21:18-26
    - b. Kuti anadetsa malo oyera: 21:27-30
  3. Zimene Paulo adachita: 21:23-26
  4. Kupulumuka kwa Paulo: 21:30-32
  5. Zimene Paulo adayankha: 21:33-23:10
    - a. Khamu la Chiyuda: 22:1-23
    - b. Kenturiyo wa Chiroma: 22:24-26
    - c. Kapitao wamkuru: 22:26-30
    - d. Bwalo la akuru: 23:1-10
      - (1) Chivomerezo cha Paulo: 23:1
      - (2) Kukumana ndi Mkulu wansembe: 23:2-5
      - (3) Kugawanika kwa bwalo: 23:6-10
  6. Chivumbulutso kwa Paulo: 23:11
  7. Chiwembu chofuna kupha Paulo: 23:12-15
  8. Kupulumuka kwa Paulo: 23:16-32
    - a. Chiwembu chiululika: 23:16-22
    - b. Kalata: 23:25-30
    - c. Kuthawa: 23-32
- B. Ku Kaesareya: 23:33-26:32
1. Pa maso pa Felike: 23:33-24:27
    - a. Chitsutso cha Tertulo: 24:1-9
    - b. Yankho la Paulo: 24:10-21
    - c. Yankho la Felike: 24:22-27
  2. Pamaso pa Festo: 25:1-12
  3. Felike ndi Agripa: 25:13-27
  4. Pamaso pa Agripa: 26:1-32
    - a. Paulo adzilankhulira yekha: 26:1-23
    - b. Kuitanira ku chipulumutso: 26:24-29
    - c. Chigamulo: 26:30-32
- C. Ulendo wa kwa Aroma: 27:17-28:31
1. Mafunde: 27:1-44
  2. Njoka: 28:1-6
  3. Machiritso: 28:7-10
  4. Ulendo upitilira: 28:11-15
- D. Kwa Aroma: 28:16-31
1. Mkumano ndi Ayuda: 28:16-29
  2. Utumiki: 28:30-31

## MAFUNSO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Machitidwe ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene analemba Machitidwe.

---

---

3. Kodi wolembe buku la Machitidwe analemba ndani?

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Machitidwe.

---

---

5. Lembani Vesi lotsogolera la buku la Machitidwe kuchokera pantima.

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Pangani dongosolo la tchati kuti muthe kuphunzira zozizwa zonse zomwe zikupezeka mu buku la Machitidwe.

Mtundu wa chozizwa Njira zomwe zinagwira ntchito Malo ake Anthu opezeka Zotsatira

2. Phunzirani maulaliki a Machitidwe, pangani dongosolo la tchati kuti mulembepo zomwe mwaphunzira:

Mabuku            Wolalikira            Anthu otumikiridwa    Chidule cha Uthenga

3. Phunzirani mapemphero onse omwe akupezeka mbuku la Machitidwe. Gwiritsani ntchito tchati pochita maphunzirowa.

Mabuku    Malo    Amene amapemphera    Chidule cha pemphero    Zotsatira za pemphero

4. Phunzirani moyo wa mtumwi Paulo pogwiritsa ntchito magawo awa:

-Mmene Paulo analili moyo wake: Machitidwe 22:3

-Mmene Paulo anazunzira Chikristu: Machitidwe 8:1-4; 9:1-2

-Kusandulika mtima kwa Paulo: Machitidwe 9:3-21

-Zaka zoyambirira za utumiki wa Paulo: Machitidwe 9:22-31; 11:22-30

-Ulendo woyamba wa umishoni: Machitidwe 13:1-14:28

-Akuluakulu a ku Yerusalemu: Machitidwe 15:1-35

-Ulendo wachiwiri wa umishoni: Machitidwe 15:36-18:22

-Ulendo wachitatu wa umishoni: Machitidwe 18:23-21:27

-Paulo amangidwa ku Yerusalemu, atumizidwa ku Kaesareya, pempho kwa Kaesara:  
Machitidwe 21:17-26:32

-Ulendo wa kwa Aroma kudzera pa nyanja: Machitidwe 27:1-44

-Ukapolo woyamba wa Paulo ku Aroma (zaka ziwiri): Machitidwe 28:1-31

-Maulendo otsiriza a Paulo: Aroma 15:28

-Ukapolo wachiwiri wa Paulo ndi kuphedwa kwake: II Timoteo 4:6

5. Mu Uthenga wa Luka, mtumwi Luka analeba zonse zimene Yesu anayamba kuchita ndi kuphunzitsa mthupi. Mu buku la Machitidwe Luka analemba zimene Yesu anapitiliza kuchita ndi kuphunzitsa kudzera mu thupi lake la Uzimu, ndiye Mpingo.

6. Phunzirani kufanana pakati pa utumiki wa Petulo ndi wa Paulo komwe kukupezeka mmbuku la Machitidwe mmachaputala alembedwawa:

### **Petulo**

Ulaliki woyamba: 2  
Munthu wopuwala achiritsidwa: 3  
Simoni wa nyanga: 8  
Mphamvu ya chithunzithunzi: 5  
Kusanjika manja: 8  
Petulo analambira: 10  
Tabita aukitsidwa: 9  
Petulo aikidwa mndende: 12

### **Paulo**

Ulaliki woyamba: 13  
Wopuwala achiritsidwa: 14  
Elemasi wamasenga: 13  
Mphamvu ya tinsalu: 19  
Kusanjika manja: 19  
Paulo analambira: 14  
Utiko aukitsidwa: 20  
Paulo atsekeredwa mndende: 28

7. Moyo wa mpingo woyamba unali:

-Wovomereza: 2:4  
-Wokhudzidwa: 2:7  
-Wotembenuka: 2:37  
-Wakhama: 2:42  
-Wopitilira: 2:46  
-Wachiyanjano: 2:46  
-Wofalikira: 2:47

8. Chidule cha zinthu izi chikuthandizani kukumbukira zomwe zikupezeka mbuku la Machitidwe:

-Munthu: Yesu Khristu  
-Mphamvu: Mzimu Woyera  
-Alaliki: Petulo, Paulo, Stefano, Filipino  
-Malo: Yerusalemu, Yudeya, Samaliya, Malekezero a dziko lapansi  
-Ntchito: Kukulitsa Uthenga wabwino

9. Mu Machitidwe 2, Petulo akuchitira umboni za uneneri womwe unaperekedwa kwa mneneri Yoweli. Mungathe kuwerenga uneneriwu mu buku la Yoweli 2:28-32.

## MAWU OYAMBA A MAKALATA

Gawo lotsatira Mchipangano Chatsopano ndiwo makalata. Ndipo makalatawa ali motere:

**Aroma:** Kalata imeneyi imapereka uthenga umene umatsindika za chipulumutso mwa chikhulupiriro chokha.

**I Akorinto:** Iyi inalembedwa ndi cholinga chofuna kukonza makhalidwe olakwika a akhristu mu mpingo.

**II Akorinto:** Kalatayi imakamba za utumiki weniweni wa Uthenga Wabwino, Woyang'anira bwino chuma ndi ulamuliro wa mtumwi Paulo.

**Agalatiya:** Uthenga wa mu kalatayi umalimbana ndi zolakwika za kusakaniza lamulo ndi chikhulupiriro. Mutu waukulu mu kalatayi ndi kulungamitsidwa ndi chikhulupiriro chokha basi.

**Aefeso:** Kalatayi inalembedwa ndi cholinga chofuna kulimbikitsa okhulupirira onse amene amagawana malo a kumwamba limidzi ndi Yesu ngati ziwalo za mpingo.

**Afilipi:** Kalatayi imasindika za chimwemwe chakukhala Mkhristu.

**Akolose:** Iyi imalimbana ndi zolakwikwa za chipunzitso cha bodza chakuti chipulumutso timachipeza pokhala anzeru. Chiphunzisochi chimakana kuti Yesu analidi Mwana wa Mulungu ndi Mwana wa Munthu.

**I Atesalonika:** Limapereka uphungu wa makhalidwe a Chikhristu ndi kutsindika pa zakubweranso kwa Yesu.

**II Atesalonika:** Limapereka malangizo oonjezera pa za kubwera kwa Ambuye Yesu, ndi mmene angakhalire moyo wa tsiku ndi tsiku atatha kuzindikira malangizowa.

**I Timoteo:** Kalatayi imatsindika za chiphunzitso cholondora, dongosolo la utsogoleri wa mpingo ndi mfundo zotsogolera mpingo mu zaka zamtsogolo.

**II Timoteo:** Iyi imalongosola za Yesu Mkhristu ngati Mtumiki weniweni. Limachenjezanso za kulowa pansu kwa moyo wa uzimu kumene kudayamba kale, ndi kuonetsera Mawu a Mulungu ngati chida chokonza zolakwikwa.

**Tito:** Iyi ndi kalata ya Paulo yolembera mtumiki wachichepere wotchedwa Tito amene amatumikira Mulungu pa chilumba cha Krete. Bukuli limakamba za chiphunzitso ndi moyo wa umulungu.

**Filemoni:** Kalata iyi ndi pembedzero la Paulo kwa kapolo yemwe anathawa kwa Filimoni yemwe anali Mkhristu wochita bwino kwa Akolose. Limaonetsera pembedzero la Yesu mmalo mwa okhulupirira onse amene anamasulidwa ku ukapolo wa uchimo.

**Ahebri:** Kalata iyi imalongosola za kupambana kwa Chikhristu kuyerekeza ndi Chiyuda. Komanso limamufotokoza Yesu ngati Mkulu wa Nsembe mkhala pakati pa Mulungu ndi anthu.

**Yakobo:** Buku ili limaphunzitsa za Chikhulupiriro chenicheni chokhala ndi ntchito zake, ngakhale chipulumutso chimachokera ku chikhulupiriro chokha.

**I Petulo:** Iyi ndi kalata ya chithonhozo komanso chilimbikitso kwa okhulupirira, makamaka iwo amene akulandira chizunzo cha muuzimu kuchokera kwa iwo amene ndi osakhulupirira ali kunja kwa mpingo.

**II Petulo:** Kalata iyi imapereka chenjenzo kwa iwo amene akupereka chiopsezo cha kuuzimu kuchokera kwa iwo amene ali mkati mwa mpingo. Mwachitsanzo aphunzitsi oneynga amene anali ndi ma udindo mu mpingo.

**I Yohane:** Iyi ndi kalata imene idalembedwa ndi cholinga chofuna kulimbana ndi chiphunzitso cha nzeru chimene chimene chimakana kuti Yesu ndi Mwana wa Mulungu komanso Mwana wa Munthu. Komanso limalimbikitsa za chiyanjano komanso chikondi pakati pa okhulupirira ndi kuwatsikimizira kuti za moyo osatha.

**II Yohane:** Kalata iyi imachenjeza za kusakaniza chikhristu ndi chiphunzitso cholakwikwa, komanso kuti choonadi chitsogoleledwe ndi chikondi.

**III Yohane:** Kalata iyi imachenjeza za tchimo losafuna kuyanjana ndi omwe ndi okhulupirira owona.

**Yuda:** Iyi imapereka chenjezonso koma lotsutsana ndi kulowa pansu kwa moyo wa uzimu ndi chiphunzitso cha bodza. Mutu wa kalatayi umafanana ndi kalata ya II Petulo.

**Chibvumbulutso:** Buku ili limapereka uneneri ndipo ndi buku lokhali mu chipangano chatsopano. Limaonetsera dongosolo la Mulungu ndi chimaliziro cha nthawi, kulengedwa kwa miyamba yatsopano ndi dziko latsopano, chiweruzo ndi chiambi cha nthawi zosatha.

## **MAGULU A MABUKU A MAKALATA**

Makalatawa akhonza kugawidwa moetre:

**Mabuku okhuzana ndi kubwera kwa Yesu:** I ndi II Atesanonika

**Mabuku omwe amatsindika za Uthenga Wabwino:** Aroma, Agalatiya, I ndi II Akorinto

**Mabuku omwe analemba Paulo akadali ku ndende:** Aefeso, Akolose, Afilipi, Filemoni

**Makalata a ubusa:** Awa ndi mabuku amene zitsanzo zenizeni za utsogoleri ndi dongosolo la mpingo. Makalatawa ndi I ndi II Timoteo ndi Tito.

**Makalata ena onse:** Awa ndi makalata onse amene atsalira.



“Apostasy” awa ndi awu amene mukuyenera kuwadziwa pamene mukupanga kafukufuku wa makalata. Mawuwa amanthauza kuti “kuchoka mchikhulupiriro.” Wolembe makalata mmakalata ambiri amalimbana ndi vutoli lomwe limapezeka mu mpingo.

## CHAPUTALA CHA 6

### AROMA

#### ZOLINGA

Pakutha pa mutu uwu muyenera:

- Kutchula wolembe buku la Aroma.
- Kudziwa amene amawalemba.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Aroma.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Aroma kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndo Mfundo ya Utumiki ya buku la Aroma.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**KULEMBA:** Okhulupirira a kwa Aroma

**CHOLINGA:** Kupereka tanthauzo la Uthenga mogwirizana ndi lamulo, uneneri ndi chosowa cha munthu kuti alungamitsidwe ndi chikhulupiriro.

**VESI LOTSOGOLERA:** Aroma 1:16-17

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Okhulupirira azakhala ndi moyo mwa chikhulupiriro

**ANTHU OPEZEKA:** Paulo, Adamu, Abrahamu, Isaki (Onani mndandanda wa maina mmutu 16)

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-7

A. Mnthenga: Paul: 1:1-6

1. Utumiki wa Yesu Khristu.
2. Kuitanidwa ngati mtumwi.
3. Kupatulidwa ku Uthenga Wabwino wa Mulungu.

B. Wowernga: 1:7

1. Wokhulupirira opezeka kwa Aroma.
2. Okondedwa ndi Mulungu.
3. Oyitanidwa kukhala oyera mtima.

C. Kupereka moni: Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu ndi Yesu: 1:7

II. Ubale wa Paulo ndi kwa Aroma: 1:8-16

- A. Kuwathokoza chifukwa cha iwo: 1:8
- B. Pemphero lake kwa iwo: 1:9-10
- C. Khumbo lake kwa iwo: 1:11-16
  - 1. Khumbo: 1:11
  - 2. Cholinga cha khumbo: 1:11-12
  - 3. Zotchinga kukukwaniritsa: 1:13
  - 4. Cholinga chenicheni chokhalira ndi khumbo: 1:14-16
    - a. Khumbo lobala chipatso: 1:14
    - b. Khumbo lake la kwa amitundu: 1:14
    - c. Changu chake kukulalikira Uthenga: 1:15
    - d. Kulimbika mtima kwake mu Uthenga wabwino: 1:16

III. Mawu okhudza za mutu waukulu wa buku: Uthenga wamphamvu umaulura chilungamo cha Mulungu: 1:16-17

**Gawo Loyamba: La Chiphunzitso**

**Chilungamo cha Mulungu chowululidwa mu Uthenga Wabwino**

**1:18-8:39**

I. Kusowa chilungamo cha Mulungu chifukwa cha tchito la aliyense: 1:18-3:20

- A. Chiweruzo cha anthu amitundu: 1:18-32
  - 1. Mkwiyu wa Mulungu pa Tchimo: 1:18
  - 2. Zifukwa za mkwiyo wa Mulungu: 1:19-23
    - a. Asowa chowiringula chifukwa cha kumdziwa Mulungu: 1:19-20.
    - b. Akadali mmachimo awo chifukwa cha kuononga chidziwitso cha Mulungu: 1:21-23
  - 3. Mkwiyu wa Mulungu: 1:24-32
    - a. Adawapereke ku zodetsa zawo: 1:24-25
    - b. Adawapereka ku zikhumbitso zawo zonyasa: 1:26-27
    - c. Adawapereka ku maganizo awo oyipitsitsa: 1:28-32
      - (1) Zotsatira za chisankho chawo: 1:28
      - (2) Mmene zinalili nyengo zawo: 1:28-32
- B. Chiweruzo cha Ayuda: 2:1-3:8

1. Mfundo ya chiweruzo cha umulungu: 2:1-16
  - a. Chiweruzo cha Mulungu molingana ndi choonadi: 2:1-5
    - (1) Tchimo loza kamba koweruza ena: 2:1
    - (2) Mfundo za chiweruzo: 2:2
    - (3) Pempfo la kwa ochimwa: 2:3-5
  - b. Chiweruzo cha Mulungu molingana ndi ntchito: 2:6-15
    - (1) Mfundo ya chiweruzo: 2:6
    - (2) Magawo awiri a muchiweruzo: 2:7-12
    - (3) Kumvera lamulo ngati muyeso wa chiweruzo: 2:13-15
  - c. Chiweruzo mogwirizana ndi Uthenga Wabwino wa Paulo: 2:16
2. Kulephera kwa Ayuda mmakhalidwe: 2:17-29
  - a. Mfundo za Ayuda: 2:17-20
  - b. Kukana mfundo za Ayuda: 2:21-24
  - c. Kulephera kukhala ndi udindo: 2:25-29
    - (1) Udindo wa mdulidwe: 2:25
    - (2) Udindo wa kumvera: 2:26-27
    - (3) Mamvetsetsedwe a Myuda owona ndi onama: 2:28-29
3. Kukuna kwa Ayuda: 3:1-8
  - a. Mafunso a Ayuda: 3:1-4
    - (1) Funso: 3:1
    - (2) Yankho: 3:2-4
    - (3) Chitsutso: 3:5
    - (4) Kukana chitsutsocho: 3:6-8
- C. Chiweruzo cha dziko lonse: 3:9-20
  1. Chigamulo choti onse anachimwa: 3:9
  2. Chitsimikizo cha tchimo la aliyense kuchokera mmalemba: 3:10-18
    - a. Chikhalidwe cha uchimo: 3:10-12
    - b. Mchitidwe wa uchimo: 3:13-17
      - (1) Mu zolankhula: 3:13-14
      - (2) Mu chikhalidwe: 3:15-17
    - c. Chifukwa kamba ka uchimo: 3:18
  3. Tanthauzo kwa Myuda yemwe ali ndi chilamulo: 3:19-20
- II. Chilungamo cha Mulungu polungamitsa: 3:21-5:21

- A. Kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro: 3:21-26
  - 1. Ichi ndi chionetsero cha chilungamo cha Mulungu: 3:21
  - 2. Kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro: 3:21-26
    - a. Ubale wake ndi Chipangano Chatsopano: 3:21
    - b. Kupezeka mwa chikhulupiriro: 3:22-23
    - c. Madziko ake pa chiombolo cha Yesu: 3:24-25
    - d. Kuonetsera chilungamo cha Mulungu: 3:25-26
- B. Chidule cha chiphunzitso cha kulungamitsa: 3:27-31
  - 1. Sikuwerengera kuyenera kwa munthu: 3:27-28
  - 2. Chithunzithunzi cha chikhalidwe cha Mulungu: 3:29-30
  - 3. Kukhazikitsidwa kwa lamulo: 3:31
- C. Chitsimikizo cha kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro Mmalemba: 4:1-25
  - 1. Kulungamitsidwa kwa Abrahamu: 4:1-12
    - a. Funso la zimene Abrahamu anadutsamo: 4:1
    - b. Mmene ungalungamitsidwire: 4:2-3
    - c. Kusiyantsa njira ziwiri zolungamitsa: 4:4-5
    - d. Chitsimikizo kuchokera ku umboni wa Davide: 4:6-8
  - 2. Kulungamitsa mwa chikhulupiriro osati mwa mdulidwe: 4:9-12
    - a. Funso lokhuza mdulidwe: 4:9-10
    - b. Mayankho a nyengo za Abrahamu: 4:10
    - c. Mdulidwe wa Abrahamu: 4:11-12
  - 3. Lonjezo likwaniritsidwa mwa chikhulupiriro: 4:13-17
    - a. Mmene tipezera cholowa: 4:13
    - b. Chifukwa cha njira ya chikhulupiriro: 4:14-15
    - c. Olandira lonjezo: 4:16
    - d. Chiyanjano ndi malemba: 4:17
  - 4. Chitsanzo cha chikhulupiriro cha Abrahamu: 4:17-25
    - a. Maziko a chikhulupiriro ake: 4:17
    - b. Chikhalidwe cha chikhulupiriro chake: 4:18-21
    - c. Mphoto ya chikhulupiriro chake: 4:22
    - d. Kufunika kwa chikhulupiriro chake: 4:23-25
- D. Umuyaya wa kulungamitsa: 5:1-11
  - 1. Zotsatira zake za kulungamitsa: 5:1-2
  - 2. Kulephera kwa mayesero kuthana ndi chiyembekezo: 5:3-5
    - a. Zotsatira za mayesero: 5:3-4

- b. Kuona chikondi cha Mulungu: 5:5
- 3. Chikondi cha Mulungu wa Khristu kumatsimikiza chiyembekezo: 5:6-11
  - a. Chikondi cha Mulungu: 5:6-10
    - (1) Kuonetsera chikondi cha Mulungu kwa otayika: 5:6-8
    - (2) Chitsimikizo cha chipulumutso: 5:9-10
  - b. Kukumana ndi chiyanjanitso: 5:11
- E. Maziko a chilungamo: 5:12-21
  - 1. Anthu awiri oimira: 5:12-14
    - a. Zotsatira za Adamu: 5:12-14
    - b. Udindo wa Adamu ngati Mkhristu: 5:14
  - 2. Kusiyana pakati pa Adamu ndi Khristu: 5:15-17
    - a. Mmakhalidwe: 5:15
    - b. Mu zochita: 5:16
    - c. Mu zotsatira: 5:17
  - 3. Kufanana pakati pa Adamu ndi Khristu: 5:18-21
    - a. Kufanana ku malire ntchito yawo: 5:18
    - b. Kufanana mu zochita: 5:19
    - c. Kufanana mu mulingo: 5:20-21

### III. Chilungamo cha Mulungu mu chiyeretso: 6:1-8:39

#### A. Ubale wa okhulupirira ku tchimo: 6:1-23

- 1. Kufa ku uchimo: 6:1-14
  - a. Funso la Uchimo: 6:1
  - b. Kukana maganizowo: 6:2
  - c. Mbali yathu mu ubatizo: 6:3-11
    - (1) Funso losadziwa lokhuza ubatizo: 6:3
    - (2) Kufunika kwa ubatizo: 6:4
    - (3) Ntchito yake kwa okhulupirira: 6:5-10
    - (4) Mayiyanidwe ku mbali imeneyi: 6:11
- 2. Imfa ya okhulupirira ku uchimo: 6:15-23
  - a. Funso la tchimo lopitilira: 6:15

- b. Kukana maganizowo: 6:15
  - c. Yankho kuchokera pa mmene umakhalira ukapolo wa munthu: 5:16-23
    - (1) Funso lokhuza kukhala ndi ambuye awiri: 6:16
    - (2) Zimene okhulupirira amakumana nazo pa kukhala ndi ambuye awiri: 6:17-18
    - (3) Pempho pa makhalidwe atsopano: 6:19
    - (4) Kusiyana kwa zithu ziwiro: 6:20-22
    - (5) Zotsatira za ambuye awiri: 6:23
- B. Ubale wa okhulupirira ku lamulo: 7:1-25
- 1. Kufa ku chilamulo ndi kukhala ndi moyo mwa Mulungu: 7:1-6
    - a. Mphamvu ya chilamulo: 7:1
    - b. Chitsanzo cha lamulo la ukwati: 7:2-3
    - c. Mmene limagwirira ntchito kwa okhulupirira: 7:4-6
  - 2. Kulephera kwa lamulo kuombola tchimo: 7:7-25
    - a. Ubale wa lamulo ku uchimo: 7:7-13
      - (1) Chikhalidwe cha lamulo si cha uchimo: 7:7
      - (2) Chivumbulutso cha tchimo mwa lamulo: 7:7-13
      - (3) Ntchito ya tchimo mwa lamulo: 7:8-11
      - (4) Chivumbulutso cha lamulo uchimo wa tchimo: 7:12-13
    - b. Kulephera kwa lamulo pa kugonjetsa tchimo: 7:14-25
      - (1) Chivomerezo choyamba cha kugonja kwa tchimo: 7:14-17
      - (2) Chivomerezo chachiwiri cha kupezeka kwa tchimo: 7:18-20
      - (3) Chivomerezo chachitatu ndi njira ya chigonjetso: 7:21-25
- C. Chigonjetso cha okhulupirira mwa Mzimu: 8:1-39
- 1. Chipulumutso ku zilakolako za thupi mwa Mzimu: 8:1-11
    - a. Ufulu wa okhulupirira wosalowa mkuweruzidwa: 8:1-2
    - b. Maziko a chipulumutso: 8:3
    - c. Cholinga cha chipulumutso: 8:4
    - d. Njira ya chipulumutso: 8:5-10
      - (1) Magulu awiri a anthu: 8:5
      - (2) Maganizo awiri: 8:6-7
      - (3) Magawo awiri: Thupi ndi mzimu: 8:8-11
    - e. Kumasulidwa ku imfa ya thupi: 8:11
  - 2. Moyo wa umwana mwa Mzimu: 8:12-17
    - a. Lamulo loyenda ndi Mzimu: 8:12-13

- b. Zizindikiro za moyo woyenda ndi Mzimu: 8:14-17
  - (1) Chitsogozo cha Mzimu: 8:14
  - (2) Chikhalidwe cha Mzimu: 8:15
  - (3) Umboni wa Mzimu: 8:16
  - (4) Cholowa cha okhulupirira: 8:17
- 3. Ulemerero mu nyengo ya Mtsautso: 8:18-30
  - a. Kusanthula masautso: 8:18
  - b. Chitsimikizo cha ulemerero: 8:19-30
    - (1) Chitsimikizo cha chilengedwe: 8:19-22
    - (2) Chitsimikizo cha chiyembekezo: 8:23-25
    - (3) Chitsimikizo cha Mzimu: 8:26-27
    - (4) Chitsimikizo cha machitachita a Mulungu mmoyo: 8:28
    - (5) Chitsimikizo cha machitachita a Mulungu opitilira mwa ife: 8:29-30
- 4. Chitsimikizo cha chigonjetso cha okhulupirira: 8:31-39
  - a. Ubale wa okhulupirira kwa Mulungu: 8:31-33
  - b. Ubale wa okhulupirira kwa Khristu: 8:34
  - c. Ubale wa okhulupirira ku nyengo zoipa: 8:35-39
    - (1) Kulephera kwa zoipa za dziko looneka kutisiyanitsa ndi Khristu: 8:35-37
    - (2) Kulephera kwa zoipa za dziko losanoneka kutisiyanitsa ndi Khristu: 8:38-39

**Gawo Lachiwiri: Za mu mbiri**

**Chilungamo cha Mulungu pamene akukhala ndi Israyeli ndi amitundu**

**9:1-11:36**

I. Chisoni cha Paulo chifukwa cha kukana kwa Israyeli: 9:1-5

- A. Kukhuzidwa kwake: 9:1
- B. Kuya kwa kukhuzidwa kwake: 9:2-3
- C. Maziko a kukhuzidwa kwake: 9:3-5

II. Kukana kwa Israyeli ndi Ulamuliro wa Mulungu: 9:6-29

- A. Kukana kwa Israyeli ndi lonjezo la Mulungu: 9:6-13



1. Kukana pa kulephera kwa Mawu a Mulungu: 9:6
  2. Chitsimikizo chakuti lonjezo silinabwere kudzera mwa thupi: 9:6-13
    - a. Chitsimikizo cha kubanja la Abrahamu: 9:6-9
    - b. Chitsimikizo cha ku banja la Isaki: 9:10-13
- B. Kukana kwa Israyeli ndi Chilungamo cha Mulungu: 9:14-29
1. Chilungamo cha Mulungu mchifuniro chake: 9:14-18
    - a. Funso la chilungamo cha Mulungu: 9:14
    - b. Vumbulutso la chifuniro chake: 9:15-17
      - (1) Chifundo chake chiulura chifuniro chake: 9:15-16
      - (2) Chiweruzo chake chioneka mu chifuniro chake: 9:17
    - c. Ntchito yake mu chifuniro chake: 9:18
  2. Mphamvu ya Ulamuliro wa Mulungu: 9:19-29
    - a. Funso ndi chidzudzulo: 9:19-20
    - b. Ufulu wa Mulungu mu tchito: 9:20-21
    - c. Kuonetsera mphamvu za Mulungu: 9:22-24
      - (1) Kuleza mtima kwake ndi oyipa: 9:22
      - (2) Vumbulutso la ulemmero wake: 9:22-24
    - d. Kuyembekezera kuitana Ayuda ndi Amitundu: 9:25-29
      - (1) Kuitana Amitundu: 9:25-26
      - (2) Kulengeza zokhuza tsogolo la Israyeli: 9:27-29
- III. Kukana kwa Israyeli: 9:30-10:21
- A. Kulephera kwa Israyeli kufikira chilungamao: 9:30-33
    1. Zoonza zake zenizeni za kulephera kwa Israyeli: 9:30-31
    2. Chifukwa chimene Israyeli walepherera: 9:32
    3. Mmene Israyeli walepherera: 9:32
    4. Chitsimikizo cha zotsatira: 9:32
  - B. Kukana kwa Israyeli kulandira chilungamo cha Mulungu: 10:1-11
    1. Chomwe chidayambitsa kukana kwa Israyeli: 10:1-4
    2. Chikhalidwe cha chilungamo mwa chikhulupiriro: 10:5-11
      - a. Kufanitsa njira ziwiri za chilungamo: 10:5-8
        - (1) Chilungamo chobwera chifukwa chosunga lamulo: 10:5
        - (2) Chilungamo chobwera chifukwa cha chikhulupiriro: 10:6-8
      - b. Kuzindikira chilungamo chochokera ku chikhulupiriro: 10:9-10
      - c. Chitsimikizo cha malemba pa za chilungamo cha chikhulupiriro: 10:11
  - C. Kunyalanyaza kwa Israyeli pa Uthenga wabwino wa wina aliyense: 10:12-21
    1. Zoonza zake za Uthenga Wabwino wa wina aliyense: 10:12-13
    2. Kulengeza za Uthenga Wabwino wa wina aliyense: 10:14-15

3. Zimene Israyeli anachita pa Uthenga Wabwino wa wina aliyense: 10:16-21
  - a. Sunasamalidwe: 10:16-17
  - b. Udakanidwa: 10:18-21

IV. Kukana kwa Israyeli ndi cholinga cha Mulungu pa za tsogolo lawo: 11:1-32

- A. Kukana sikunali kwa Israyeli onse ena anasala: 11:1-10
  1. Kukana kuti Mulungu wayiwala mtundu wake: 11:1-2
  2. Chitsimikizo cha za osalawo: 11:2-6
    - a. Chitsimikizo chochokera mmalemba: 11:2-4
    - b. Chitsimikizo chochekera kwa osalawo: 11:5-6
  3. Kusi yana kwa osalawo ndi mtundu wonse: 11:7-10
- B. Kukana kwa Israyeli si kwamuyaya: 11:11-32
  1. Nyengo yomwe Israyeli analimo: 11:11-16
    - a. Kugwa kwa Israyeli si kwamuyaya: 11:11
    - b. Kugwa kwa Israyeli kunatsegulira chipulumutso kwa amitundu: 11:11
    - c. Kubwenzeretsedwa kwa Israyeli kuzabweretsa madalitso kwa aliyense: 11:12-15
    - d. Chizindikiro cha tsogolo la Israyeli kuchokera pakale: 11:16
  2. Chenjezo la anthu amitundu: 11:17-24
    - a. Lotsutsana kudzitamanda: 11:17-18
    - b. Lotsutsana kudzikonda: 11:19-21
    - c. Lotsutsana ndi kuoneka ngati ozindikira: 11:22-24
  3. Kusamvetsetsana pa kubwenzeretsedwa kwa Israyeli: 11:23-24
  4. Uneneri wa kubwenzeretsedwa kwa Israyeli mtsogolo: 11:25-32
    - a. Vumbulutso la kubwenzeretsedwa kwa Israyeli: 11:25-26
    - b. Chiyanjano chobwenzeretsa ndi uneneri: 11:26-27.
    - c. Chiyanjano ndi kuitanidwa kwa Israyeli: 11:28-29
    - d. Chiyanjano ndi cholinga cha Mulungu: 11:30-32

V. Nyimbo ya matamando a kwa Mulungu: 11:33-36

- A. Chilengezo cha Mulungu: 11:33
- B. Mafunso okhuza Mulungu: 11:34-35
- C. Matamando a kwa Mulungu: 11:36

**Gawo Lachitatu: Machitachita**  
**Chilungamo cha Mulungu kwa okhulupirira**  
**12:1-15:13**

I. Ubale wa okhulupirira ndi Mulungu: 12:1-2

- A. Kuzionetsera kwa Mulungu: 12:1
- B. Kukumana ndi kusintha kopitilira: 12:2

II. Ubale wa okhulupirira ndi Mpingo: 12:3-13

- A. Kugwiritsa nrchito mphatso za Mzimu modzichepetsa: 12:3-8
  - 1. Kufunika kodzichepetsa: 12:3
  - 2. Ubale wa ziwalo za mpingo muthupi: 12:4-5
  - 3. Kuonetsera kudzichepetsa mu utumiki: 12:6-8
    - a. Kuchuluka kwa mphatso zimene zapatsidwa: 12:6
    - b. Mphatso zotumikira: 12:6-8
- B. Kuonetsera chikondi ku ziwalo za mumpingo: 12:9-13
  - 1. Chikhalidwe cha chikondi: 12:9
  - 2. Kuonetsera chikondi: 12:9-13
    - a. Chopanda chinyengo: 12:9
    - b. Dana nacho choipa: 12:9
    - c. Chita chimene ndi chabwino: 12:9
    - d. Khalani okoma mtima ndi wina ndi mzache: 12:10
    - e. Onetseranani chikondi cha pa ubale: 12:10
    - f. Chitiranani ulemu wina ndi mzache: 12:10
    - g. Musakhale aulesi mmachitdwe anu: 12:11
    - h. Khalani achangu muuzimu: 12:11
    - i. Tumikirani Ambuye: 12:11
    - j. Kondwerani muchiyembekezo: 12:12
    - k. Khalani oleza mtima mumtsautso: 12:12
    - l. Limbikani kupemphera kosaleka: 12:12
    - m. Patsani zosowa oyera mtima: 12:13
    - n. Cherezani alendo: 12:13
    - o. Dalitsani omwe akuzunza inu: 12:14
    - p. Kondwani nawo iwo akukondwrea: 12:15
    - q. Lirani nawo iwo akulira: 12:15
    - r. Khalani ndi mtima umodzi wina ndi mzache: 12:16
    - s. Musafune zinthu zapamwamba koma phatikizanani ndi odzichepetsa: 12:16
    - t. Musakhale anzeru mwa inu nokha: 12:16
    - u. Musabwenzere muntu choipa ndi choipa: 12:17
    - v. Ganizirani zinthu zaulemu kwa anthu onse: 12:17
    - w. Khalani pa mtendere ndi anthu onse: 12:18
    - x. Musabwenzere mwa inu nokha: 12:19

- y. Kondani ndi kusamalira adani anu: 12:20
- z. Musagonjetsedwe ndi choipa koma ndi chabwino gonjetsani choipa: 12:21

III. Ubale wa okhulupirira kwa anthu onse: 12:14-21

- A. Kondani adani anu: 12:14
- B. Chikondi chosamalira za ena: 12:15
- C. Chikondi cha anzanu: 12:16
- D. Chikondi cha pa dziko loipa: 12:17-21
  - 1. Kulephera kuchita choipa: 12:17-19
  - 2. Kuchita change pa choipa: 12:20-21

IV. Ubale wa okhulupirira ndi dziko: 13:1-14

- A. Ntchito za okhulupirira ku akulu a boma: 13:1-7
  - 1. Ntchito ya kumvera ku boma: 13:1
  - 2. Chifukwa chimene timamvera a boma: 13:1
  - 3. Kukana kumvera a boma: 13:2
  - 4. Zolinga zotipangisa kumvera a boma: 13:3-5
    - a. Kuyambira ntchito zake za boma: 13:3-4
    - b. Kuyambira chikumbumtima cha Mkhristu: 13:5
  - 5. Chitasnzo cha kumvera boma: 13:6
  - 6. Pakufunika kumvera boma: 13:7
- B. Ntchito za okhulupirira kwa mzika nzawo: 13:8-10
- C. Chilimbikitso cha okhulupirira pa chiyembekezo cha kubweranso kwa Yesu: 13:11-14
  - 1. Pempho kuti akhale tcheru: 13:11
  - 2. Chifukwa chokhalira tcheru: 13:11-12
  - 3. Chilimbikitso pa kukhala tcheru: 13:12-13
  - 4. Zoyenera pa kukhala tcheru: 13:14

V. Ubale wa okhulupirira kwa pa ofoka: 14:1-15:13

- A. Chenjezo la kuweruza wina: 14:1-12
  - 1. Malingaliro abwino kwa ofoka: 14:1
  - 2. Madera ovutirapo: 14:2-5
    - a. Vuto loyamba ndi masinthidwe ake: 14:2-4
    - b. Vuto lachiwiri ndi masinthidwe ake: 14:5
  - 3. Kubweretsa kusintha: 14:6
  - 4. Chotilimbikitsa: 14:7-9
  - 5. Chidzudzulo pa kuweruza ena: 14:10-12

- a. Funso la chidzudzulo: 14:10
- b. Maziko a chidzudzulo: 14:10-12
- c. Kuletsa kuphwanya chikumbumtima cha mbale: 14:13-23
  - (1) Chilimbikitso pa kusaweruzana: 14:13
  - (2) Chikumbumtima cha mtumwi pa zakudya: 14:14
  - (3) Ntchito ya chikumbumtimayi mmakhalidwe: 14:15-20
  - (4) Mfundo zotsogolrea kwa mbale wamphamvu: 14:21
  - (5) Pempho kwa mbale wa mphamvu ndi wofooka: 14:22-23
- B. Mmene tingakhalire pa umodzi pa kusanza Yesu: 15:1-13
  - 1. Lamulo la mbale wamphamvu: 14:1
  - 2. Pempho la umodzi pa chitsanzo cha Yesu: 4:2-4
    - a. Mawu okhuza pempho: 14:2
    - b. Mitsutso yokhuza pempho: 14:3
      - (1) Chitsanzo cha Yesu: 14:3
      - (2) Cholinga cha Malemba: 14:4
  - 3. Pempho la mtumwi: 15:5-6
  - 4. Lamulo lololerani wina ndi nzake: 15:7
  - 5. Chitsanzo kuchokera ku ubale wa Yesu pakati pa Ayuda ndi Amitundu: 15:8-12
    - a. Utumiki wa Mkhristu: 15:8-9
    - b. Chitsimikizo cha mmalemba: 15:9-12
  - 6. Pemphero la utumwi: 15:13

**Mawu Otsiriza**  
**15:14-16:20**

- I. Zokhuza munthu: 15:14-33
  - A. Cholinga chimene Paulo amalemba: 15:14-21
    - 1. Malingaliro ake pa kulemba: 15:14-16
      - a. Kuwazindikira kwake: 15:14
      - b. Kulimba mtima kwake mwa iwo: 15:15
      - c. Mawu pa kutumidwa kwake: 15:16
    - 2. Ulamuliro wake pa kulemba: 15:17-21
      - a. Kudzitamandira kwake: 15:17
      - b. Kudzichepetsa kwake pochita ntchito yake: 15:18
      - c. Utumiki wake kwa Amitundu: 15:18-19
      - d. Cholinga chake pakusankha munda wa ntchito: 15:20-21
  - B. Malingaliro ake munthawi imene amalemba: 15:22-29
    - 1. Malingaliro osakwaniritsidwa: 15:22-24

- a. Malingaliro oyendera kwa Aroma: 15:22-23
- b. Malingaliro ake a ku Spanya: 15:24
- 2. Malingaliro ake achangu: 15:25-27
  - a. Malingaliro ake atsopano: 15:25
  - b. Kufunika kwa malingaliro ake atsopano: 15:26-27
- 3. Mlaingaliro ake amtsogolo: 15:28-29
- C. Pempho lake pa mapemphero awo: 15:30-33
  - 1. Pempho la pemphero: 15:30-32
  - 2. Nyimbo: 15:33

## II. Zokhuza maubale: 16:1-23

- A. Mayamikiro a Febe: 16:1-2
- B. Moni kwa abale a kwa Aroma: 16:3-16
  - 1. Moni kwa aliyense wa kwa Aroma: 16:3-15
  - 2. Moni wa okhulupirira a kwa Aroma: 16:16
  - 3. Moni kuchokera ku mipingo kupita kwa okhulupirira a kwa Aroma: 16:16
- C. Chenjezo kwa okhulupirira a kwa Aroma: 16:17-20
  - 1. Zopezeka mu chenjezero: 16:17
  - 2. Mtundu wa anthu amene akuwachenjeza: 16:18
  - 3. Chifukwa chimene akuwachenjezera: 6:19
  - 4. Lonjezo la chigonjetso: 16:20
  - 5. Nyimbo: 16:20
- D. Moni wa abwenzi ache: 16:21-24

## III. Nyimbo yomaliza: 16:25-27

- A. Olandira matamando: 16:25-27
  - 1. Iye amene ali ndi kuthekera kowakhazikitsa: 16:25-29
  - 2. Mulungu yekhayo wanzeru mwa Khristu: 16:27
- B. Matamando: 16:27

**MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Aroma ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chomwe amalemba buku la Aroma.

---

---

---

3. Kodi bukuli amalemba ndani?

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo za Utumiki za buku la Aroma.

---

---

---

5. Lembani Vesi lotsogolera la buku la Aroma kuchokera pantima.

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Buku la Aroma limanena mwa chimvemvemve za mkwiyo wa Mulungu pa kuipitsitsa kwa munthu pa nkhani zogonana.
2. Aroma amalongosolanso bwino za mmene Mulungu anachitira ndi mtundu wa Israyeli kuchokera kumbuyo, tsopano ngakhale ndi mtsogolo. Onani machaputala 9 mpaka 11.
3. Bukuli mulinso nyimbo zisanu kapena kuti madalitso zimene zimapereka mawuotsiriza a bukuli. Onani 11:33-36; 15:30-33; 16:20; 16:24-27.
4. Zotsatira zisanu ndi ziwiri za kulungamitsidwa ndi chikhulupiriro zikupezeka pa Aroma 5:1-11. Kulungamitsidwa ndi chikhulupiriro zimatanthauza kuti:
  - Tili ndi mtendere ndi Mulungu.
  - Tili ndi mwayi wa chikhulupiriro.
  - Tikondwera mu chiyembekezo cha ulemerero.
  - Ulemerero mmatsautso.
  - Kukhala ndi chikondi cha Mulungu chotsanulidwa mmitima yathu
  - Tidzapulumuka ku mkwiyo wa Mulungu.
  - Kukhala ndi chimwemwe mwa Mulungu.
5. Pali imfa zitatu zimene zikupezeka mbuku limeneli la Aroma monga:
  - Kufa ku uchimo, kukhala ndi moyo kwa Mulungu: 6:11
  - Kufa ku chilamulo, kukwatiwa ndi Mkhristu: 7:4
  - Kufa kuthupi, kutsogozedwa ndi Mzimu: 8:18



## **CHAPUTALA CHA 7**

### **I NDI II AKORINTO**

#### **ZOLINGA:**

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba I ndi II Akorinto.
- Kuzindikira omwe amawalemba.
- Kutchula zolinga zomwe amalemba I ndi II Akorinto.
- Kulemba ma Vesi otsogolera a buku la I ndi II Akorinto kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo za Utumiki za mabuku onse awiri.

### **I AKORINTO**

#### **MAWU OYAMBA**

**WOLEMBA:** Paulo

**KULEMBERA:** Okhulupirira a kwa Akorinto

**CHOLINGA CHOLEMBERA:** Paulo analemba ndi cholinga chofuna kuthetsa mavuto omwe adamudziwitsa komanso kuyankha ena mwa mafunso amene Akhristu a ku Akorinto anamufunsa.

**VESI LOTSOGOLERA:** I Akorinto 13:13

**MOYO NDI MFUNZO YA UTUMIKI:** Chikondi ndiye chida cha uzimu chapamwamba pa moyo ndi utumiki wa Khristu.

**ANTHU OPEZEKAMO:** Paulo, Timoteo, Apolo, Stefano (Onani mayina enanso kumapeto kwa ndime ya 16).

### **MAGAWO**

I. Mawu oyamba: 1:1-9

- A. Olemba: Paulo ndi Sositene: 1:1
- B. Owerenga: 1:2
  - 1. Kumpingo wa Mulungu kwa Akorinto.
  - 2. Iwo amene ayeretsedwa mwa Khristu Yesu.
  - 3. Iwo amene aitanidwa kuti akhale oyera mtima.
  - 4. Iwo onse amene kulikonse amaitanira pa dzina la Yesu Khristu.
- C. Moni: Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu ndi Yesu: 1:3
- D. Chiyamiko: 1:4-8
  - 1. Chikhalidwe cha chiyamiko: 1:4
  - 2. Maziko a chiyamiko: 1:4
  - 3. Chiyamiko chifukwa cha kudzadzidwa kwawo kwa kale: 1:5-6
  - 4. Chiyamiko chifukwa cha nyengo zawo za tsopano: 1:7-8
- E. Chitsimikizo chawo cha chikhulupiriro: 1:9

## II. Magawano a mpingo: 1:10-4:21

- A. Mmene adachitira atamva za kugawana kwawo: 1:10-17
  - 1. Pempho la umodzi: 1:10
  - 2. Kumene uthenga unachokera okhuza kugawana: 1:11
  - 3. Chikhalidwe cha magawano awo: 1:12
  - 4. Kufunsa za kugawana kwawo: 1:13
  - 5. Kugawana kwawo si kamba ka utumiki wake: 1:14-17
- B. Mitsutso yokhuza kugawana kwa mpingo: 1:18-4:5
  - 1. Kugawana sikugwirizana ndi Uthenga wabwino: 1:18-3:4
    - a. Uthenga sukhala mu mzeru ya dziko: 1:18-2:5
      - (1) Chitsimikizo kuchokera ku zotsatira za Uthenga: 1:18-25
      - (2) Chitsimikizo kuchokera ku mmene mpingo ulili: 1:26-31
      - (3) Chitsimikizo kuchokera ku ntchito za Paulo: 2:1-5
    - b. Uthenga ndi mzeru ya kumwamba: 2:6-3:4
      - (1) Olandira mzeruyi: 2:6
      - (2) Chikhalidwe cha mzeruyi: 2:6-12
      - (3) Matengedwe a mzeruyi: 2:13-3:4
  - 2. Mmene atumiki olondora ayenera kukhalirira: 3:5-4:5

- a. Atumiki ndi ogwira ntchito mmunda wa Mulungu: 3:5-9
  - (1) Ntchito za atumiki: 3:5
  - (2) Ntchito ndi mphoto za atumiki: 3:6-8
  - (3) Chidule cha chiphunzitso: 3:9
- b. Atumiki ndi iwo omanga nyumba ya Mulungu: 3:10-23
  - (1) Ntchito ya omanga idzayetsedwa: 3:10-15
  - (2) Kuonongeka kwa nyumba ya Mulungu kukulangidwa: 3:16-17
  - (3) Chilimbikitso cha mmene amawaonera atumiki: 3:18-23
- c. Atumiki ndi adindo oyang'anira zinsisi za Mulungu: 4:1-5
  - (1) Mnene amaonera anthu za kukhala atumiki: 4:1
  - (2) Kufunika kwa kukhulupirika ngati adindo a Mulungu: 4:2
  - (3) Ambuye ali ngati oweruza adindo: 4:3-4
  - (4) Pempho loti asaweruza kufikira Ambuye abwere: 4:5

### C. Pempho kwa Akorinto: 4:6-21

- 1. Tanthauzo la mtsutso mmagawano awo: 4:6-21
  - a. Cholinga cha tanthauzo: 4:6
  - b. Kulephera kuzindikira luso ndi mphoto: 4:7
  - c. Zotsatira: 4:8
  - d. Zimene atumwi adakumana nazo: 4:9-13
    - (1) Malo a pansa a atumwi: 4:9
    - (2) Kusiyana kwa iwo ndi aku Akorinto: 4:10
    - (3) Chilongosolo cha zimene adakumana nazo: 4:11-13
- 2. Pempho loti atsatire chitsanzo chake: 4:14-17
  - a. Cholinga cha chimene amalemba: 4:14
  - b. Ubale wake ngati tate wawo muuzimu: 4:15-16
  - c. Chifukwa chimene amawatumizira Timoteyo: 4:17
- 3. Chenjezo lakuti malingaliro awo adzapangitsa kuti awalankhule: 4:18-21
  - a. Malingaliro odzikweza a okhulupirira ena: 4:18
  - b. Kubwera kwa Paulo kwa Akorinto: 4:19-21

### III. Mavuto a makhalidwe mu mpingo: 5:1-6:20

#### A. Za chigololo: 5:1-13

- 1. Mwambo kwa amene agona ndi achibale ake: 5:1-8
  - a. Chikhalidwe cha tchimo: 5:1
  - b. Kulephera kwa mpingo kuchitapo kanthu: 5:2

- c. Chiweruzo cha muthu wolakwa: 5:3-5
- d. Pempho kwa mpingo kuti uchitepo kanthu: 5:6-8

2. Mfundo yomwe angatsate pothana ndi vutoli: 5:9-13

- a. Malingizo ake a poyamba: 5:9-11
- b. Kufunika kwa kuchitapo kanthu pa mfundoyi: 5:12-13

B. Tchimo la kuweruzana mlandu pachibale usanafike ku mabwalo a dziko: 6:1-11

- 1. Funso la chiweruzo cha pachibale: 6:1
- 2. Zifukwa zothetsera mavuto mu mpingo: 6:2-6
  - a. Chifukwa cha ntchito yoweruza ya kutsogolo: 6:2-3
  - b. Chifukwa cha chiweruzo chawo pa iwo osayenera: 6:4-5
  - c. Chifukwa zimaonetsa kulephera kwa mpingo pa kupereka chigamulo: 6:5-6
- 3. Zotsatira: 6:7-8
- 4. Chenjezo pa zosalungama: 6:9-11

C. Chiyero cha thupi: 6:12-20

- 1. Malire a ufulu wa Mkhristu: 6:12
- 2. Magwiritsidwe ntchito ake a mfundoyi magawo awiri: 6:13-14
  - a. Ku zakudya: 6:13
  - b. Ku zachigololo: 6:13-14
- 3. Chikhalidwe cha thupi la okhulupirira pokana chiwerewere: 6:15
- 4. Kusiyanana pakati pa ziyanjano ziwiri: 6:16-17
- 5. Chenjezo kuti athawe chiwerewere: 6:18
- 6. Chikhalidwe cha tchimo la chiwerewere: 6:18
- 7. magwiritsidwe ntchito a thupi oyenera: 6:19-20

IV. Ukwati: 7:1-40

A. Vuto la ukwati ndi kukhala osakwatira (kukhala osakwatira chifukwa chotumikira Mulungu): 7:1-9

- 1. Mwayi wokhala munthu yekha: 7:1
- 2. Malngizo kwa amene ali mbanja: 7:2-6
  - a. Chifukwa chosankha kukhala mbanja: 7:2
  - b. Chikhalidwe cha maubale a mbanja: 7:2
  - c. Ntchito za maubale a mbanja: 7:3-4
  - d. Malangizo pa za kugonana: 7:5-6

3. Kuzindikira kuti ukwati ndi kusakhala mu ukwati ndi zabwino: 7:7

4. Malangizo kwa osakwatira: 7:8-9
- B. Vuto la ukwati ndi kulekana: 7:10-16
1. Langizo kwa a khristu a pabanja: 7:10-11
    - a. Lamulo la langizolo: 7:10
    - b. Zomwe zili mu langizolo: 7:10-11
  2. Langizo kwa iwo ali ndi mabanja ambiri: 7:12-16
    - a. Chikhalidwe cha langizolo: 7:12
    - b. Zomwe zili mu langizolo: 7:12-16
      - (1) Kusi yana osati chifukwa cha okhulupirira: 7:12-14
      - (2) Kusi yana chifukwa cha osakhulupirira: 7:15-16
- C. Moyo wa okhulupirira ndi malo awo pa dziko: 7:17-24
1. Maziko a moyo wa okhulupirira: 7:17
  2. Kugwiritsa ntchito mazikowa mmoyo: 7:18-24
    - a. Kugwiritsa ntchito mfundozi pa kuumba chipembedzo chapaderadera: 7:18-20
    - b. Kugwiritsa ntchito mfundozi ku moyo wa okhulupirira wa tsiku ndi tsiku: 7:21-24
- D. Malangizo kwa iwo osakwatira: 7:25-40
1. Malangizo kwa iwo sanalowepo mbanja: 7:25-35
    - a. Chikhalidwe cha langizo: 7:25-27
    - b. Chifukwa choperekera langizo: 7:28-31
    - c. Ufulu wochokera ku langizo: 7:33-35
  2. Malangizo kwa makolo a ana akazi a pabanja: 7:36-38
    - a. Nyengo zimene banja likuyenera kuvomerezedwa: 7:36
    - b. Nyengo zimene chilolezo cha banja sichikulolodwa: 7:37

- c. Zonse ndi zabwino: 7:38
- 3. Langizo kwa akzi amasiye: 7:39-40
- V. Zakudya zoperekedwa ku mafano: 8:1-11:1
- A. Ubale wa chikondi ndi chidziwitso: 8:1-13
  - 1. Kusowa kwa chikondi ndi chidziwitso: 8:1-3
  - 2. Kufuna ufulu mwa chidziwitso: 8:4-8
    - a. Ufulu pa kudya: 8:4-6
    - b. Ngozi kwa mbale ofooka: 8:7
    - c. Chakudya sichitiyeneleza pamaso pa Mulungu: 8:8
  - 3. Chenjezo pa kuchimwitsa mbale ofooka: 8:9-12
    - a. Chenjezo kwa iwo amene ali ndi chidziwitso: 8:9
    - b. Zotsatira za chidziwitsochi: 8:10
    - c. Kuopsa kwa kuchitapo kanthu pa chidziwitsocho: 8:11-12
    - d. Kusankha kukhala osakhumudwitsa mbale chifukwa cha ufulu: 8:13
- B. Chisanzo cha Paulo pa kusankha kuti asakhumudwitse: 9:1-27
  - 1. Ulamuliro wake ngati mtumwi: 9:1-3
  - 2. Ufulu wake ngati mtumwi: 9:4-12
    - a. Ufulu wake aulengeza: 9:4-7
    - b. Chilungamisyo cha kulengezako: 9:8-12
  - 3. Chifukwa cholengezera ufulu wake: 9:12-23
    - a. Sazatchinga Uthenga wabwino: 9:12-14
    - b. Zikumpatsa chifukwa chozitamndirira: 9:15-18
    - c. Zikumpatsa kuthekera kobweretsa ena kwa Mkhristu: 9:19-23

4. Pempho kwa iwo kuti atsatire chitsanzo chake: 9:24-27
- C. Nkhani ya Israyeli ngati chenjezo kuti asagwiritse ntchito ufulu wawo molakwika: 10:1-13
1. Chikumbutso ku mbiri ya Israyeli: 10:1-5
    - a. Mimwayi ya Israyeli: 10:1-4
    - b. Tsogolo la Israyeli: 10:5
  2. Machenejezo kuchokera ku mbiri ya Israyeli: 10:6-10
    - a. Phunziro la mbiri ya Israyeli: 10:6-10
      - (1) Chenjezo pa za chilakolako: 10:6
      - (2) Zitsanzo zenizeni: 10:7-10
    - b. Kufunikira kwa zomwe Israyeli anadutsamo: 10:11
  3. Chilimbikitso kamba ka iwo akuyesedwa: 10:12-13
    - a. Kuzindikira kuopsa kwa kugwa: 10:12
    - b. Chilimbikitso kwa iwo akuyetsedwa: 10:13
  4. Pempho kuti apewe mafano: 10:14-22
    - a. Thawani mafano: 10:14
    - b. Mtsutso pa kutenga nawo mbali: 10:15-22
      - (1) Mtsutso wa olandira: 10:15
      - (2) Kufinika kwa kutenga nawo mbali: 10:16-22
- D. Chidule cha makhalidwe abwino: 10:23-11:1
1. Malire pa ufulu wa mkhristu: 10:23
  2. Kuganizira ena za bwino: 10:24
  3. Malangizo pa nyama yogulitsidwa: 10:25-30
    - a. Malangizo kwa iwo odyera kunymba: 10:25-26

b. Malangizo kwa iwo akudya ndi osakhulupirira: 10:27-30

E. Malangizo otsiriza: 10:31-11:1

1. Chitani ulemerero onse wa Mulungu: 10:31

2. Sungani ubale wabwino ndi onse: 10:32-33

3. Tsatirani chitsanzo cha atumwi: 11:1

VI. Chipembedzo: 11:2-14:40

A. Zophimba za akazi: 11:2-16

1. Matamando pa kumvera kwawo: 11:2

2. Mfundo ya kukhala malo pansi: 11:3-6

3. Kukhazikitsa mfundo ya malo a pansi: 11:7-15

a. Kuchokera ku ubale wa chilengedwe: 11:7-12

b. Kuchokera ku ubale wa uzimu: 11:13-15

c. Kumalizitsa zokambirana: 11:16

B. Chisokonezo pa mgonero wa Ambuye: 11:17-34

1. Chisokonezo cha Akorinto pa mgonero wa Ambuye: 11:17-22

a. Chikhalidwe cha chisokonezo: 11:18-21

(1) Zimene zinamvekapo pa za magawano: 11:18-19

(2) Mmene chisokonezo chinalili pa mgonero wa Ambuye: 11:20-21

b. Kudzudzula chisokonezocho: 11:22

2. Mgonero wa Ambuye: 11:23-28

a. Chivumbulutso pa mgonero wa Ambuye: 11:23

b. Dongosolo pa mgonero wa Ambuye: 11:23-25

c. Tanthauzo la mgonero wa Ambuye: 11:26



- d. Kudya mgonero mosayenera: 11:27
  - e. Kudya mgonero moyenera: 11:28
3. Zotsatira za kudya mosayenera: 11:27-34
- C. Vuto lokhuza mphatso za Mzimu mu mpingo: 12:1-14:40
- 1. Kupatsidwa kwa mphatso: 12:1-31
    - a. Kuyesa Mzimu: 12:1-3
      - (1) Chikhumbo chawo kuti azidziwe: 12:1
      - (2) Kuwakumbutsa za mmene analili kale: 12:2
      - (3) Mayeso kwa amene alankhula mwa Mzimu: 12:3
    - b. Kuchuluka kwa mphatso: 12:4-11
      - (1) Zochokera kwa mmodzi yemweyo: 12:4-6
      - (2) Cholinga cha mphatso: 12:7
      - (3) Mphatso: 12:8-10
      - (4) Kumene mphatso zonse zimachokera: 12:11
    - c. Chikhalidwe cha Thupi la Khristu: 12:12-31
      - (1) Umodzi wa Thupi: 12:12
      - (2) Khomo lolowera Mthupi: 12:13
      - (3) Chiyanjano Mthupi: 12:14-26
      - (4) Kuzindikira Thupi: 12:27
      - (5) Kusiyana kwa ntchito ya ziwalo: 12:28-31
  - 2. Kugwiritsa ntchito mphatso: 13:1-13
    - a. Kufunika kwa chikondi potumikira mphatso: 13:1-3
      - (1) Kufunika kwa chikondi ndi mphatso ya malilime: 13:1

(2) Chikondi ndi mphatso za pamwamba: 13:2

(3) Chikondi ndi kupereka: 13:3

b. Makhalidwe a chikondi: 13:4-7

(1) Makhalidwe oipa a chikondi: 13:4-6

(2) Makhalidwe abwino a chikondi: 13:6-7

c. Kupambana kwa chikondi: 13:8-13

(1) Kufananitsa kwa chikondi ndi zinthu zopita: 13:8-12

(2) Kupambana kwa chikondi pa zinthu za muyaya: 13:13

3. Magwiritsidwe ntchito abwino a mphatso za Mzimu: 14:1-40

a. Kufananitsa kufunikira kwa kulankhula malilime ndi uneneri: 14:1-25

(1) Kufananitsa kufunikira kwawo mu mpingo: 14:1-19

(2) Kufananitsa kufunikira kwawo kwa osakhulupirira: 14:20-25

b. Kugwiritsa ntchito bwino malilime ndi uneneri: 14:26-36

(1) Dongosolo polambira: 14:26

(2) Malangizo okhuzana utumiki wolambira: 14:27-36

c. Mawu otsiriza: 14:37-40

VII. Chiukitso: 15:1-58

A. Uthenga wabwino wa chiukitso cha Khristu: 15:1-11

1. Kulalikira ndi kulandira Uthenga Wabwini: 15:1-2

2. Chikhalidwe cha Uthenga Wabwino: 15:3-4

3. Maumboni a chiukitso cha Khristu: 15:5-10

4. Chidule cha zolankhula: 15:11

- B. Kufunika kwa chiukitso cha Khristu: 15:12-34
  - 1. Kufunika kwa chiukitso chake pa chipulumutso: 15:12-19
    - a. Kukana kwa chiukitso kwa anthu ena: 15:12
    - b. Zotsatira za kukana kwawo: 15:13-19
  - 2. Kufunika kwa chiukitso mu mbiri: 15:20-28
    - a. Kufunika mu mbiri: 15:20
    - b. Dalitso la umulungu: 15:21-22
    - c. Dongosolo la umulungu mu zochitika: 15:23-28
      - (1) Chiukitso cha Khristu ngati zipatso zoyamba: 15:23
      - (2) Chiukitso cha amene ali mwa Khristu pa kubwera kwake: 15:23
      - (3) Chimaliziro cha dongosolo la Mulungu: 15:24-28
  - 3. Kufunika kwa chiukitso cha Khristu mmakhalidwe a okhulupirira: 15:29-34
    - a. Funso lokhuza ubatizo wa wa akufa: 15:29
    - b. Funso loopseza moyo wathu: 15:30-34
      - (1) Kupusa kwa makhalidwewo: 15:30-32
      - (2) Chidzudzulo: 15:33-34
  - 4. Tsogolo la chiukitso cha akhristu: 15:35-58
    - a. Chikhalidwe cha thupi loukitsidwa: 15:35-49
      - (1) Funso lokhuza thupi loukitsidwa: 15:35
      - (2) Mayankho okhuza matupi owukitsidwa: 15:36-49
    - b. Kusintha kumene kumabweretsa thupi loukitsidwa: 15:50-58
      - (1) Nyengo yofuna kusinthaku: 15:50
      - (2) Chikhalidwe cha kusinthaku: 15:51-52
      - (3) Zoyenereza pa kusinthaku: 15:53
      - (4) Chigonjetso pa kusinthaku: 15:54-57
      - (5) Pempho lomaliza la kukhazikika: 15:58

VIII. Zochitachita ndi za munthu: 16:1-24

A. Malangizo a zopereka: 16:1-4

1. Malangizo oti aperekedwenso ku mpingo wa ku Agalatiya: 16:1
2. Njira zomwe atsate pochita zopereka: 16:2
3. Kutumiza chopereka: 16:3-4

B. Ulendo wopita kwa Akorinto: 16:5-12

1. Ulendo wa Paulo: 16:5-9
2. Ulendo wa Timoteo: 16:10-11
3. Ulendo apolo: 16:12

C. Chilimbikitso chomaliza kwa Akorinto: 16:13-14

D. Kuzindikira mthumwi zochokera kwa Akorinto: 16:15-18

1. Pempho la nyumba ya Stefana: 16:15-16
2. Mawu okhuzana ndi kubwera kwa mthumwi zitaut: 16:17-18

E. Moni otsiriza: 16:19-24

1. Moni ochokera kwa anthu ena: 16:19-20
2. Mawu omaliza ochokera kwa Paulo: 16:21-24
  - a. Kusainira ndi dzanja lake: 16:21
  - b. Chenjezo lomaliza: 16:22
  - c. Nyimbo: 16:23
  - d. Kuonetsera chikondi: 16:24

**II AKORINTO**  
**MAWU OYAMBA**

**WOLEMBA:** Paulo

**KULEMBERA KWA:** Okhulupirira a kwa Akorinto

**CHOLINGA:** Kukhazikitsanzo ulamuliro wake ngati mtumwi, ndi zinthu zina zofunika.  
(Onani 8:10.)

**VESI LOTSOGOLERA:** II Akorinto 12:9

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Chifooka cha munthu chimaonetsera mphamvu ya Mulungu.

**ANTHU OPEZEKA:** Paulo, Tiomteo, Tito

**MAGAWO**

I. Mawu oyamba: 1:1-11

A. Kupereka moni: 1:1-2

1. Kuchokera: Paulo ndi Timoteo: 1:1
2. Kupita ku: Mpingo wa Mulungu kwa Akorinto ndi oyera mtima a ku m' Akaya: 1:1
3. Chisomo ndi mtendere kuchokera kwa Mulungu ndi Yesu: 1:2

B. Mazunzo: 1:3-11

1. Matamando kwa Mulungu chifukwa cha mazunzo: 1:3

- a. Atate wa Ambuye Yesu Khristu.
- b. Atate wa zifundo.
- c. Mulungu wa chitonthozo chonse.

2. Kufunika kwa mazunzo: 1:4-7

- a. Kuthekera kotonthoza ena ndi chitonthozo chimene tinatonthozedwa nacho: 1:4
- b. Chitonthozo cha munthu mwa Khristu: 1:5
- c. Chitonthozo ndi chipulumutso cha ena: 1:6-7

3. Chitasanzo cha chizunzo: Paulo ku m'Asiya: 1:8-11

**Gawo Loyamba:**

## Chilimbikitso chokhuza Utumiki

1:12-7:16

### I. Makhalidwe a Paulo: 1:12-14

#### A. Umboni wake: 1:12

1. Kudzichepetsa.
2. Kuona mtima kwa umulungu.
3. Osati ndi mzeru za dziko.
4. Mwa chisomo cha Mulungu.

#### B. Makalata ake: 1:13

#### C. Ubale wake: 1:14

#### D. Malingaliro ake: 1:15-2:4

1. Malingaliro oyamba: 1:15-16
2. Kusintha kwa malingaliro: 1:17-22
3. Chifukwa chosinthira: 1:22-2:4

#### E. Malangizo kwa wolakwa koma wolapa: 2:5-11

1. Cholakwacho: 2:5
2. Ntchito zomwe akufunika malangizo: 2:6-8
3. Cholinga chimene amachitira zimenezo: 2:9-11

### II. Chikhalidwe cha utumiki: 2:12-6:10

#### A. Chigonjetso cha utumiki: 2:12-17

1. Nkhawaku Trowa: 2:12-13
2. Triumph in Christ: 2:14-17

#### B. Ulamuliri pa utumiki: 3:1-3

1. Mafunso a ulamuliro wawo: 3:1
2. Madziko a ulamuliro: 3:2-3

#### C. Ulemerero wa utumiki: 3:4-18

1. Ukupatsidwa mphamvu ndi Mulungu: 3:4-6
2. Ndi utumiki wa ulemerero: 3:7-11
3. Ndi utumiki wosavuta: 3:12
4. Ndi utumiki wa poyera, ndi wovumbulutsidwa: 3:13-16
5. Ndi utumiki wa ufulu: 3:17
6. Ndi utumiki umene umasintha moyo mkukhala wofananan ndi Ambuye: 3:18

D. Kupirira kwa utumiki: 4:1-5:10

1. Kupirira ngakhale pali khungu la Uthenga Wabwino: 4:1-7
  - a. Kuona mtima kwa utumiki: 4:1-2
  - b. Khungu la uzimu la otayika: 4:3-4
  - c. Chiletso cha Satana ku utumiki: 4:4
  - d. Kuwala kwa Uthenga kulowa mu mdima: 4:5-6
  - e. Chuma cha utumiki chili mu zotengera za dziko: 4:7
2. Kupirira mmazunzo: 4:7-15
  - a. Mmene mazunzowo analili: 4:8-9
  - b. Cholinga cha mazunzo: 4:10-12
  - c. Chigonjetso mmazunzo: 4:13-15
3. Chipiriro chilimbikitsidwa ndi chiyembekezo: 4:16-5:10
  - a. Chiyembekezo mmoyo uno: 4:16-18
  - b. Chiyembekezo mmoyo uli mkudza: 5:1-10
4. Maganizo athu chifukwa cha chiyembekezochi: 5:6-8
  - a. Kulimbika: 5:6
  - b. Chikhulupiriro: 5:7
  - c. Kupanda mantha a imfa: 5:8
  - d. Kukhala kovomerezeka: 5:9
5. Chimaliziro chake cha chiyembekezochi: 5:10

E. Chilimbikitso cha utumiki: 5:11-17

1. Cholinga chokhala ndi mantha a pa Mulungu: 5:11
2. Cholinga chokhalandi chidwi ndi anthu ena: 5:12-13
3. Cholinga chc chikondi cha Khristu: 5:14-15
4. Cholinga cha Moyo watsopano mwa Khristu: 5:16-17

F. Uthenga wa utumiki: 5:18-21

1. Mbali yawo ya atumiki mu utumiki: Kuyanjanitsidwa 5:18
2. Utumiki wawo wa atumiki: Chiyanjanitso: 5:18-19
3. Pempho kwa atumiki: Chiyanjanitso: 5:20
4. Maziko ake a uthenga: 5:21

III. Chidule cha utumiki: 6:1-10

A. Mbali yawo ya atumiki: Ogwira ntchito limodzi ndi Mulungu: 6:1

B. Pempho la atumiki: 6:1-2

C. Makhalidwe a atumiki: 6:3-10

1. Olakwikwa: Asapereke chokhumudwitsa mu china chilichonse: 6:3
2. Abwino: Azitsimikizire mwa iwo okha ngati atumiki a Mulungu mu zonse: 6:4-10
  - a. Mchipiriro: 6:4

- b. Mmasautso: 6:4
- c. Muzosowa: 6:4
- d. mzipinjo: 6:4
- e. Mmikwingwirima: 6:5
- f. Mndende: 6:5
- g. Mmapokoso: 6:5
- h. Mmautuito: 6:5
- i. Mmadikiro: 6:5
- j. Mmasalo a chakudya: 6:5
- k. Mmayeretsedwe: 6:6
- l. Mchidziwitso: 6:6
- m. Mchilekerero: 6:6
- n. Mkukoma mtima: 6:6
- o. Mwa Mzimu Woyera: 6:6
- p. Mchikondi chosanyenga: 6:6
- q. Mmawu a choonadi: 6:7
- r. Mu mphamvu ya Mulungu: 6:7
- s. Mwa zida za Mulungu: 6:7
- t. Mwa ulemerero ndi mwa mnyozo: 6:8
- u. Mu mbiri yoipa ndi mbiri yabwino: 6:8
- v. Osocheretsa koma ali owona: 6:8
- w. Osadziwika koma ali odziwika bwino: 6:9
- x. Akufa koma ali ndi moyo: 6:9
- y. Olangika koma osaphedwa: 6:9
- z. A chisoni koma okondwera: 6:10
- aa. A umphawi koma olemera: 6:10
- bb. Opanda kanthu koma okhala nazo zinthu zonse: 6:10

#### IV. Awadandauliranso za utumiki: 6:11-7:4

- A. Kudandaula ngati tate: 6:11-13
- B. Dandaulo pa kusiyana: 6:14-7:1
  - 1. Lamulo pa kusiyana: 6:14
  - 2. Mitsutsano pa kusiyana: 6:14-16
  - 3. Zotsatira pa kusiyana: 6:17-6:18
    - a. Kuchoka pakati pawo: 6:17
    - b. Kulandiridwa: 6:17
    - c. Ubale: 6:18
- C. Dandaulo la chiyero: 7:1
- D. Dandaulo pa umodzi: 7:2-4



V. Kuzindikira utumiki: 7:5-16

- A. Masautso ku Makedoniya: 7:5
- B. Kubwera kwa Tito: 7:6-7
  - 1. Chithonθοzo cha Tito: 7:6
  - 2. Uthenga wake: 7:7
- C. Kalata yoyamba ya Paulo: 7:8-12
  - 1. Kalata: 7:8
  - 2. Zotsatira za kalata: 7:8-11
    - a. Chisoni cha umulungu: 7:8-9
    - b. Kulapa: 7:9-10
    - c. Chipulumutso: 7:10
    - d. Kusamalitsa: 7:11
    - e. Kuzikonza tokha: 7:11
    - f. Mkwiyο: 7:11
    - g. Mantha: 7:11
    - h. Khumbo: 7:11
    - i. Machawi: 7:11
    - j. Kubwenzera: 7:11
    - k. Kutsimikizika mu zonse: 7:11
  - 3. Cholinga cha kalata yoyamba: 7:12
- D. Chithonθοzo ku chimwemwe cha Tito: 7:13-15
- E. Kulimbika kwa okhulupirira a ku Akorinto: 7:16

**Gawo Lachiwiri:**  
**Pempho la chopereka**  
**8:1-9:15**

I. Chitsanzo: Kupereka kwa Amakedoniya: 8:1-6

- A. Kufokokozapo za chopereka chawo: 8:1
- B. Nyengo za chopereka chawo: 8:2
  - 1. Mayesero a akulu a msautso.
  - 2. Chimwemwe chochuluka.
  - 3. Umphawi waukulu.
  - 4. Chuma cha ufulu.
- C. Mtundu wa maparekedwe awo: 8:3-5
- D. Zotsatira za chopereka chawo: 8:6

- II. Chilimbikitso: Dandaulo pa zopereka za khristu: 8:7-15
  - A. Dandaulo: 8:7
  - B. Cholinga choperekera: 8:8-12
    - 1. Chikondi: 8:8
    - 2. Chitsanzo cha Yesu Khristu: 8:9
    - 3. Kufuna: 8:19-12
  - C. Mfundo za kupereka bwino: 8:13-15
  
- III. Uthenga wa kwa Akorinto: 8:16-9:5
  - A. Chitsimikizo cha mthumwi: 8:16-24
    - 1. Kubwera kwa Tito kwa Akorinto: 8:16-17
    - 2. Abale omwe anamutsata Tito ku Akorinto: 8:18-22
    - 3. Chiyamikiro kwa aminthenga: 8:23
    - 4. Pempho loti awalandira bwinobwino: 8:24
  - B. Kulongosola mmene angatumizire aminthenga: 9:1-5
    - 1. Nyengo za ku Akaya zokhuzana ndi zopereka: 9:1-2
    - 2. Zolinga zotumizira abale pa nkhani ya zopereka: 9:3-4
    - 3. Awatuma abale pa nkhani ya zopereka: 9:5
  
- IV. Madalitso akupereka mwa ufulu: 9:6-15
  - A. Maziko a mfundo za kaperekedwe: 9:6
  - B. Mzimu wabwino pa kaperekedwe: 9:7
  - C. Zotsatira za kupereka mwaufulu: 9:8-14
    - 1. Zisomo zonse za kwa Mulungu: 9:8
    - 2. Okwanira mu zonse: 9:8
    - 3. Ochulukidwa mu ntchito zabwino: 9:8
    - 4. Madalitso kwa osauka: 9:9
    - 5. Madalitso a zinthu: 9:10
    - 6. Madalitso a kuuzimu: 9:10
    - 7. Kuchuluka mu zipatso za chilungamo: 9:10
    - 8. Kuchukitsidwa mu zonse: 9:11
  - D. Zimene anachita atangolandira mphatso: 9:11-14
    - 1. Mayamiko kwa Mulungu: 9:11-13
    - 2. Zokhuza iwo opereka: 9:14
  - E. Maziko a madalitso pa kupereka: 9:15
  
- V. Kulungama: Paulo atchinjiriza utumiki wake: 10:1-13:10

- A. Mphamvu: Ulamuliro wa mtumwi: 10:1-18
  - 1. Dandaulo lake ku mpingo: 10:1-6
    - a. Maziko a dandaulo lakelo: 10:1
    - b. Zimene amadandaula: 10:2
    - c. Kulongosola za nkondo yake mmene inalili: 10:3-6
      - (1) Chikhalidwe cha uzimu cha nkondo yake: 10:3
      - (2) Zida za uzimu za nkondo yake: 10:4
      - (3) Nkhondo pakati pa nkondo: 10:5-6
- B. Yankho kwa chiwalo chosocheretsedwa: 10:7-11
  - 1. Dandaulo lopenyerera zolondola: 10:7
  - 2. Chitsimikizo cha ulamuliro wake: 10:8-9
  - 3. Chitsutso: 10:10
  - 4. Chenjezo kwa "wotereyo": 10:11
- C. Za aphunzitsi onyenga: 10:12-18
  - 1. Kudzitukumula kwa aphunzitsi onyenga: 10:12
  - 2. Kudzitukumula koyenera: 10:13-18
    - a. Muyeso woyenera: 10:13
    - b. Zoyenera kuti ziyesedwe: 10:14-18

VI. Utumwi: Kudzitama ka Paulo: 11:1-12:13

- A. Pempho lake loti akhoza kudzitandira: 11:1-4
  - 1. Mawu okhuza pempho: 11:1
- 2. Zifukwa zoperekera pempho: 11:2-4
  - a. Kukhudzidwa kwake kwa iwo: 11:2
  - b. Nkhawa yake kwa iwo: 11:3-4
- B. Kukana kudzionera pansi kwa munthu: 11:5-15
  - 1. Mbali yake: 11:5
  - 2. Ulaliki wake: 11:6
  - 3. Utumiki wake: 11:7-15
- C. Zifukwa za Paulo zodzitamandira: 11:16-12:10
  - 1. Kukonzekera kudzitamandira: 11:16-21
    - a. Kusafuna kudzitamandira: 11:16-17
    - b. Kufunika kodzitamandira: 11:18
    - c. Chithonhozo mkudzitamandira: 11:19-21
  - 2. Kudzitamandira koyamba: 11:22-33
    - a. Kudzitamandira kwa thupi: 11:22
    - b. Kudzitamandira kokhuza utumiki: 11:23-29
    - c. Kudzitamandira muzipsinjo: 11:30-33
  - 3. Kudzitamandira kwachiwiri: 12:1-10

- a. Maganizo ake pa kudzitamandira: 12:1
  - b. Kudzitamandira pa masomphenya: 12:2-5
  - c. Kudzitamandira mchifooko: 12:6-10
  - D. Kuonanso kudzitamandira: 12:11-13
    - 1. Maganizo ake pa kudzitamandira: 12:11
    - 2. Choyambitsa kudzitamandira: 12:11-13
      - a. Kulephera kwawo kumuyamikira: 12:11
      - b. Kuyenera kwawo kumuyamamikira: 12:11-13
- VII. Aganiza zoyendera kwa Akorinto: 12:14-13:10

- A. Utumiki wake kwa iwo: 12:14-18
  - 1. Utumiki wake waulere pakufika kwake: 12:14
  - 2. Zifukwa za malingaliro ake: 12:14
  - 3. Chidwi chake chokhala nawo: 12:15
  - 4. Kutsutsa zabodza zokhudza iye: 12:16-18
- B. Chidwi chake mu nyengo zawo pakufika kwake: 12:19-21
  - 1. Kukonza malingaliro olakwika: 12:19
  - 2. Chidwi chake pa iwo: 12:20-21
- C. Malingaliro ake pakufika kwake: 13:1-4
  - 1. Kafukufuku wake adzapanga: 13:1-2
  - 2. Chitsimikizo choti adzaperekedwa kwa iwo: 13:3-4
- D. Dandaulo lomaliza kwa okhulupirira a ku Akorinto: 13:5-10
  - 1. Dandaulo loti aziyetse okha: 13:5-10
  - 2. Pemphero la kwa iwo: 13:7-9
  - 3. Cholinga cha kalata yake kwa iwo: 13:10

**Mawu otsiliza**  
**13:11-14**

- I. Chilimbikitso: 13:11
  - A. Lamulo: 13:11
    - 1. Khalani angwiro.
    - 2. Khalani otonthozeka.
    - 3. Khalani a mtima umodzi.
    - 4. Khalani mwa mtendere.
  - B. Zotsatira: 13:11
- II. Moni wotsiriza: 13:12-13

III. Nyimbo: 13:14

- A. Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu.
- B. Chikondi cha Mulungu.
- C. Chiyanjano mwa Mzimu Woyera.

## MAFUNSO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la I ndi II Akorinto ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene analemba buku la I Akorinto.

---

3. Kodi buku la I Akorinto analemba ndani?

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la I Akorinto.

---

5. Lembani Vesi lotsogolera la buku la I Akorinto kuchokera pamtima.

---

6. State the purpose for the book of II Corinthians.

---

7. Kodi buku la II Akorinto analemba ndani?

---

8. Tchulani Moyo ndo Mfundo ya Utumiki ya buku la II Akorinto.

---

9. Lembani Vesi lotsogolera la buku la II Akorinto kuchokera pamtima.

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani I Akorinto 3:10-15 kuti mudziwe izi:

- Nyumba
- Mwini
- Womanga
- Zomangira nyumnba
- Mayeso a nyumba

2. Chomodzi mwa zifukwa zimene Paulo analemba kalata ya I Akorinto chinali kulangiza mpingo kuti uchotse munthu wochimwa wokana kulapa (I Akorinto 5:1-8). Koma mu II Akorinto Paulo akulangiza mpingo kuti umulandire munthu amene walapa (II Akorinto 2:6-11).
3. Buku la II Akorinto amawulula zambiri za munthu ndi ntchito za Satana. Onani 2:10-11; 4:4; 11:3, 13-15; 12:7.
4. Pali mayina anayi a Okhulupirira omwe akupezeka mu II Akorinto koma mayinawa sapezeka mu Baibulo. Mayinawa ndi awa: Makalata a moyo 3:2-3; Fungo lokoma la Khristu: 2:15; Chuma za muzotengera za dziko: 4:7; Akazembe a Khristu: 5:20
5. Chimodzi mwa zifukwa zofunikira kwambiri zimene Mulungu amalolera kuti okhulupirira avutike zikupezeka mu II Akorinto 1:1-6.
6. Paulo anawauza okhulupirira a ku mpingo wa ku Akorinto kuti, “Tsanzani ine monga ndinatsanza Khristu” (I Akorinto 4:16 and 11:1). Phunzirani zitsanzo za Paulo monga zikupezeka mu I Akorinto:
  - Womvera mu uthenga, mu zochikita ndi mu zolinga: 2:1-5
  - Mamangidwe abwino: 3:10-23
  - Wodalilika ndi choonadi cha Uthenga: 4:1-6
  - Wopilira mmasautso a Yesu: 4:9-16
  - Woganizira mbale amene ndi wofooka: 6:12; 8:13
  - Wochepetsa mphamvu zake: 9:12-18
  - Wodzikana yekha kuti afikire miyoyo: 9:19-23
  - Wamwambo: 9:27; 10:33
  - Wodziletsa mmisonkhano yaikulu: 14:18-20
  - Wodzichepetsa: 15:9-10
7. I Akorinto 15 ndi ndime yaitali Mbaibulo imene ikamba za chiukitso cha mtsogolo cha okhulupirira. Werengani kusintha kumenee kudzachitike:
  - Thupi lafetsedwa mu chivundi, lafa mkuikidwa, mkuukitsidwa mchosavunda
  - Lafetsedwa lopanda ulemerero, liukitsidwa la ulemerero
  - Lafetsedwa lofooka, liukitsidwa la mphamvu
  - Lafetsedwa mu thupi lachibadwidwe, liukitsidwa mu thupi la uzimu
  - Lafetsedwa mu thupi la mwazi, liukitsidwa mu thupi losinthika

-Lafetsedwa mu thupi lakufa, liukitsidwa mu thupi losafa.

8. Werengani II Akorinto 7:10. Lembani mndandanda wa zinthu zosiyana pakati pa chisoni cha umulungu ndi chisoni cha dziko lapansi.
9. Werengani II Akorinto 6:8-11. Lembani mndandanda wa zimene zikusiyana pandimeyi.
10. Werengani chiyambi cha mbiri ya mpingo ku Akorinto: Machitidwe 18:1-18; 19:1-22; 20:3,31
11. Kodi Mulungu akulembabe “makalata?” Werengani II Akorinto 3:3. Wokhulupirira ndi kalata wamoyo amene Mulungu amavumbulutsirapo uthenga wake ku dziko lapansi.
12. I Akorinto 12-14 amakamba za magwiritsidwe a mphatso za mzimu mu mpingo. Gwiritsani ntchito zolembedwazi kuti muphunzire gawoli:

### **ZOKHUZANA NDI MPHATSO ZA MZIMU**

Mzimu Woyera amapereka kapena kugawa mphatsozi kwa okhulupirira monga mmene afunira: I Akorinto 12

- Pali mphatso zambiri, koma Mzimu mmodzi: 4-11
- Pali ziwalo zambiri, koma thupi limodzi 12-27
- Pali mautumiki ambiri, koma mpingo umodzi: 28-31

Popanda chikondi, mphatsozi ndizopanda tanthauzo: I Akorinto 13

- Mphatso za mzimu sizingagwire ntchito popanda chikondi: 1-3
- Kuposa kwa chikondi: 4-8
- Chikondi ndi Mphatso yoposa: 9-13

Mphatso yotsiririka kwambiri ndi mphatso ya uneneri: I Akorinto 14

- Imalimbikitsa mpingo: 1-22
- Imatumikira osapulumsidwa: 23-28
- Ikuyenera igwiritsidwe ntchito moyenera: 29-40



## CHAPUTALA CHA 8

### AGALATIYA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa mutu umenewu muyenera:

- Kutchula wolembe buku la Agalatiya.
- Kuzindikira amene wolembe buku la Agalatiya amawalemba.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Agalatiya.
- Kulemba Vesi lotsogolera la buku la Agalatiya kuchokera pantima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Agalatiya.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**OMWE AMALEMBERA:** Okhulupirira a ku Agalatiya

**CHOLINGA:** Kukonza chiphunzitso cholakwikwa cha kusunga malamulo a Chiyuda

**VESI LOTSOGOLERA:** Agalatiya 5:1

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Yesu anatimasula ife ku lamulo mkukhala mfulu.

**ANTHU OPEZEKA:** Paulo, Petulo, Yakobo, Kefa, Yohane, Banaba, Tito, Abrahamu.

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-5

A. Kuchokera kwa: Paulo: 1:1

1. Mtumwi.
2. Osati wa anthu.
3. Wa Yesu Khristu ndi Mulungu Atate.

B. Ku: Mipingo yak u Agalatiya: 1:2

C. Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Yesu: 1:3-5

1. Amene anazipereka yekha chifukwa cha machimo athu: 1:4
2. Amene anatimasula ife ku zoipa za dziko lapansi: 1:4
3. Molingana ndi chifuniro cha Atate: 1:4
4. Kwa Iye kukhale ulemerero wa nthawi zonse: 1:5

## II. Chidzudzulo: 1:6-10

- A. Kudabwa pa kupatuka kwawo ku Uthenga: 1:6
- B. Mawu okhuza kupatuka ku “uthenga wina” umene ndi wonama: 1:6-7
- C. Zoonza zake zenzeni: Kaya uthengawo unalalikidwa ndi ndani koma ndi otembereredwa: 1:8-9
- D. Malingaliro a Paulo pa nkhani imeneyo: 1:10

### **Gawo Loyamba: Ufulu wa mu Uthenga Chitsutso 1:11-2:21**

#### I. Mmene Paulo analandilira Uthenga: 1:11-24

- A. Chiyambi kudzera mu vumbulutso: 1:11-12
- B. Makhaliidwe ake oyamba a kulandira Uthenga: 1:13-14
  1. Amaphunzitsa chipembedzo cha chiyuda: 1:13
  2. Anazunza mpingo wa Mulungu: 1:13
  3. Anapambana mu chipembedzo cha Chiyuda kuposa a usinkhu wake: 1:14
  4. Anali wachangu pa miyambo ya Chiyuda: 1:14
- C. Mnene analandirira chivumbulutso: 1:15-17
  1. Gwero la chivumbulutso: God: 1:15
  2. Mutu wa chivumbulutso: His Son: 1:16
  3. Cholinga cha vumbulutso: Kuti Paulo akalalikire anthu amitundu: 1:16
  4. Yankho ku chivumbulutso: 1:16-17
    - a. Sanafunsane ndi thupi kapena mwazi: 1:16
    - b. Sanapite kea atumwi ku Yerusalemu: 1:17
    - c. Anapita ku Arabiya ndi ku Damasiko: 1:17
- D. Kuima pa yekha kwa Paulo osadalira atumwi a ku Yerusalemu: 1:18-20
  1. Kupita kwake koyamba ku Yerusalemu: 1:18-20
    - a. Nthawi imene amapita: 1:18
    - b. Cholinga cha ulendo wake: 1:18
    - c. Kutalika kwaulendo wake: 1:18
    - d. Omwe adakumana nawo pa ulendo wake: 1:19-20
- E. Kusapezeka kwa Paulo ku Yerusalemu: 1:21-24
  1. Malo amene adachoka: 1:21

2. Kusadziwika kwake ndi mpingo wa ku Yudeya: 1:22
3. Mmene mpingo unachitira pa kunenepo za iye: 1:23-24

II. Mmene atumwi a ku Yerusalemu anakhutira ndi Uthenga wa Paulo: 2:1-10

- A. Mmene anauonetsera kwa iwo: 2:1-2
  1. Ulendo wake wa ku Yerusalemu: 2:2
  2. Kulankhula kwa Paulo ku Yerusalemu: 2:2
- B. Zotsatira za Uthenga wa Paulo ku Yerusalemu: 2:3-10
  1. Mbali yake monga ikuonetseledwa mu Tito: 2:3
  2. Kusemphana kwake ndi abale onyenga: 2:4-5
    - a. Kupezeka kwawo: 2:4
    - b. Paulo akana kugonjera zofuna zawo: 2:5
  3. Atsogoleri a ku Yerusalemu avomereza Uthenga wa Paulo: 2:6-10
    - a. Kulephera kwawo kuonjezerapo ku Uthenga wake: 2:6
    - b. Kuvomerezedwa kwa Uthenga wake ndi iwo: 2:7-10
    - c. Maziko a chivomerezo chawo: 2:7-9
    - d. Kuonetsera kuvomereza kwawo: 2:9
    - e. Pempho lawo limodzi mkuvomereza kwawo: 2:10

III. Paulo adzudzula Petulo pa kugonjera kwake ku chilamuloku Antiiokeya: 2:11-21

- A. Chifukwa chimene amamdzudzulira: 2:12
- B. Zotsatira za kusakhazikika kwa Petulo muzochitika: 2:13
- C. Chilungamitso pa chidzudzulocho: 2:14-21
  1. Paulo afunsa Petulo: 2:14
  2. Paulo alongosola mbali ya chiphunzitso chake: 2:15-21
    - a. Kuperewera kwa lamulo: 2:15-18
      - (1) Talungamitsidwa ndi chikhulupiriro, osati ndi lamulo kapena ntchito: 2:16
      - (2) Tikadalira lamulo, ndiye kuti tikhala ochimwa: 2:17-18
    - b. Moyo watsopano mwa Khristu: 2:19-21
      - (1) Zotsatira za lamulo ku moyo watsopano: 2:19
      - (2) Chikhalidwe cha moyo watsopano: 2:20
      - (3) Chisomo cha Mulungu chikhala chopanda pake ngati tisunga lamulo: 2:21

**Gawo Lachiwiri: Ufulu wa Uthenga  
Mtsutso wa Chiphunzitso 3:1-4:31**

I. Chiphunzitso cha kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro: 3:1-4:7

- A. Chilungamitso mwa chikhulupiriro: 3:1-14
  - 1. Kusakhazikika kwa makhalidwe awo: 3:1-5
    - a. Kupatuka kwa Yesu: 3:1
    - b. Funso la chiyambi cha moyo wawo wa Chikhristu: 3:2
    - c. Funso la njira yawo yokhalira angwiro: 3:3
    - d. Funso la masautso awo ngati okhulupirira: 3:4
    - e. Funso la maziko a ntchito ya Mulungu mwa iwo: 3:5
- B. Chitsanzo cha kulungamitsaidwa kwa Abrahamu: 3:6-9
  - 1. Mmene analungamitsidwira Abrahamu: 3:6
  - 2. Chizindikiro cha ana a Abrahamu: 3:7
  - 3. Mulungu alengeza kwa Abrahamu kuti ndi wolungama mwa chikhulupiriro: 3:8
  - 4. Olandira cholowa cha madalitso a Abrahamu: 3:9
- C. Kumasulidwa ku chilamulo ndi ntchito mwa Yesu Khristu: 3:10-14
  - 1. Temberero kwa iwo akusunga lamulo ndi ntchito: 3:10
  - 2. Kulephera kwa lamulo ndi ntchito pa chilungamitso: 3:11-12
  - 3. Kumasulidwa ku temberero mwa Yesu: 3:13-14
    - a. Mamasulidwe ake a temberero: 3:13
    - b. Cholinga cha mamasulidwe ku temberero: 3:14
- D. Kulephera kwa lamulo ndi ubale wake ndi chikhulupiriro: 3:15-14:7
  - 1. Pangano la chikhulupiriro ndi Abrahamu: 3:15-18
    - a. Pangano linakhazikika: 3:15
    - b. Linali kwa Abrahamu ndi mbewu zake: 3:16
    - c. Lonjezo silinasinthidwe ndi lamulo: 3:17
    - d. Cholowa sichinadze mwa lamulo koma mwa lonjezo: 3:18
  - 2. Malo enieni ndi cholinga cha lamulo: 3:19-29
    - a. Chikhulidwe cha kanthawi cha lamulo: 3:19-20
    - b. Kulephera kwa lamulo kupreka moyo: 3:21-22
    - c. Lamulo linali chipangizo chotitengera kwa Khristu: 3:23-29
- E. Kusiyanana pakati pa lamulo ndi chikhulupiriro: 4:1-7
  - 1. Chitsanzo cha mbali ya wotenga cholowa ngati mwana: 4:1-2
  - 2. Magwiritsidwe ake a chitsanzochi kwa okhulupirira: 4:3-6
    - a. Ukapolo ngati ana: 4:3
    - b. Mfulu ngati ana: 4:4-6
  - 3. Mawu otsiriza kwa okhulupirira: 4:7

II. Awadandaulira okhulupirira a ku Agalatiya kuti asiye chilamulo: 4:8-31

- A. Kuvomereza chilamulo cha chiyuda ndiko kubwerera ku ukapolo: 4:8-11
  - 1. Nyengo zawo zakale za ukapolo: 4:8
  - 2. Kumasulidwa kwawo ku ukapolo: 4:9

3. Kusunga chilamulo ndi kubwerera ku ukapolo: 4:9-10
4. Ntchito zawo zimamusautsa Paulo: 4:11
- B. Dandaulo lake la ubale wake ndi iwo: 4:12-20
  1. Pempho lawo kuti adziwe mbali ya Paulo: 4:12
  2. Awkumbutsa za ubale wawo wakalendi iwo: 4:12-14
  3. Kusintha kwa ubale wawo kwa iye: 4:15-18
  4. Kumva zowawa kwake ndi iwo: 4:19-20
- C. Dandaulo pa mapangano awiri osiyana, lamulo ndi chisomo: 4:21-31
  1. Funso la iwo ofuna kukhala pansu pa lamulo: 4:21
  2. Nkhani ya ana awiri a Abrahamu: 4:22-23
  3. Tanthauzo la nkhani: 4:24-23
    - a. Njira ziwiri zikuimira mapangano awiri: 4:24
    - b. Kufotokozera za mapangano awiri: 4:24-28
      - (1) Mmodzi ayimira ukapolo: 4:24-25
      - (2) Winayo ayimira ufulu: 4:26-28
    - c. Kutulutsidwa kwa mwana wa ukapolo: 4:29-30
    - d. Mawu otsiriza a nkhani: 4:31

**Gawo Lachitatu: Ufulu wa Uthenga  
Zoyenera Kuchita 5:1-6:18**

- I. Pempho la kusunga ufulu wa Chikhristu: 5:1-12
  - A. Vuto la mdulidwe: 5:2-6
    1. Umangitsa Mkhristu kukhala wopanda tanthauzo kwa iwo: 5:2
    2. Umawakamiza kukhala omvera lamulo: 5:3
    3. Umawachotseratu kwa Khristu: 5:4
    4. Ndi kugwa kuchokera ku chisomo: 5:4
    5. Malingaliro olondola a Mkhristu: 5:5-6
  - B. Chweruzo cha aphunzitsi onyenga: 5:7-12
    1. Kulakwa kwawo: 5:7-8
    2. Chitsanzo cha chiphunzitso chawo: 5:9
    3. Chiweruza cha iye amene akuwazunza: 5:10-12
- II. Moyo wa ufulu wa Chikhristu: 5:13-6:10
  - A. Moyo wotsogozedwa ndi chikondi: 5:13-15
    1. Wokhulupirira ayitanidwa ku ufulu: 5:13
    2. Magwiritsidwe ntchito a ufulu wa Chikhristu: 5:13
    3. Kukwaniritsidwa kwa chilamulo kudzera mu chikondi: 5:14

4. Zotsatira za kusowa kwa chikondi: 5:15
- B. Ndiko kuyenda mwa Mzimu, osati mwa thupi: 5:16-25
  1. Lamulo loyenda mu Mzimu: 5:16
  2. Kulimbana pakati pa Mzimu ndi thupi: 5:17-18
  3. Kusiyana pakati pa zofuna za thupi ndi zofuna za Mzimu: 5:19-23
    - a. Ntchito za thupi: 5:19-21
    - b. Chipatso cha Mzimu: 5:22-23
  4. Anthu okhala mwa Mzimu: 5:24-25
    - a. Adapachika thupi lawo: 5:24
    - b. Amakhala mmoyo wa kuyenda mwa Mzimu: 5:25
- C. Ndi moyo wonyamulirana zothodwetsa: 5:26-6:10
  1. Kunyamula zofooka: 5:26-6:5
    - a. Chenjezo lokhuza kukhala ndi malingaliro oyipa ndi anthu ena: 5:26
    - b. Malingaliro odzichepetsa pofuna kubwenzeretsa wakugwa: 6:1
    - c. Kunyamulirana zolemetsa: 6:2
    - d. Malingaliro abwino kwa anthu ena: 6:3-5
- D. Ndi moyo wotsogozedwa ndi mfundo: 6:6-10
  1. Mfundo ya kulumikizana: 6:6
  2. Mfundo ya kholora la muuzimu: 6:7-8
  3. Mfundo ya kuchita bwino: 6:9-10

### III. Mawu otsiriza:

- A. Reference to his large letters: 6:11
- B. Rebuke of his adversaries: 6:12-13
- C. Kulimba mtima kwake mu mtanda: 6:14-16
  1. Ulemerero wa mtanda: 6:14
  2. Kupachikidwa kudzera mwa mtanda: 6:15
  3. Blessings on those accepting this principle: 6:16
  4. Ali ndi chizindikiro cha Ambuye mu thupi lake: 6:17

### IV. Nyimbo: 6:18

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Agalatiya ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chomwe amalemba buku la Agalatiya.

---

---

---

3. Kodi bukuli amalemba ndani?

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Agalatiya.

---

---

---

5. Lembani Besi lotsogolera la buku la Agalatiya kuchokera pamtima.

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Onani pa Habakuku 2:4. Ndimeyi ikupezeka ku Agalatiya 3:11.
2. Phunzirani kusiyana pakati pa chipatso cha Mzimu Woyera ndi ntchito za thupi: Agalatiya 5:19-23.
3. Mawu aakulu a m’buku la Agalatiya ndi ufulu. Mawuwa agwiritsidwa ntchito kokwana khumi ndi chimodzi (11). Pezani mavesi amene mawuwa akupezeka ndipo fotokozani mwachidule pa zimene zikuphunzitsidwa zokhuza ufulu.
4. Fananitsani moyo wa Paulo asanatembenuke mtima ndi pamene atatembenuka mtima: Agalatiya 1:13-17.
5. Chiphunzitso cholakwikwa ku mpingo wa Agalatiya chimadziwika kwa Paulo ngati “uthenga wina wapadera.” Okhulupirirawa amafuna kulungamitsidwa mwa chilamulo (5:4). Amayenera kumakumbukira masiku oyera (4:10) ndi mdulidwe ngati njira ya chipulumutso (5:2; 6:12-13). Amafunanso kuonjezera ntchito za Mzimu Woyera ngati mwa chilamulo ndi pakuchita chilungamo mwa iwo okha (3:3). Amalimbikitsa kusunga chilamulo cha Mose (4:21). Sikuti iwowa uthenga adaukana ayi, koma amaonjezera kusunga chilamulo ndi miyambo ina.
6. Werengani kusiyana kwa buku la Agalatiya pa nkhani ya izi: chikhulupiriro ndi ntchito, Mzimu ndi thupi, chisomo ndi lamulo, mdulidwe ndi moyo watsopano, mtanda ndi dziko, ufulu ndi ukapolo, cha chilengedwe (Isimayeli) ndi cha uzimu (Isaki).
7. Zinthu zomwe mukuyenera kuchita:
  - Kubala chipatso: Agalatiya 5:22-23
  - Kunyamula zolemetsa: Agalatiya 6:2
  - Kufetsa mbewu: Agalatiya 4:7,9
  - Kukhala ndi chizindikiro: Agalatiya 6:17 (zizindikiro cha Ambuye Yesu)



## CHAPUTALA 9

### AEFESO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula wolembe buku la Aefeso.
- Kuzindikira kumene wolembe amawalemba.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Aefeso.
- Kulemba vesi lotsogolora la buku la Aefeso kuchokera pantima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Aefeso.

#### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**KOMWE AMALEMBERA:** Ku mpingo wa ku Aefeso.

**CHOLINGA:** Kuwadziwitsa okhulupirira za chuma chawo chomwe chili mwa Khristu ndi kuwalangiza zokhuzana mayendedwe awo mwa Khristu.

**VESI LOTSOGOLERA:** Aefeso 1:3

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Wokhulupirira ali ndi cholowa cha madalitso (chuma) ndi udindo (mayendedwe) wa mayitanidwe awo mwa Khristu.

**ANTHU OPEZEKAMO:** Paulo, Tikiko

#### MAGAWO

#### GAWO LOYAMBA: CHUMA CHATHU

I. Mawu oyamba: 1:1-2

A. Kuchokera kwa Paulo: 1:1

B. Kupita kwa oyera mtima a ku Aefeso: 1:1

C. Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu ndi Yesu: 1:2

II. Mayamiko pa chuma cha uzimu: 1:3-14

- A. Watisankha ife: 1:4
- B. Adatisankhiratu: 1:5-6
- C. Tili ndi maomboledwe mwa Iye: 1:7
- D. Amatipatsa ife nzeru: 1:8
- E. Anaululu chinsisi cha chifuniro chake: 1:9-10
- F. Mwa Iye tili nacho cholowa: 1:11-12
- G. Tinasindikizidwa ndi Mzimu Woyera: 1:13-14

III. Mapemphero chifukwa cha maganizidwe athu a uzimu mwa Khristu: 1:15-23

- A. Maziko a pemphero: 1:15
- B. Chikhalidwe cha pemphero: 1:16
- C. Mulungu timalankhula naye mpemphero: 1:17
- D. Mphatso zomwe timapempha mpemphero: 1:17
  - 1. Nzeru.
  - 2. Vumbulutso la ku chidziwitso cha Iye.
- E. Cholinga cha pemphero: 1:18-23
  - 1. Kuti akazindikire chiyembekezo cha maitanidwe ake: 1:18
  - 2. Kuti akalandire chuma cha cholowa chake: 1:18
  - 3. Kuti akazindikire mphamvu yake: 1:19-23
    - a. Chikhalidwe cha mphamvu yake: 1:19
    - b. Chionetsero cha mphamvu yake mwa Khristu: 1:20-23

IV. Nyengo zathu mwa Khristu: 2:1-10

- A. Asanabwere Khristu: 2:1-3
  - 1. Imfa ya uzimu: 2:1
  - 2. Kueyenda molingana ndi makhalidwe a dziko lapansi: 2:2
  - 3. Omvera Satana: 2:2
  - 4. Mzimu osamvera: 2:2
  - 5. Malankhulidwe oyipa: 2:3
  - 6. Ana a mkwiyo: 2:3
  - 7. Okonda zilakolako za thupi: 2:3
    - a. Zokhuma za thupi: Makonda a dziko

- b. Zokhumba za maganizo: Zolinga za dziko
- B. Nyengo zathu zatsopano mwa Khristu: 2:4-10
  - 1. Kupatsidwa moyo: 2:5
  - 2. Kupulumutsidwa mwa chisomo: 2:5
  - 3. Kuukitsidwa kupita ku malo akumwamba: 2:6
  - 4. Wokonderedwa ndi Mulungu: 2:7
- C. Chifukwa chokhala ndi nyengo zatsopano: 2:8-10
  - 1. Chipulumutso chimene ndi: 2:8
    - a. Chachikhulupiro: 2:8
    - b. Mphatso ya Mulungu: 2:8
  - 2. Chipulumutso chimene sichichokera: 2:8-9
    - a. Kwa ife: 2:8
    - b. Ku ntchito zathu: 2:9
  - 3. Kupitilira kwa ntchito ya Khristu mmoyo wathu: 2:10

V. Chiyanjano chathu chakale: 2:11-12

"Amene kale munali..."

- A. Opanda Khristu: 2:12
- B. Alendo: 2:12
- C. Osadziwika: 2:12
- D. Opanda chiembekezo: 2:12
- E. Opanda Mulungu: 2:12

VI. Ubale watsopano: 2:19-22

"Komano tsopano muli..."

- A. Mbadwa ya dziko limodzi: 2:19
- B. A banja limodzi la Mulungu: 2:19
- C. Omangidwa pa madziko amodzi: 2:20
- D. Magawo a mamangidwe: 2:21
- E. Okhalamo Mzimu Woyera: 2:22

VII. Mmene kusintha kwachitikira: 2:13-18

"Koma tsopano muli mwa Khristu..."

- A. Utali watha: Tsopano muli chifupi: 2:13
- B. Khoma lakudula pakati latha: Onse akhala limodzi: 2:14
- C. Kugawika kwatha: Khoma lapakati laphwanyika: 2:14
- D. Kusamvana kwatha: Udani watha: 2:15

- E. Kusiyana kwathetsedwa: 2:15-18
  - 1. Munthu watsopano mmodzi: 2:15
  - 2. Oyanjanitsidwa kwa Mulungu: 2:16
  - 3. Mtendere ndi Mulungu: 2:17
  - 4. Okhala ndi mwayi kwa Mulungu: 2:18
  - 5. Palibenso alendo kapena akutali: 2:19-22
    - a. Mbadwa zokhazokha: 2:19
    - b. Omangidwa pa maziko oyenera: 2:20
    - c. Chimango choyenera cha Mzimu Woyera: 2:21
    - d. Kachisi woyera mwa Ambuye: 2:21
    - e. Malo okhalamo Mulungu mwa Mzimu: 2:22

VIII. Kuulula chinsisi ya Umulungu: 3:1-12

- A. Paulo ngati mnthenga wa chinsisi: 3:1-13
  - 1. Ubale wake ku chinsisicho: 3:1-5
    - a. Mbali yake ngati kapolo mmalo mwa Amitundu: 3:1
    - b. Udindo wake pa chisomo cha Mulungu kwa Amitundu: 3:2
    - c. Chidziwitso chake cha chinsisi mwa vumbulutso: 3:3-5
  - 2. Mawu a chinsisi: 3:6
  - 3. Utumiki wa Paulo molumikizana ndi chinsisi: 3:7-12
    - a. Gwero la utumiki wake: 3:7
    - b. Malingaliro a amene wapatsidwa utumiki: 3:8
    - c. Zimene zili mu utumiki: 3:8-9
    - d. Cholinga cha utumiki: 3:10-11
    - e. Madalitso a utumiki: 3:12
    - f. Mazunzo a utumiki: 3:13

IX. Kukhala ndi chinsisi cha Umulungu: 3:14-21

- A. Mawo oyamba ku pemphero la kukhala ndi chinsisi: 3:14-15
- B. Pemphro: 3:16-17
  - 1. Kuti alimbikitsidwe munthu wa mkati ndi Mzimu wamphamvu: 3:16
  - 2. Kuti akumane ndi kupezeka kwa Yesu: 3:17
  - 3. Kuti azikike ndi kukhazikika mu chikondi: 3:17
  - 4. Kuti akhale ndi chidziwitso cha Mzimu cha chikondi cha Yesu: 3:18-19
    - a. Malire ake: 3:18
    - b. Chikhalidwe cha Umulungu wake: 3:19
  - 5. Kuti akadzazidwe ndi chidzalo cha Umulungu: 3:19

- C. Mawu omaliza okhuza pemphero: 3:20-21
1. Kuthekera kwa Iye amene ndi mwini nkhani: 3:20
  2. Matamando a Iye amene ndi mwini nkhani: 3:21

**Gawo Lachiwiri: Mayendedwe athu mwa Khristu 4:1-6:24**

- I. Kuyenda limodzi kwa mpingo: Yendani moyenera: 4:1-16

A. Kuchokera mmalingaliro abwino: 4:2

1. Kudzichepetsa.
2. Kufatsa.
3. Chipiriro.
4. Kuthandizana wina ndi nzake mchikondi.

B. Kuchokera mu umodzi: 4:3-6

1. Mu mtendere: 4:3
2. Mu thupi limodzi: 4:4
3. Mu mzimu umodzi: 4:4
4. Mu chiyembekezo chimodzi cha mayitanidwe anu: 4:4
5. Mwa Ambuye mmodzi: 4:5
6. Mu chikhulupiriro chimodzi: 4:5
7. Mu ubatizo umodzi: 4:5
8. Mwa Mulungu mmodzi: 4:6
  - a. Atate wa onse.
  - b. Pamwamba za zonse.
  - c. Mwa onse.
  - d. Mwa inu nonse.

C. Pa kukhala akusanza ache a Khristu: 4:7-10

D. Mu ndondomeko yabwino: 4:11-13

1. Mphatso za Mzimu: 4:11
  - a. Atumwi.
  - b. Aneneri.
  - c. Alaliki.
  - d. Abusa.
  - e. Aphunzitsi.
2. Zolinga zawo: 4:12-16
  - a. Kulungamitsa oyera mtima: 4:12
  - b. Ntchito ya utumiki: 4:12
  - c. Kulimbikitsa thupi la Khristu: 4:12
  - d. Umodzi wa muchikhulupiriro: 4:13

- e. Chidziwitso cha Mwana wa Mulungu: 4:13
  - f. Ungwiro pambuyo pa Khristu: 4:14
  - g. Kukhwima mu uzimu: 4:14-15
- E. Pakukhala gawo limodzi la thupi: 4:16
- 1. Olumikizika limodzi.
  - 2. Gawo lilionse la thupi kugwira ntchito malo ake.
  - 3. Kuchuluka mwa chilimbikitso cha chikondi.

## II. Mayendedwe a panokha ngati wokhulupirira: 4:17-5:2

- A. Tisayende motani: 4:17-25
- 1. Mu chitsilu cha mtima: 4:17
  - 2. Ndi chidziwitso chodetsedwa: 4:18
  - 3. Kuchotedwa ku moyo wa Mulungu mwa chifukwa cha umbuli ndi khungu: 4:18
  - 4. Kudzipereka kukukhumba zonyasa, chidetso ndi umbombo: 4:19
- B. Tiyende bwanji: 4:20-5:2
- 1. Mwa Khristu: 4:20-21
  - 2. Kuvula munthu wakale: 4:22
  - 3. Kukunzeka mu uzimu kukhala watsopano: 4:23
  - 4. Kuvala munthu watsopano: 4:24
  - 5. Kutaya makhalidwe a uchimo: 4:25-30
    - a. Bodza: 4:25
    - b. Mkwiyo: 4:26-27; 31
    - c. Kuba: 4:28
    - d. Nkhani zovunda: 4:29
    - e. Kumvetsa chisoni Mzimu Woyera: 4:30
    - f. Chiwawa: 4:31
    - g. Mkwiyo: 4:31
    - h. Kupsa mtima: 4:31
    - i. Kulankhula zoipa: 4:31
    - j. Choipa chonse: 4:31
  - 6. Kukhala ndi makhalidwe okoma: 4:32-5:1
    - a. Okoma: 4:32
    - b. Mtima wachifundo: 4:32
    - c. Kukhululukira: 4:32
    - d. Ngati ana omvera: 5:1

## III. Makhalidwe athu mogwirizana ndi dziko: 5:2-21

- A. Yendani mu chokondi pa kutsanza Khristu: 5:2

- B. Yendani mchiyero: 5:3-5
    - 1. Opanda dama: 5:3
    - 2. Opanda chidetso: 5:3
    - 3. Opanda kusirira: 5:3
    - 4. Opanda chinyaso: 5:4
    - 5. Opanda zolankhula zopanda pake: 5:4
    - 6. Opanda zopusa: 5:4
    - 7. Opanda malingaliro oyamika: 5:4
  - C. Kuyenda ndi umuyaya wa mmaganizo: 5:5
  - D. Musanyengedwe ndi mawu opanda pake: 5:6
  - E. Osapanga mgwirizano oipa: 5:7
  - F. Yendani mkuunika: 5:8
  - G. Balani chipatso cha Mzimu: 5:9
    - 1. Ukoma.
    - 2. Chilungamo.
    - 3. Choonadi.
  - H. Chitani chimene ndi chovomerezeka kwa Ambuye: 5:10
  - I. Musayende mu mdima: 5:11-14
    - 1. Musayanjane ndi mdima: 5:11
    - 2. Tzutsani ntchito zosabala kanthu: 5:11
    - 3. Musalankhule zinthu zochitika mu mdima: 5:12
    - 4. Bweretsani kuwala mu mdima: 5:13
  - 5. Dzukani inu amene mukugona mu mdima mu uzimu: 5:14
  - J. Yendani ngati anzeru, osati opusa: 5:15
  - K. Ombolani nthawi: 5:16
  - L. Dziwani chifuniro cha Mulungu: 5:17
  - M. Musaledzere ndi vinyo: 5:18
  - N. Dzazidwani ndi Mzimu: 5:18
    - 1. Zilankhulireni nyimbo za masalmo, mayamiko ndi nyimbo za uzimu: 5:19
    - 2. Kuyimba nyimbo mmitima yanu: 5:19
    - 3. Kuyamika Mulungu mu zinthu zonse mwa Yesu Khristu: 5:20
- IV. Mayendedwe athu molingana ndi maubale ena: 5:21-6:9
- A. Okhulupirira ena: Gonjerani nokha mkuchitira mantha Mulungu: 5:21
  - B. Akazi: 5:22-24
    - 1. Gonjerani nokha kwa amuna anu ngati kwa Ambuye: 5:22
    - 2. Zindikirani amuna anu ngati mutu wa mkazi monganso Khristu ali mutu wa mpingo: 5:23
    - 3. Gonjerani kwa amuna anu mu zonse monganso mpingo kwa Khristu: 5:24
  - C. Amuna: 5:25-33

1. Kondani akazi anu monganso Khristu anaconda mpingo: 5:25-29
2. Lumikizikani kwa akazi anu monganso mpingo walumikzika kwa Khristu: 5:30-33
  - a. Thupi limodzi: 5:30
  - b. Kusiya onse: 5:31-32
- D. Kwa amuna ndi akazi: 5:33
  1. Amuna kondani akazi anu a inu nokha: 5:33
  2. Akazi inu mverani amuna anu: 5:33
- E. Ana: Lemekezani makolo anu: 6:1-3
- F. Atate inu: 6:4
  1. Musayambitse mkwiyo kwa ana anu.
  2. Alereni iwo mmaleredwe ndi mchisamaliro cha Ambuye.
- G. Akapolo inu: 6:5-8
  1. Khalani omvera kwa mbuye wanu: 6:5
  2. Khalani ndi mtima waulemu: 6:5
  3. Khalani omvera (a mtima umodzi): 6:5
  4. Atumikireni ngati kutumikra Khristu: 6:6-7
  5. Dziwani kuti mphoto yanu idzachokera kwa Ambuye: 6:8
- H. Ambuye inu: 6:9
  1. Chitirani akapolo anu chomwechonso: 6:9
  2. Podziwa kuti Ambuye wawo ndi wanu ali mmwamba: 6:9
  3. Ambuye alibe tsankhu: 6:9
- V. Mayendedwe athu molingana ndi mphamvu za Satana: 6:10-20
  - A. Khalani amphamvu mwa Ambuye ndi kulimbika mu mphamvu yake: 6:10
  - B. Valani zida zonse za Mulungu: 6:11-20
    1. Cholinga: Kuit mukaime ndi kutsutsana ndi machenjero a Satana: 6:11,13
    2. Mdani: 6:12
      - a. Maukulu.
      - b. Mphamvu.
      - c. Olamulira a mdima wa dziko lapansi.
      - d. Ndi mizimu yoipa ya mlengalenga.
    3. Zida: 6:14-20
      - a. Mutazimangirira choonadi mchiuno mwanu: 6:14
      - b. Cha pachifuwa cha chilungamo: 6:14
      - c. Mapazi anu mutaziveka uthenga wabwinowa mtendere: 6:15
      - d. Chikopa cha chikhulupiriro: 6:16
      - e. Chisoti cha chipulumutso: 6:16
      - f. Lupanga la Mzimu: 6:17



g. Pemphero: 6:18-20

VI. Mawu otsiriza: 6:21-24

A. Okhuza za munthu: 6:21-22

1. Kutuma Tukiko ngati mnthenga: 6:21
2. Cholinga chotumira Tukiko ku Atene: 6:21-22
  - a. Kuti adziwitse uthenga: 6:21-22
  - b. Akadziwitse za Paulo: 6:22
  - c. Kuti akawatonthoze: 6:22

B. Mawu otsiriza: 6:23-24

1. Chikhumbo cha pa abale: 6:23
  - a. Mtendere.
  - b. Chikondi.
  - c. Chikhulupiriro.
2. Madalitso kwa amene akonda Khristu: 6:24

## **MAYESO ODZIYESA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Aefeso ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la Aefeso.

---

---

---

3. Kodi buku la Aefeso amalemba kwa yani?

---

---

4. Tchuani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Aefeso.

---

---

---

5. Lembani Vesi lotsogolera la Aefeso kuchokera pantima.

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino).

**KUPITILIZA KUPHUNZIRA**

Buku la Aefesolimawafanizira okhulupirira ndi zinthu zambiri monga:

-Mbadwa: 2:19

-Thupi: 1:22-23; 4:4,12,16

-Mpingo: 5:22-23

-Akapolo: 6:6-9

-Chimango: 2:20-22

-Asirikali: 6:10-17

Ubale wathu ndi Mulungu uli ngati ubale wa m'banja (3:15). Tinalandilidwa ngati ana (1:5-6); nyumba (2:19); ndi ana okonedwa (5:1).

Werengani pemphero la Paulo kwa Aefeso. Anapemphera kuti azindikire zinthu zina (1:16-19) ndipo akhale ndi zinthu zina (3:14-19). Zonsezo ndi zofunika pa kuitanitsa cholowa chatu cha uzimu. Choncho tikuyeneranso kudziwa ndi kuitanitsa cholowa chatu. Werengani mfundo zotsogolera zopezeka mu Aefeso za mmene tingapempherere: 5:18-20; 6:18.

Pali ndime zambiri mu buku la Aefeso zokhuzana ndi mpingo. Lembani vesi lililonse ndi kulemba mwachidule chimene akuphunzitsa.

Werengani mawu akuluakulu: Zinsisi, mayendedwe, chikondi, ulemelero, mphamvu, mu kugwira ntchito, mtenedere, chuma, kukhalalimodzi, amodzi mzakumwamba.

Werengani Aefeso 4:22-23 ndi 6:11-18. Lembani mnadndanda wa zinthu zimene tikuyenera kuzivula ndi zimene tikuyenera kuzivala. Fanizirani mndandamda wa zinthu zimenezi ndi zomwe zikupezeka pa Akolose mutu 3.

Lembani mndandanda wa zinthu zomwe ndi zosiyana mu buku la Aefeso. Izi ndi zina mwa zitsanzo zongokuyambirani:

Chipulumutso cha ntchito: 2:9

Chipulumutso cha chisomo: 2:8

Chvumbulutso chobisika: 3:5

Chinsisi chiululuka: 3:3

Ana akusamvera: 5:6

Ana akuunika: 5:8

Siyanitsani zimene buku la Aefeso likuphunzitsa zokhuzana ndi chimene ife tili mwa Khristu ndi chimene tinali kale pamene tinali okufa mu zolakwa zathu ndi uchimo.

Munthu wotchedwa Tukiko akutchulidwa pa Aefeso 6:21-22. Pezani mabuku ena amene akukamba za iye monga Machitidwe 20:4; II Timoteo 4:12; Tito 3:12; Akolose 4:7.

Pezani ndime zokwana khumi ndi ziwiri zokhuza Mzimu woyera mu buku la Aefeso. Ndime zopezeka kuyambira mutu 1-3 wa Aefeso amakamba za chimene Mzimu Woyera ndi zimene amachita kwa okhulupirira. Pomwe ndime kuyambira 4-6 amakamba zimene tikuyenera kukhala ndi kuchita kwa Iye.

## CHAPUTALA 10

### AFILUPI

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Afilipi.
- Kudziwa amene wolembe amamulemba.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Afilipi.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Afilipi kuchokera pantima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Aefeso.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**KOMWE AMALEMBA:** Kumpingo wa ku Afilipi

**CHOLINGA:** Kupempha umodzi wa Chikhristu

**VESI LOTSOGOLERA:** Afilipi 2:2

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Umodzi mwa Yesu umabweretsa chimwemwe

**ANTHU OPEZEKAMO:** Paulo, Timoteo, Epafrodito, Kaesala

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-26

A. Moni: 1:1-2

1. Kuchokera kwa Paulo ndi Timoteo: 1:1
2. Kupita kwa: Oyera mtima mwa Khristu, oyang'anira ndi atumiki a ku Filipi: 1:1
3. Chisomo ndi mtendere: 1:2

B. Pemphero la kwa Afilipi: 1:3-11

1. Mayamiko ake chifukwa cha iwo: 1:3-5
  - a. Cholinga choyamikira: 1:3
  - b. Kufotokoza mayamikowo: 1:4

- c. Chimene chinapangisa kuwayamikira: 1:5
- 2. Kulimba mtima kwake mwa iwo: 1:6-7
  - a. Chikhalidwe cha kulimba mtima: 1:6
  - b. Kulungamitsidwa kwa kulimba mtima kwake: 1:7
- 3. Khumbo lake: 1:8
- 4. Pemphero lake kwa iwo: 1:9-11
  - a. Kuti chikondi chikachuluke muchidziwitso ndi muchiweruzo: 1:9
  - b. Kuti mutsimikize zinthu zimene ndi zapawamba: 1:10
  - c. Kuti mukakhale oona mtima ndi opanda cholakwa: 1:10
  - d. Kuti mukadzadzidwe ndi chipatso cha chilungamo: 1:11
- C. Zinthu zokhuza munthu: 1:12-26
  - 1. Zochitika zimene zathandizira kulalikira uthenga wabwino: 1:12-18
    - a. Ukapolo: 1:12-14
    - b. Ulaliki: 1:15-18
    - c. Pemphero: 1:19
  - 2. Funso lakutu ndi bwino kukhala ndi moyo kapena kufa: 1:19-26
    - a. Kusiyana pakati pa moyo ndi imfa: 1:20-21
    - b. Zofuna za moyo: 1:22
    - c. Kulimbana ndi khumbo la imfa: 1:23-24
    - d. Chitsimikizo cha moyo wautali: 1:25-26
- II. Chilimbikitso pa umodzi 1:27-2:18
  - A. Pempho la umodzi mmasautso: 1:27-30
    - 1. Makhalidwe abwino: 1:27
    - 2. Kukhazikika mu mzimu ndi maganizo amodzi: 1:27
    - 3. Kulimbikira limodzi mchikhulupiriro cha uthenga wabwino: 1:27
    - 4. Osaopsezewa ndi adani anu ndi chilichonse: 1:28-30
  - B. Umodzi mwa Khristu: 2:1-11
    - 1. Kuchokera mmakhalidwe abwino: 2:1-4
      - a. Chikondi: 2:1-2
      - b. Chiyanjano: 2:1
      - c. Chifundo: 2:1
      - d. Mtima umodzi: 2:2
      - e. Maganizo amodzi: 2:2
      - f. Osachita kanthu monga mwa chotetana kapena mofuna ulemerero koma mofatsa: 2:3
      - g. Osaganizira zinthu za inu nokha, koma muganizirensa kuchitira ena: 2:4
    - 2. Kuchepetsedwa kwa Khristu: Konzani maganizo anu kuti afanane ndi Khristu: 2:6-8
      - a. Kudzikhutula: 2:7

- b. Mmakhalidwe akapolo: 2:7
    - c. Kufanana ndi anthu: 2:7
    - d. Anadzichepetsa yakha: 2:8
    - e. Kumvera pa imfa ya pamtanda: 2:8
  - 3. Kukwezedwa kwa Khristu: 2:9-11
    - a. Anakwezedwa pamwamba: 2:9
    - b. Dzina lopusamayina onse: 2:9
    - c. Bondo lililonse ligwade: 2:10
    - d. Lilime lililonse livomereze: 2:11
- C. Kukula mu uzimu kumabweretsa umodzi: 2:12-18
  - 1. Gwirani ntchito yanu ya chipulumutso mwa mantha: Pakuti ndi Mulungu: 2:12-13
  - 2. Mupange zinthu osanyinyilika: Kuti mukakhale opanda banga: 2:14-15
  - 3. Gwirtsani mawu amoyo: Kuti ndikondwere: 2:16-18

### III. Malingaliro a Paulo: 2:19-30

- A. Malingaliro ake a Timoteo: 2:19-23
  - 1. Malingaliro: 2:19
  - 2. Cholinga cha malingaliro: 2:19
  - 3. Zifukwa zosankhira Timoteo: 2:20-21
  - 4. Ubale wa Timoteo ndi Paulo: 2:22
  - 5. Nthawi ya ulendo wa Timoteo: 2:23
- B. Malingaliro a iye yekha: 2:24
- C. Malingaliro a Epafrodito: 2:25-30
  - 1. Zimene zinali mmalingalirozo: 2:25
  - 2. Umboni wa Epafrodito: 2:25
  - 3. Chifukwa chomtumira Epafrodito: 2:26-27
  - 4. Kulandirdwa kuperekedwa: 2:28-30

### IV. Machenjezo 3:1-4:1

- A. Okhuzana ndi aphunzitsi a Chiyuda: 3:1-16
  - 1. Chimwemwe cha Ambuye ngati chodzitetezera: 3:1
  - 2. Awalimbikitsa kuti akhale tcheru: 3:2
  - 3. Chizindikiro cha Israyeli weniweni: 3:3
  - 4. Zimene Paulo anakumana nazo zokhuza izi: 3:4-11
    - a. Maziko ake odzitamandira pa chilamulo: 3:4-6
      - (1) Kudulidwa: 3:5
      - (2) Wa m'badwo wa Israyeli: 3:5
      - (3) Wa fuko la Benjamini: 3:5

- (4) Mfalisi: 3:5
  - (5) Machawi (Mpingo wozunzidwa): 3:6
  - (6) Chilungamo mwa chilamulo: 3:6
  - b. Masinthidwe ake a zinthu: 3:7-11
    - (1) Chikhalidwe cha kusinthako: 3:7
    - (2) Zifukwa zosinthirazo: 3:8
    - (3) Cholinga chosinthiracho: 3:8-11
  - 5. Ungwiro ngati chothanira kusunga malamulo: 3:12-16
    - a. Malingaliro pa ungwiro: 3:12
    - b. Kuchitapo kanthu kufikira cholinga: 13-14
    - c. Chilimbikitso ku ungwiro: 3:15-16
  - B. Zokhuza aphunzitsi onyenga: 3:17-21
    - 1. Chikhalidwe chawo: 3:18
    - 2. Tsogolo lawo: 3:19
    - 3. Mmene okhulupirira achitire: 3:20-21
- V. Zilimbikitso: 4:1-9
- A. Umodzi pakati pa Euidiya ndi Suntuke: 4:1-3
  - B. Umodzi mu chimwemwe: 4:4
  - C. Umodi mu chifatso: 4:5
  - D. Umodzi mpemphero: 4:6
  - E. Umodzi mu mtendere: 4:7
  - F. Umodzi mmaganizo: Makhalidwe ka malingaliro oyenera: 4:8
    - 1. Olondola.
    - 2. Olemekezeka.
    - 3. Olungama.
    - 4. Oyera.
    - 5. Okonda.
    - 6. Ambiri yokoma.
    - 7. Zinthu zabwino.
    - 8. Zinthu zotamandika.
  - G. Umodzi pakati pa chidziwitso ndi ntchito: 4:9
- VI. Chiyamiko chifukwa cha mphatso: 4:10-20
- A. Chinsisi cha kukhala wokwanitsidwa: 4:10-13
    - 1. Kuthokoza kwake chifukwa cha mphatso yawo: 4:10
    - 2. Kukhala payekha osadalira zinthu zawo: 4:11
    - 3. Kulongosola chinsisi chake: 4:11-12

4. Gwero la mphamvu: 4:13
- B. Chinsisi cha kupereka: 4:14-20
  1. Kuyamikira kwake pa mphatso: 4:14
  2. Chikumbutso chake pa zomwe zidachitika kale: 4:15-16
  3. Malingaliro ake pa mphatso yawo: 4:17
  4. Umboni wake woti walandira mphatso: 4:18
  5. Chinsisi cha kupereka: 4:19-20

VII. Nyimbo: 4:21-23

- A. Ulemu kwa oyera mtima mwa Khristu: 4:21
- B. Abale limodzi ndi Paulo apereka moni: 4:21
- C. Oyera mtima ndi a mnyumba ya Kaisara apereka moni: 4:22
- D. Chisomo chikhale ndi inu: 4:23



## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Afilipi ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amelemba buku la Afilipi.

---

---

---

3. Kodi buku la Afilipi amalemba ndani?

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Afilipi.

---

---

---

5. Lembani Vesi lotsogolera la buku la Afilipi kuchokera pamtima.

---

---

---

(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kweni-kweni kwa bukhu lino).

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani mawu aakulu monga kukondwera ndi chimwemwe. Mawuwa akupezeka kokwanira khumi ndi kasanu ndi mphambu katatu (18).
2. Iyi ndi njira inaso imene mungawerengere buku la Afilipi:

<b>Mutu</b>	<b>Vesi Lalikulu</b>	<b>Mutu waukulu</b>
1	21	Moyo wa Okhulupirira
2	5	Maganizo a okhulupirira
3	10	Cholinga cha okhulupirira
4	13	Mphamvu za okhulupirira

3. Mpingo wa ku Afilipi unayambika chifukwa cha zotsatira za masomphenya amene Paulo anakumana nawo. Werengani zokhudza izi pa Machitidwe 16:8-10.
4. Afilipi akulongosola mitundi iwiri ya mtendere imene ikupezeka M'baibulo. Kukhala pamtendere ndi Mulungu kwa okhulupirira onse monga akulankhula pa Aroma 5:1. Mtendere wa Mulungu umene ndi wa okhulupirira onse ukupezekanso pa Afilipi 4:7.
5. Mulungu adachita zodwabwitsa kwa anthu atatu mu mpingo wa ku Afilipi:
  - Wobwebeta mkumalosera: Machitidwe 16:16-18
  - Mzimayi wochita malonda: Machitidwe 16:13-15
  - Mdindo wa Chiroma: Machitidwe 16:19-20
6. Onani zolinga za Paulo mu mutu 3:
  - Kuti akapindule:8
  - Kuti akadziwe: 10
  - Kuti akafikire: 11
  - Kuti akazindikira: 12
7. Lembani mndandanda wa zomuyenereza Paulo ku dziko lapansi: 3:8-12
8. Werengani Afilipi 1:12-21. Lembani njira zosiyasiyani zimene uthenga wabwino unapambana.
9. Lembani makhalidwe abwino amene akupezeka pa Afilipi 4:8-9

## CHAPUTALA CHA 11

### AKOLOSE

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Akolose.
- Kudziwa yemwe wolembe bukuli amawalemba.
- Kutchula cholinga chomwe amalemba buku la Akolose.
- Kulemba Vesi lotsogolera la buku la Akolose kuchokera pantima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Akolose.

#### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**KOMWE AMALEMBERA:** Kwa onse okhulupirira a ku Akolose limodzi ndi a ku Laodikaya.

**CHOLINGA:** Kulimbana ndi ziphunzitso za mpingo

**VESI LOTSOGOLERA:** Akolose 3:3-3

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Yesu ali zonse mu zonse

**ANTHU OPEZEKAMO:** Paulo, Tukiko, Luka, Dema, Epafrata

#### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-14

A. Moni: 1:1-2

1. Kuchokera kwa: Paulo ndi Timoteo: 1:1
2. Kupita kwa: Oyera mtima ndi abale okhulupirirka a ku Akolose: 1:2
3. Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu ndi Yesu: 1:2

B. Chiyamiko: 1:3-8

C. Pemphero la Paulo kwa Akhristu a ku Akolose: 1:9-14

1. Lopitilira: 1:9
2. Kukhumbitsa kuti adzdzidwe ndi chidziwitso cha chifuniro chake mu nzeru ndi mzimu wa kumvetsetsa: 1:9
3. Kuti ayende mayendedwe oyenera a Ambuye: 1:10
4. Kuti akabale chipatso mu ntchito zonse zabwino: 1:10
5. Kuti akachuluke mu nzeru za Mulungu: 1:10
6. Kuti alimbikitsidwe ndi chipiriro, kukuma mtima ndi mchimwemwe chonse: 1:11
7. Kuti mayamiko apite kwa Atate: 1:12-13
  - a. Ndi kulandira nawo cholowa cha oyera mtima mkuunika: 1:12
  - b. Potiwombola ife kuchokera ku mphamvu ya mdima: 1:13
  - c. Potitengera ife mu Ufumu wa mwana wake: 1:13

## II. Umunthu ndi ntchito za Yesu: 1:15-23

### A. Ambuye wa chilengedwe: 1:15-17

1. Mogwirizana ndi chiyambi: 1:15-16
2. Mogwirizana ndi kupitilira: 1:17

### B. Ambuye wa mpingo: 1:18-19

1. Mutu wa thupi: 1:18
2. Chiyambi: 1:18
3. Wobadwa oyamba wa akufa: 1:18
4. Kuti akakhale Iye mwa zonse woyambayamba: 1:18
5. Mwa Iye, muli chidzalo chonse: 1:19

### C. Woyanjanitsa: 1:20-23

1. Wapereka mtendere mwa mwazi wake wa pamtanda: 1:20
2. Wayanjanitsa zinthu zonse kwa Iye, zapadziko ndi zamwamba: 1:20
3. Kwa iwo amene anali akutali mwa ntchito zawo wayanjanitsa: 1:21
4. Mwa imfa yake, tayenereredwa kukhala: 1:22
  - a. Woyera.
  - b. Opanda chilema.
  - c. Osaweruzidwa mmaso mwake.
5. Tikuyenera tipitilire muchikhulupiriro: 1:23
  - a. Ozikika: 1:23
  - b. Osagwedezeke: 1:23
  - c. Osasunthika ku uthenga wabwino umene: 1:23
    - (1) Adaumva ndi iwo.

(2) Wolalikiidwa ku cholengedwa chonse.

(3) Umene Paulo anatchedwa now mtumiki.

### III. Paulo: Mtumiki wa Mulungu woyanjanitsa: 1:24-2:7

#### A. Masautso: 1:24

1. Kuthupi.
2. Ndi choline cha ku uzimu.

#### B. Mtumiki wa chinsisi cha Khristu: 1:25-29

1. Nyengo za utumiki wake: 1:25
2. Uthenga wa utumiki wake: 1:26-27
  - a. Chinsisi cha Mulungu: 1:26-27
  - b. Yesu Mwini: 1:27
3. Njira zimene anachitira utumiki wake: 1:28
  - a. Kulalikira.
  - b. Kuchenjeza.
  - c. Kuphunzitsa.
4. Cholinga cha utumiki wake: Kupanga aliyense kukhala wangwiro wa Yesu: 1:28
5. Mphamvu ya utumiki wake: Kuchita molingana ndi machitidwe ake a mphamvu:  
1:29

#### C. Khumbo la umodzi ndi kukhazikika mwa Khristu: 2:1-7

1. Chidwi chake cha pa okhulupirira: 2:1
  - a. Ku Akolose.
  - b. Ku Laodikaya.
  - c. Kwa iwo amene sanawaone.
2. Kwa iye amene akufunafuna: Mulungu Atate ndi Khristu: 2:2
3. Cholinga cha kufunafunako: 2:2-7

- a. Kuti mitima yawo itonthozedwe: 2:2
- b. Kuti akhalire limodzi mchikondi: 2:2
- c. Kuti atsimikizike pa chuma chonse ndi kukuzindikira: 2:2
- d. Kuti akazindikire chuma ndi nzeru chobisika mwa Yesu: 2:3
- e. Kuti munthu asakusokeretseni ndi mawu okopakopa: 2:4
- f. Kuti akhale okhazikika mchikhulupiriro: 2:5
- g. Kuti akayende mwa Khristu: 2:6
- h. Kuti akakhale ozika mizu mwa Iye: 2:7
- i. Kuti akakhale owumbika mwa Iye: 2:7
- j. Kuti akhazikike mchikhulupiriro monga anaphunzitsidwa 2:7
- k. Kuti akachuluke chichulukire mchiyamiko: 2:7

IV. Umbuye wa Khristu kuposa chiphunzitso chabodza: 2:8-3:4

A. Ambuye wa mphamvu yonse: 2:8-10

- 1. mnzeru: 2:8
- 2. Chinyengo chopanda pake: 2:8
- 3. Miyambo ya anthu: 2:8
- 4. Makhalidwe a dziko lapansi osati a Khristu: 2:8
  - a. Mwa Iye chidzalo chonse cha Umulungu kuthupi: 2:9
  - b. Ndinu okwanira mwa Iye: 2:10
  - c. Iye ndi mutu wa ma ukulu ndi mphamvu: 2:10

B. Moyo watsopano: 2:11-14

- 1. Mdulidwe wa mumtima: 2:11
- 2. Kuikidwa ndi Iye mu ubatizo: 2:12
- 3. Kuuka naye Mchikhulupiriro: 2:12
- 4. Kudzutsidwa limodzi ndi Iye: 2:13

5. Zolakwa zonse zakhululuikidwa: 2:13
6. Adafafaniza zolembedwa za ife zotsutsana nafe: 2:14

C. Mgonjetsi wa ma ukulu ndi mphamvu: 2:15

1. Anaziononga: 2:15
2. Adaziika poyera: 2:15
3. Anazigonjetsa: 2:15

D. Makhalidwe okana Umbuye wa Khristu: 2:16-3:4

1. Zikhalidwe: 2:16-17

- a. Nyama: 2:16
- b. Zakumwa: 2:16
- c. Masiku opatulika: 2:16
- d. Tsiku lokhala mwezi: 2:16
- e. Masiku a sabata: 2:16

2. Kulambira Angelo: Amene achita izi ndi: 2:18-19

- a. Kukhazikika mu zinthu zimene simunazione: 2:18
- b. Odzitukumula ku maganizo ake akuthupi: 2:18
- c. Osamutenga Khristu ngati mutu: 2:19
  - (1) Kumene thupi lonse litengako zofunikira.
  - (2) Amene ndi Iye talumikizana mchikondi.
  - (3) Amene ndi Iye tichulukitsa chidziwitso cha Mulungu.

3. Ogonjera ku makhalidwe a dziko lapansi: 2:20-23

- a. Sitawagonjera iwo: 2:20
- b. Zimene achita nazo: 2:21
- c. Lamulo la ziphunzitso za anthu: 2:22
- d. Amasamala za maonekedwe a kunja: 2:23

- (1) Anzeru mu mafunidwe a chipemebdzo.
- (2) Akudzichepetsa.
- (3) Osasamala za thupi.
- (4) Osati ku ulemerero okwaniritsa zofuna za thupi.

4. Zadziko, ziyanjano za nthawi yochepa: 3:1-4

- a. Funani zinthu za pamwamba: 3:1
- b. Lingalirani zinthu zakumwamba, osati za pansu: 3:2
- c. Izi ndi zotheke chifukwa cha ubale wanu mwa Khristu: 3:3

(1) Kale: Munaukitsidwa ndi Khristu: 3:3

(2) Tsopano: Moyo wanu wabisika ndi Khristu mwa Mulungu: 3:3

(3) Mtsogolo: Pamene Khristu adzonekera, nanunso mudzaonekera ndi Iye mu ulemerero:  
3:4

V. Umbuye wa Khristu ndi moyo wa chikristu: 3:5-4:6

A. Tili ndi udindo wofesa zilakolako za thupi: 3:5

B. Mkwiyu wa Mulungu ubwera pa osamvera ndi okwaniritsa zokhumba za thupi: 3:6

C. Kale tinayenda mmakhalidwe otere, koma pano tivule makhalidwewo: 3:7-8

D. Kuvula moyo wakale: 3:5-9

- 1. Dama: 3:5
- 2. Chidetso: 3:5
- 3. Chifunitso cha manyazi: 3:5
- 4. Chilakolako choipa: 3:5
- 5. Chisiliro kumene ndi kupembedza mafano: 3:5-7
- 6. Kupsa mtima: 3:8



7. Mkwiyoy: 3:8
  8. Dumbo: 3:8
  9. Mwano: 3:8
  10. Zonyasa zotuluka mkamwa: 3:8
  11. Mabodza: 3:9
- E. Kuvala moyo watsopano: 3:10-17
1. Munthu watsopano: 3:10
    - a. Amene ali kukonzedwa watsopano mu chizindikiro cha iye amene anamulenga: 3:10
    - b. Mwa Iye mulibe kugawana: 3:11
  2. Zotengera za zifundo: 3:12
  3. Kukoma mtima: 3:12
  4. Kudzichepetsa mmaganizo: 3:12
  5. Chifatso: 3:12
  6. Kuleza mtima: 3:12
  7. Kulolerana wina ndi nzake: 3:13
  8. Kukhulukirana: 3:13
  9. Chokondano: 3:14
  10. Mtendere wa Mulungu: 3:15
  11. Umodzi mthupi: 3:15
  12. Chiyamiko: 3:15
  13. Mawu a Mulungu akhale mwa inu chichulukire: 3:16
    - a. Mu nzeru zonse.
    - b. Chiphunzitso.

c. Kulimbikitsana wina ndi nzake mmasalimo, mu nyimbo ndi maimbidwe a uzimu.

14. Ntchito za bwino: 3:17

- a. Mmawu ndi mu ntchito.
- b. Zikachitike mu dzina la Yesu.
- c. Kuyamika Mulungu.

F. Nyengo za paderadera: 3:18-4:6

1. Pakhomo: 3:18-21

- a. Akazi: 3:18
- b. Amuna: 3:19
- c. Ana: 3:20
- d. Atate: 3:21

2. Maubale akutchito: 3:22; 4:1

- a. Mverani iwo amene ndi ambuye mu thupi: 3:22
- b. Tumikirani ngati kwa Khristu: 3:22
- c. Inu amene ndi ambuye chitirani akapolo anu cholungama ndi chofanana: 4:1

3. Zoyenera kutsatidwa: 3:23-25

- a. Chitani ngati mukuchitira Ambuye osati munthu: 3:23
- b. Zindikirani kuti mukutumikira Ambuye amene adzakupatsani mphoto: 3:24
- c. Dziwitsani kuti ochita zoipa adzalandira chilungamo kwa Mulungu: 3:25

VI. Malangizo otsiriza: 4:2-6

A. Ntchito ya pemphero: 4:2-4

1. Udindo wopitiliza kukhala mpemphero: 4:2
2. Kudikira ndi kuyamika: 4:2
3. Kupempherera makomo atseguke kwa iwo akulalikira uthenga wabwino: 4:3-4

B. Ntchito ya kuchitira umboni: 4:5-6

1. Mayendedwe oyenera a nzeru: 4:5
2. Kugwiritsa ntchito nthawi moyenera: 4:5
3. Mayankhulidwe oyenera: 4:6
  - a. Ndi chisomi.
  - b. Okhala ndi mchere.
  - c. Ndi chidziwitso cha mmene mungayankhire aliyense.

VII. Mawu otsiriza: 4:7-18

A. Moni wake: 4:7-17

1. Eni wake a kalatayi: 4:7-9
  - a. Tukiko: 4:7-8
  - b. Onesimo: 4:9
2. Moni kuchokera kwa amene anali nawo limodzi: 4:10-14
3. Mawu otsiriza a ku Laodikaya ndi kuwapempha kuti awerengenzso kalatayi: 4:15-16
4. Uthenga wapadera wopita kwa Arkipo: 4:17

B. Mawu otsiriza: 4:18

1. Ndi dzanja la Paulo.
2. Pempho loti akumbukire ubale wawo.
3. Chisomo chikhale ndi inu.

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Akolose ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la Akolose.

---

---

3. Kodi wolemba bukuyi amalemba ndani?

---

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Akolose.

---

---

5. Lembani Vesi lotsogolera la buku la Akolose kuchokera pamtima.

---

---

---

**(mayankho amafunso amenewa ali kumapeto kwa buku limeneli)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani Akolose 3:2-17. Lembani mndandanda wa zintu zimene okhulupirira ayenera kuzivula ndi zimene ayenera kuvala mu moyo wawo wa uzimu.
2. Werengani Akolose 3:18-25. Ndimeyi imakamba za ziwalo zosiyanasiyana mu mpingo. Lembani malamulo amene anaperekedwa kwa akazi, amuna, ana, atate, ndi akapolo.
3. Buku la Akolose limaphunzitsa zinthu zambiri zokhuza Yesu. Werengani bukuli and kulemba vesi imene imakamba za Yesu ndipo nenani mwachidule zimene mwaphunzira zokhuza Yesu mu vesi lililonse.
4. Akolose ndi limodzi mwa makalata awiri a Muchipangano Chatsopano limene limapereka lamulo ku mpingo kuti athe kusinthana ndi kuwerenga makalata kumpingo ina. Fananitsani Akolose 4:16 ndi I Atesalonika 5:27.
5. Kalata ya Akolose ndi Aefeso imafanana. Ku Aefeso Paulo amakamba za thupi la Khristu ngati mpingo. Ku Akolose akulemba za mutu wa thupi, ndiye Yesu Khristu. Pafupifupi Mwa ma vesi 78 pa mavesi 95 ku Akolose ndi ofanana ndi mavesi amu Aefeso. Werengani ndi kufananitsa mabuku awiriwa.
6. Wrengani Akolose 1:12-22. Pali zinthu zisanu ndi ziwiri zofunika zokhuza chipulumutso ngati:
  - Cholowa: Olandira cholowa cha oyera mtima mkuunika: 12
  - Mamasulidwe: Amene anatisintha kupita ku Ufumu wa Mwana wake wa chikondi: 13
  - Kusinthana: Ndipo anatisintha kupita ku Ufumu wa Mwana wake wa chikondi: 13
  - Maomboledwe: Mwa Iye tili nawo maomboledwe mwa mwazi wake: 14
  - Chikhululukiri: Ngakhale chikhululukiro cha machimo: 14
  - Chiyanjanitso: Ndipo anatiyanjanitsa: 21
  - Mawalitsidwe: Kuti tikakhale oyera ndi opanda banga pamaso pake: 22

## CHAPUTALA CHA 10

### I NDI II ATESALONIKA

#### ZOLINGA

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula wolembe mabuku a I ndi II Atesalonika.
- Kuzindikira komwe wolembe mabukuwa amawalemba.
- Kutchula zolinga zimene amalemba mabuku a I ndi II Atesalonika.
- Kulemba mavesi lotsogolera a mabuku a I ndi II Atesalonika kuchokera pamtima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya mabuku onse awiri.

### I ATESALONIKA

#### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**KOMWE AMALEMBERA:** Okhulupirira a ku Tesalonika

**CHOLINGA:** Kutsimikiza kuti Ambuye akubweranso. Kuyamikira komanso kulimbikitsa chifukwa cha chikhulupiriro komanso kukonza chiphunzitso chabodza. Komanso Paulo amayankhapo za zimene amamunena zabodza zokhuza utumiki wake.

**VESI LOTSOGOLERA:** I Atesalonika 4:16-18

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Chithonhozo chikhale cha chiyembekezo cha ulemerero wa kubweranso kwa Yesu Khristu.

**ANTHU OPEZEKA:** Paulo, Silivano, Timoteo.

#### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1

- A. Kuchokera kwa: Paulo, Silivano ndi Timoteo
- B. Kupita kwa: Okhulupirira a ku Atesalonika.
- C. Chisomi ndi Mtendere zochokera kwa Mulungu ndi Yes: 1:1

## II. Kunyang'ana kumbuyo: 1:2-3:13

### A. Makhalidwe otsanza Khristu: 1:2-10

1. Mphamvu ya uthenga wabwino: 1:2-5
2. Zitsanzo za uthenga wabwino: 1:5-6
  - a. Okhulupirira a ku Atesalonika anatsatira chitsanzo cha Paulo: 1:5-6
  - b. Anakhala chitsanzo kwa okhulupirira ena: 1:7
3. Mboni za uthenga wabwino: 1:8-10
  - a. Chikhulupiriro cha okhulupirira a ku Atesalonika chinafalikira paliponse: 1:8
  - b. Adachitira umboni ku choonadi chanuthenga wabwino: 1:9-10

### B. Kulalikira kwa chitsanzo: 2:1-20

1. Mmalingaliro: 2:1-6
  - a. Osati mu zopanda pake: 2:1
  - b. Mkulimba mtima: 2:2
  - c. Osati muchinyengo, mchodetsa kapena mmachenjerero: 2:3
  - d. Kusangalasa Mulungu osati munthu: 2:4
  - e. Opanda mawu okopa: 2:5
  - f. Opanda kusirira: 2:5
  - g. Not to seek glory of men: 2:6
2. Mmakhalidwe: 2:7-11
  - a. Kufatsa: 2:7
  - b. Kukhala ngati azamba ndi ana: 2:7
  - c. Mu chikondi
  - d. Mu ululu kapena nyengo yowawa: 2:9
  - e. Ndi makhalidwe oyenera: 2:10
  - f. Monga tate ndi ana ake: 2:11
3. Mu uthenga: 2:12-13
  - a. Kuti muyende koyenera Mulungu: 2:12
  - b. Zinali zokhazikika pa mawu a Mulungu: 2:13
4. Mu chivomerezo: 2:13-16
  - a. Chikhalidwe cha kulandira kwawo kwa mawu: 2:13
  - b. Zotsatira za kulandira kwawo kwa mawu: 2:14-16
    - (1) Adakhala akusanza a mipingo ya ku Yudeya: 2:14
    - (2) Adalowa mu chiyanjano cha zowawa cha mawu a Mulungu: 2:14-16

### C. Chitsanzo chotsamalira otembenuka kumene: 3:1-13

1. Chidwi chawo: 3:1-5
  - a. Zolinga zawo: 3:1
  - b. Kutumidwa kwa Timoteo: 3:2
  - c. Mmene analili wotumidwayo: 3:2
    - (1) Mbale wathu.

- (2) Mtumiki.
- (3) wogwira ntchito limodzi mu Uthenga wabwino.
- d. Cholinga chomtumira Timoteo: 3:2-4
  - (1) Kuti akhazikitse inu: 3:2
  - (2) Kuti atonthoze inu: 3:2
  - (3) Kuti alimbikitse kukhazikika posatengera zovuta: 3:3-4
  - (4) Kuti akutetezeni kwa oyesayo: 3:5
  - (5) Kuti ateteze ntchito yawo: 3:5
- 2. Machitidwe ake a kalondolondo: 3:6-8
  - a. Zimene zinali mu zolembe za Timoteo: 3:6
  - b. Mmene adachitira pa zolembe za Timoteo: 3:7-10
    - (1) Chithonhozo ndi chilimbikitso: 3:7-8
    - (2) Mayamiko ndi pemphero: 3:9-13
- III. Kuyang'ana kutsogolo: Makhalidwe molingana ndi kubwera kwa Ambuye: 4:1-5:24
  - A. Makhalidwe okondweretsa Mulungu: 4:1-2
  - B. Chiyeretso: 4:3-8
    - 1. Maziko a chiyeretso chawo: Ndicho chifuniro cha Mulungu: 4:3
    - 2. Machitidwe a chiyeretsocho: 4:3-8
      - a. Kudziletsa ku dama: 4:3-5
      - b. Kudziletsa kwa mbale wonyenga: 4:6
  - C. Zifukwa zokhala ndi makhalidwe oyenera: 4:6-8
    - 1. Mulungu amabwenzera pa tchimo: 4:6
    - 2. Makhalidwe oyenera amagwirizana ndi mayitanidwe a Mulungu: 4:7
    - 3. Kukana makhalidwe oyenera ndiko kukana Mulungu: 4:8
  - D. Chikondi cha pa abale: 4:9-10
    - 1. Kuwayamikira chifukwa cha chikondi: 4:9
    - 2. Chilimbikitso cholimbikitsa chikondi: 4:10
  - E. Chilimbikitso choti akhale ochitachita: 4:11-12
    - 1. Phunzirani kukhala chete: 4:11
    - 2. Chitani za inu nokha: 4:11
    - 3. Gwirani ntchito ndi manja anu: 4:11
    - 4. Yendani moona mtima kwa osakhulupirira: 4:12
  - F. Malangizo okhuzana za iwo akufa mwa Ambuye: 4:12-18
    - 1. Kufunika kwa malangizo oyenera: 4:12-13
    - 2. Ubale wa iwo akufa ndi kubweranso kwa Yesu: 4:14-15
      - a. Okufa mwa Ambuye adzawatengera kwa Iye: 4:14
      - b. Amoyo sadzatsogolera okufa mwa Khristu: 4:15
    - 3. Mmene angazabwerere Khristu ndi zotsatira zake: 4:16-17
      - a. Mabweredwe ake: 4:16



- b. Zotsatira za kubwera kwake: 4:16-17
      - (1) Akufa adzauka koyamba: 4:16
      - (2) Amoyo adzakwatulidwa: 4:17
      - (3) Okhulupirira adzakhala ndi Ambuye kwa muyaya: 4:17
  - 4. Chithonhozo cha mawu awa chigwiritsidwe ntchito ndi okhulupirira: 4:18
- G. Kudikilira za kubwera kwa Ambuye: 5:1-11
  - 1. Nthawi ya kubwera kwake siidziwika: 5:1-2
    - a. Kusowa kwa kufunika kwa malangizo: 5:1
    - b. Chidziwitso chawo pa zakubwera kwake: 5:2
  - 2. Zotsatira za kusadziwa nthawi kwa iwo osakonzekera: 5:3
  - 3. Zotsatia kwa kusadziwa nthawi kwa okhulupirira: 5:4-11
    - a. Khalani okonzeka: 5:4
    - b. Yendani mkuunika: 5:5
    - c. Musagone kuuzimu: 5:6
    - d. Dikirani: 5:6
    - e. Musaledzere: 5:6-8
    - f. Valani cha pachifuwa cha chikhulupiriro ndi chikondi: 5:8
  - 4. Chitsimikizo cha okhulupirira: 5:9-11
    - a. Tinasnkhidwa ku chipulumutso, osati ku mkwiyo: 5:9-10
    - b. Chithonhozo ndi chilimbikitso cha chiyembekezo: 5:11
- H. Maubale a mipingo: 5:12-15
  - 1. Zindikirani iwo akugwira ntchito mwa inu ndi kwa inu: 5:12
  - 2. Alemkezeni chifukwa cha ntchito yawo mmalo mwanu: 5:13
  - 3. Achenjezeni bwino: 5:14
  - 4. Limbikitsani amphwayi: 5:14
  - 5. Thandizani ofooka: 5:14
  - 6. Lezani mmtima kwa onse: 5:14
  - 7. Musabwenzere choipa ku choipa: 5:15
  - 8. Londolani choyenera: 5:15
- I. Makhalidwe a munthu: 5:16-22
  - 1. Kondwerani nthawi zonse: 5:16
  - 2. Pempherani osalekeza: 5:17
  - 3. Mu zonse yamikani: 5:18
  - 4. Musazime mzimuyo: 5:19
  - 5. Musanyoze chinenero: 5:20
  - 6. Yetsani zinthu zonse: 5:21
  - 7. Gwiritsani chabwino: 5:21
  - 8. Pewani maonekedw onse a choipa: 5:22
- IV. Mawu otsiriza: 5:23-28

- A. Mdalitso pa onse: 5:23-24
- B. Dandaulo la pemphero: 5:25
- C. Moni: 5:26
- D. Lamulo: 5:27
- E. Kufuna chisomo cha Ambuye: 5:28

## II ATESALONIKA

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**OMWE AMAWALEMBERA:** Mpingo wa ku Atesalonika

**CHOLINGA:** Kulangiza okhulupirira amene akudikira kubweranso kwa Ambuye

**VESI LOTSOGOLERA:** II Ateasalonika 2:3

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Poganzira kuti padzakhala kugwa kwakukulu lisanafike tsiku la Ambuye, ndi zofunika kuphunzitsa ndi kusunga chiphunzitso cholondola.

**ATHU OPEZEKA:** Paulo, Silivano ndi Timoteo

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-2

- A. Kuchokera kwa Paulo, Silivano ndi Timoteo: 1:1
- B. Kupita ku mpingo wa ku Atesalonika: 1:1
- C. Chisomo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu ndi Yesu: 1:2

II. Chithonhozo pa chiyembekezo cha kubweranso kwa Ambuye: 1:3-12

- A. Kuyamika chifundo cha makhalidwe a Chikhristu: 1:3-4
  - 1. Chifukwa chimene amawayamikira: 1:3
    - a. Kukula kwa chikhulupiriro chawo mopitilira: 1:3
    - b. Kuchitira ena zachifundo kwawo: 1:3
  - 2. Zotsatira za makhalidwe awo kwa olemba: 1:4
- B. Chithonhozo mwa kuweruza kolungama kwa Mulungu: 1:5-10
  - 1. Chizindikiro cha chiweruzo cholungama cha Mulungu: 1:5
  - 2. Vumbulutso la chiweruzo cholungama cha Mulungu: 1:6-8
    - a. Zotsatira za chiweruzo chake: 1:6-7
      - (1) Mulungu akutumiza chitsautso kwa amene akutsautsa: 1:6
      - (2) Iwo otsautsidwa adzapeza mpumulo Ambuye akafika: 1:7
    - b. Nthawi ya chiweruzo: Pamene Ambuye adzaonekera kumwamba



- e. Adzabweretsa chiweruzo kwa iwo amene: 2:12
  - (1) Sanakhulupirire choonadi.
  - (2) Amakondwera ndi chosalungama.
- C. Pemphero la okhulupirira a ku Atesalonika: 2:13-17
  - 1. Kuyamika chifukwa Mulungu adawasankha: 2:13-14
    - a. Adawasankha ku chipulumutso mwa Chiyeretso cha Mzimu Woyera ndi kukhulupirira choonadi: 2:13
    - b. Adawayitana mwa Uthenga wabwino ku ulemerero wa Yesu: 2:14
  - 2. Chilimbikitso kuti akhazikike: Gwiritsani chimene munachiphunzira: 2:15
  - 3. Pemphero la chitonthozo ndi kukhazikika kwawo: 2:16-17
    - a. Kwa amene pemphero likupita: 2:16
    - b. Zomwe zili mu pemphero: 2:17
      - (1) Kukutonhozani.
      - (2) Kukukhazikitsani mu mawu ndi ntchito yabwino.
- IV. Malamulo okhuza za kuberanso kwa Yesu: 3:1-15
  - A. Lamulo lopemphera: 3:1-2
    - 1. Ufulu polalikira uthenga wabwino: 3:1
    - 2. Chitetezo kwa olalikira uthenga: 3:2
      - a. Kuchokera kwa anthu osamvetsa.
      - b. Kuchokera kwa anthu oipa.
      - c. Kuchokera kwa anthu opanda chikhulupiriro.
  - B. Lamulo loti akule mu uzimu: 3:3-5
    - 1. Khalani okhazikika mwa Ambuye: 3:3
    - 2. Khalani osungidwa ku choipa mwa Ambuye: 3:3
    - 3. Chitani zimene mwalamulidwa: 3:4
    - 4. Ikani mitima yanu mu chikondi cha Mulungu: 3:5
    - 5. Dikirani mopilira za kubweranso kwa Khristu: 3:5
  - C. Lamulo lokhazana ndi makhalidwe ndi maubale: 3:6-12
    - 1. Patukani kwa iwo amene sayenda moyenera molingana ndi mawu a Mulungu: 3:6
    - 2. Londolani chitsanzo chabwino cha utsogoleri wa uzimi: 3:7-10
    - 3. Wokhulupirira aliyense akhale ochitachita: 3:10-12
    - 4. Musaleme pakuchia zabwino: 3:13
    - 5. Osayanjana nawo iwo amene sachita mawu a Mulungu: 3:14
    - 6. Musawatenge iwo ngati adani, koma muwalimbikitse: 3:15
- V. Mawu omaliza: 3:16-18
  - A. Pembedzero: 3:16
    - 1. Ambuye akupatseni mtendere.
    - 2. Ambuye akhale ndinu nose.
  - B. Kusimikidwa: Yosindikizidwa ndi Paulo: 1:17

C. Nyimbo: 1:18

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba mabuku a I ndi II Atesalonika ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la I Atesalonika.

---

3. Kodi buku la I Atesalonika amalemba kwa ndani?

---

4. Tchulani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la I Atesalonika.

---

5. Lembanani vesi lotsogolera la buku la I Atesalonika kuchokera pamtima.

---

6. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la II Atesalonika.

---

7. Kodi buku la II Atesalonika amallembera ndani?

---

8. Tchualani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la II Atesalonika.

---

9. Lembanani vesi lotsogolera la buku la II Atesalonika kuchokera pamtima.

---

**(Mayankho a mafunso onsewa ali kumapeto kwa bukhu lino).**

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Atesalonika ndi limodzi mwa mabuku a Chipangano Chatsopano amene akutambasula ndime ziwiri zokhuza kubwera kwa wokana Khristu. (Onani II Atesalonika 2:1-12 ndi Chibvumbulutso 13:1-8).
2. Mpingo wa ku Atesalonika Udayambika ndi Paulo panthawi ya ulendo wake wachiwiri wa utumiki. (Onani Machitidwe 17:1-10).
3. Palibe buku lina M'baibulo limene limakamba za mkwatulo wa mpingo kupatula I Atesalonika. Nkhani ya mkwatuloyi ikupezeka mmachaputala asanu a buku la I Atesalonika. (Onani 1:10; 2:19; 3:13; 4:13-18; 5:1-11,23). Lembani chidule cha mndandanda wa zimene zikufotokozedwa zokhuza kubwera kwa Ambuye.
4. Onetsetsani zinthu izi zimene zikuyenera kuchitika Ambuye Yesu asanabwere:
  - Kugwa kwa okhulupirira: II Atesalonika 2:3
  - Kubwera poyera kwa munthu wosaweruzika: II Atesalonika 2:3
  - Kuchotsedwa kwa Mzimu Woyera pa dziko: II Atesalonika 2:7
  - Kusocheretsa kwakukulu: II Atesalonika 2:1
5. Machaputala 4 ndi 5 a I Atesalonika amafotokoza za chonadi chokhudza iwo amene “akugona” ndi iwo amene “ali amoyo otsala.” Lembani zimene zikukambidwa zokhuza magawo awiriwa.
6. Mu II Atesalonika Paulo akufotokozapo za mavuto amene akufunika kukonzedwa. Lembani mndandanda mavutowa ndi malangizo okhudzana vuto lililonse.
7. Mu II Atesalonika, Paulo akuwayamikira Atesalonika komanso akuwalimbikitsa za zinthu zimene akuchita bwino. Lembani zilimbikitsodzi.
8. Molingana ndi II Atesalonika, kodi chitadzachitike ndi chiyani kwa amene samvera Uthenga Wabwino?
9. Mawu otsogolera mu I Atesalonika: Uthenga Wabwino, chikhulupiriro, chikondi, chiyembekezo, Ambuye Yesu Khristu, Mulungu, Mzimu Woyera, masautso, tsiku la Ambuye.



10. Mawu otsogolera mu II Atesalonika: Masautso, zowawa, kubwera kwa Yesu, Mulungu, Mzimu, munthu wosaweruzika, chosaweruzika, tsiku la Ambuye, choonadi.

## CHAPUTALA 13

### I NDI II TOMOTEO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula amene analemba mabuku a I ndi II Timoteo.
- Kudziwa kumene mabukuwa amalemba.
- Kutchula cholinga chimene amalemba I ndi II Timoteo.
- Kulemba vesi lotsogolera la mabuku a I ndi II Timoteo kuchokera pantima.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya mabuku a I ndi II Timoteo.

**WOLEMBA:** Paulo

**OMWE AMAWALEMBERA:** Timoteo

**CHOLINGA:** Paulo analemba kalatayi kwa Timoteo ngati wogwira naye ntchito limodzi amene anali mbusa woyembekezera ku mpingo wa wa ku Aefeso. Bukuli limakamba za mavuto ena ndi zosowa zimene zinzli mu mpingowo.

**VESI LOTSOGOLERA:** I Timoteo 4:12

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Tikuyenera kukhala moyo wachitsanzo cha utumiki umene tayitanidwa.

**ANTHU OPEZEKA:** Paulo, Timoteo, Humenayo ndi Alesandro.

#### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-3

- A. Kuchokera kwa: Paulo, mtumwi wa Yesu mwa lamulo la Mulungu ndi Yesu: 1:1
- B. Kupita kwa: Timoteo, mwana wa chikhulupiriro: 1:2
- C. Chisomo, chifundo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu ndi Yesu: 1:2
- D. Personal instructions to stay in Ephesus: 1:3

**Gawo Loyamba: Lamulo kwa Timoteo kuti asunge  
chiphunzitso cholondola 1:3-20**

I. Sunga chiyero cha uthenga wabwino: 1:3-11

A. Lamulo: 1:3-4

1. Osaphunzitsa chiphunzitso china: 1:3
2. Osasamala nkhani zachabe: 1:4
3. Osasamala mawerengedwe a makolo: 1:4

B. Cholinga cha lamulo: Chikondi: 1:5

1. Chochokera mumtima woyera.
2. Cha chikumbumtima chabwino.
3. Cha chikhulupiriro chosanyenga.

C. Chifukwa chimene anamulamula: 1:6-11

1. Ena anatsata mawu opanda pache: 1:6
2. Anasankha kukhala aphunzitsi koma osazindikira: 1:6
3. Anasata chilamulo mosayenera: 1:8-11
  - a. Chilamulo chilibwino ngati chigwiritsidwa ntchito moyenera: 1:8
  - b. Chilamulo sichinapangidwire olungama: 1:9
  - c. Chilamulo chinapangidwira ophwanya lamulo: 1:9-10
    - (1) Osamvera: 1:9
    - (2) Osapembedza: 1:9
    - (3) Ochimwa: 1:9
    - (4) Osayera: 1:9
    - (5) Osalemekeza ndi amnyozo: 1:9
    - (6) Akupha: 1:9
    - (7) Achigololo: 1:10
    - (8) Akuchita zoipa ndi amuna: 1:10
    - (9) Akuba anthu: 1:10
    - (10) Amabodza: 1:10
    - (11) Olumbira zonama: 1:10
    - (12) Ndi kena kalikonse kotsutsana ndi chiphunzitso cholamitsa: 1:10

4. Lamulo likuyenera liyanjane ndi Uthenga wabwino: 1:11

II. Ubale wa Paulo ndi Uthenga wabwino: 1:12-17

A. Kuyamika Mulungu chifukwa cha maitanidwe ake ku ntchito ya utumiki: 1:12

1. Maitanidwe ake anachokera kwa Yesu: 1:12
2. He was enabled by Jesus: 1:12
3. Anayesedwa okhulupirirka: 1:12
4. Anaikidwa mu utumiki: 1:12

B. Mmene oitanidwa amakhallira: 1:13

1. Amachita mwano: 1:13
2. Anali ozunza: 1:13
3. Anali wa ziwembu: 1:13

4. Koma analandira chifundo chifukwa anachita mosadziwa ndi mosakhulupirira: 1:13
- C. Kulongosola maitanidwe ake: 1:13-26
1. Chifukwa cha chisomo cha Mulungu: 1:13-14
  2. Kumpanga kukhala chitsanzo kwa ena: 1:15-16
- D. Chiyamiko zha Paulo chifukwa cha ubale wake ndi uthenga: 1:17
- III. Kuonanso lamulo la Timoteo: 1:18-20
- A. Kudzipereka ku lamulo: 1:18
- B. Ntchito ya Timoteo: 1:18-19
1. War a good warfare: 1:18
  2. Gwira chikhulupiriro: 1:29
  3. Khalandi chikumbumtima chabwino: 1:29-20
    - a. Chenjezo kwa amene ataya chikhulupiriro ndi chikumbumtima: 1:29
    - b. Humenayo ndi Alesandro, amene ndawapereka kwa Satana: 1:20

**Gawo Lachiwiri:**  
**Dongosolo ndi kayendetsedwe ka mpingo**  
**2:1-3:13**

- I. Pemphero: 2:1-8
- A. Ntchito ya pemphero: 2:1
- B. Chikhalidwe cha pemphero: 2:1
1. Mayamiko.
  2. Mapemphero.
  3. Mapembedzero.
  4. Kuyamika.
- C. Malire a pemphero: 2:1-2
1. Kwa anthu onse: 2:1
  2. Kwa mafumu: 2:2
  3. Kwa onse a ulamuliro: 2:2
- D. Zotsatira za mapemphero: 2:2-3
1. Moyo wachete, mtendere, mkulemekeza Mulungu ndi kulemekezeka: 2:2
  2. Ovomerezeka pamaso pa Mulungu: 2:3
- E. Lingaliro la pemphero: 2:5-7
1. Yesu Khristu Mpulumutsi: 2:5-6
  2. Chifukwa cha Mkhala pakati Uyu, Paulo sankhidwa kukhala mlaliki, mtumwi ndi mphunzitsi: 2:7
- F. Kukula kwa Pemphero: 2:8

1. Anthu onse kulikonse apemphere: 2:8
2. Akweze manja awo oyera: 2:8
3. Apemphere opanda mkwiyo ndi makani: 2:8

II. Akazi mumpingo: 2:9-15

A. Maonekedwe awo: 2:9-10

1. Zovala zawo zikhale zosakopa: 2:9
2. Akhazikike pa malingaliro ndi ntchito zabwino osati maonekedwe: 2:9-10

B. Kulambira kwawo: 2:11-12

1. Aphunzire ndi malingaliro odzichepetsa: 2:11
2. Asaphunzitse mu ulamuliro wa iwo okha (osadzitengera mphamvu kwa inu nokha. Tonse tiphunzitse mu ulamuliro wa Mulungu osati wa ife): 2:12

C. Chipulumutso chawo: Angakhale mkazi anayengedwa koyamba, koma Mesiya anabadwa kupyolera mwa mkazi: 2:13-15

III. Zomuyenereza woyang'anira: 3:1-7

- A. Akhale wopanda chilema: 3:2
- B. Mamuna wamkazi mmodzi: 3:2
- C. Wodzisunga: 3:2
- D. Wodziletsa: 3:2
- E. Wa makhalidwe abwino, aulemu: 3:2
- F. Ocheleza alendo: 3:2
- G. Wotha kuphunzitsa: 3:2
- H. Osaledera ndi vinyo: 3:3
- I. Wosakonda ndewu: 3:3
- J. Woleza mtima: 3:3
- K. Wopanda ndewu: 3:3
- L. Wosakonda chuma: 3:3
- M. Wosasilira: 3:3
- N. Wodziwa kuweruza bwini banja lake: 3:4-5
- O. Wosati wophunzira kumene: 3:6
- P. Wambiri yabwino kudera losapulumutsidwa: 3:7

IV. Zowayenereza atumiki: 3:8-13

- A. Olemekezeka: 3:8
- B. Osanena pawiri: 3:8
- C. Osaledzera ndi vinyo: 3:8
- D. Osakonda chuma: 3:8
- E. Okhala nacho chiphunzitso cholamitsa ndi chikumbumtima choyera: 3:9
- F. Wosati ophunzira kumene: 3:10

- G. Oyesebwa mkupezeka opanda chilema: 3:10
  - H. Ngati ndi wokwatira akhale woopa Mulungu: (Akazinsu akhale atumiki.) Akuyenera kukhala: 3:11
    - 1. Olemekezeka.
    - 2. Osadziyerekeza.
    - 3. Odziletsa.
    - 4. Okhulupirika mzonse
  - I. Mtumiki akhale mamuna wa mkazi mmodzi: 3:12
  - J. Oweruza bwino banja lake: 3:12
- V. Chifukwa chimene Paulo analemba kalata: Makhalidwe oyenera mu mpingo: 3:14-16

**Gawo Lachitatu:**  
**Mtumiki ndi makhalidwe ake**  
**4:1-6:21**

- I. Mtumiki ndi chiphunzitso chonyenga: 4:1-5
  - A. Ena adzataya chikhulupiriro masiku omaliza: 4:1
  - B. Zolakwa zawo: 4:1-5
    - 1. Adzisamala mizmu yosocheretsa: 4:1
    - 2. Adzisamala ziohunzitso za ziwanda: 4:1
    - 3. Olankhula zachinyengo: 4:2
    - 4. Okufa mchikumbumtima: 4:2
    - 5. Oletsa maukwati: 4:3
    - 6. Oletsa zakudya za nyama: 4:3-5
- II. Malangizo apadera kwa atumiki: 4:6-16
  - A. Kulangiza abale mu chiphunzitso cholamitsa: 4:6
  - B. Kana nkhani zopanda pache: 4:6
  - C. Khala wa Umulungu: 4:7-8
  - D. Landira zinthu zovomerezeka: 4:9
  - E. Gwira ntchito ndi kusautsika chifukwa cha Mulungu: 4:10
  - F. Lamulira ndi kuphunzitsa chiphunzitso cholamitsa: 4:11
  - G. Chinyamata chako chisapeputsidwe, koma khala chitsanzo cha okhulupirira: 4:12
    - 1. Mmawu.
    - 2. Mu zolankhula.
    - 3. Mu zachifundo.
    - 4. Mu mzimu.
    - 5. Mu chikhulupiriro.

6. Mu chiyeretso.
- H. Samalira zinthu izi: 4:13
  1. Kuwerenga.
  2. Kulimbikitsa.
  3. Chiphunzitso.
- I. Osanyozetsa mphatso imene ili mwa iwe: 4:14
- J. Lingalira ndi kukhala mu zinthu zimenezi: 4:15
- K. Udziyang'anire wekha ndi chiphunzitso: 4:16
  1. Khalabe mu chiphunzitso cholamitsa.
  2. Udzapulumuka wekha.
  3. Adzapulumuka onse adzamva iwe.

### III. Mtumiki ndi khalidwe lake kwa anthu a mumpingo: 5:1-6:10

#### A. Akulu ndi aang'ono: 5:1-2

1. Mkulu umudandaulira ngati atate: 5:1
2. Aang'ono ukhale nawo ngati abale: 5:1
3. Akazi aakulu ukhale nawo ngati amayi: 5:2
4. Akazi aang'ono ukhale nawo ngati azilongo: 5:2

#### B. Amasiye: 5:3-16

1. Chitira ulemu amene ali amasiye: 5:3
2. Udindo wa amasiye: 5:4
3. Tanthauzo la "wamasiye weniweni": 5:5-6
  - a. Wosiyidwa: 5:5
  - b. Wodalira Mulungu: 5:5
  - c. Wokangalika mmapemphero ndi mapembedzero: 5:5
  - d. Sakhala mu zokondweretsa za dziko: 5:6
4. Udindo wa achibale amasiye: 5:7-8
5. Zomuyenereza "wamasiya weniweni": 5:9-13
  - a. Chiwerengero cha iwo azipatulira kwa Mulungu: 5:9
  - b. Osati iwo amene sanafike zaka makumi asanu ndi limodzi: 5:9
  - c. Mkazi wa mamuna mmodzi: 5:9
  - d. Wa mbiri yabwino mu ntchito zabwino: 5:9

- (1) Osamalira ana ache.
- (2) Ocheleza alendo.
- (3) Osambitsa mapazi a oyera mtima.
- (4) Omasula ophinjika.
- (5) Wakhama pochita ntchito zwbwino.

#### 6. Iwo amene sayenera: Amasiye aang'ono: 5:11-15

- a. Akuyenera kulowanso m'banja: 5:11
- b. Zotsatira zake ndi kuphwanya pangano la kudzipatulira kwa Mulungu:

5:12

c. Adzayamba kuchita makhalidwe osayenera: 5:13

- (1) Osachita kanthu.
- (2) Kumayenda khomo ndi khomo.
- (3) Opokosera.
- (4) Otanganidwa.
- (5) Olankhula zinthu zimene sizigwirizana ndi mmene alili.

7. Malangizo kwa amasiye aang'ono amene sali mu gulu la amasiye aakulu omwe apatulira moyo wawo kwa Mulungu: 5:16-17

- a. Alowe m'banja: 5:16
- b. Abale ana: 5:16
- c. Asamalire nyumba: 5:16
- d. Akhale opanda chilema: 5:16
- e. Chenjezo kuti ena anakopeka ndi Satana: 5:17

C. Akuluakulu: 5:17-25

1. Lemekezani iwo akulamulira: 5:17
2. Patsani iwo amene akugwira ntchito nthawi yonse yotumikira: 5:17-18
3. Iwo amene sanatsogolere bwino: 5:19-20
  - a. Uwanenere pamaso pa mboni ziwiri kapena zitatu: 5:19
  - b. Uwadzudzule pamaso pa onse: 5:20

D. Zinthu zina: 5:21-25

1. Usafulumire kusanjika manja: 5:21
2. Osakhala ndi tsankho: 5:21
3. Osayanjana ndi machimo a anthu ena: 5:22
4. Dzisunge wekha kukhala woyera: 5:22-23
5. Zindikira kuti choweruzo chimachokera kwa Mulungu: 5:24-25
  - a. Machimo ena amaweruzidwa pano, ena kutsogolo: 5:24
  - b. Ntchito za anthu zina zionekera pano, zina kutsogolo: 5:25

E. Akapolo: 6:1-8

1. Chitirani ulemu ambuye anu: 6:1
2. Osawapeputsa ambuye amene ndi okhulupirira: 6:2

F. Amuna onse:

1. Ngati aphunzitsa zosiyana ndi chiphunzitso cha Yesu Khristu, ndiye kuti (3):
  - a. Ndi otukumuka: 6:4.
  - b. Osadziwa kanthu: 6:4
  - c. Asemphana ndi mafunso ndi makani a mawu amene zikuchokera: 6:4-5

- (1) Njiru: 6:4
- (2) Ndewu: 6:4
- (3) Zamwano: 6:4



- (4) Mayerekezo oipa: 6:4
- (5) Makani opanda pache a anthu oipsika nzeru ndi ochotseka choonadi, akuyesa kuti chipembedzo chipindulitsa: 6:5
- 2. Dzipatuleni nokha kwa amuna amtundu woterewu: 6:5
- 3. Chipembedzo chokhutira nacho ndi cha phindu lalikulu: 6:6-7
  - a. Tinalowa mdzikoli opanda kanthu: 6:7
  - b. Ndipo sitidzatenga kanthu kalikonse: 6:7
  - c. Tikwanitsidwe ngati zosowa zathu zikwanitsidwa: 6:8
- G. Chuma: 6:9-19
  - 1. Mavuto a chuma: 6:9
    - a. Amagwa mmayesero.
    - b. Amagwa mu nsampha.
    - c. Amapezeka mu zopusa ndi zilakolako zowawa.
    - d. Amagwa mchionongeko ndi mchitayiko.
  - 2. Malingaliro oipa a chuma: 6:10
    - a. Chikondi cha pa ndalama.
    - b. Kusilira kumene kumabwera kuchifukwa cha kupatukaku chikhulupiriro ndi chisoni.
  - 3. Zimene mtumiki akuyenera kuchita pa nkhani ya chuma: 6:11-19
    - a. Thawa zinthu izi: 6:11
    - b. Ndipo tsata izi: 6:11
      - (1) Chilungamo.
      - (2) Chipembedzo.
      - (3) Chikhulupiriro.
      - (4) Chikondi.
      - (5) Chipiriro.
      - (6) Chifatso.
    - c. Menya nkondo yabwino ya chikhulupiriro: 6:12
    - d. Gwira moyo wasatha: 6:12
      - (1) Umene unayitanidwira.
      - (2) Umene uli nawo mboni zochuluka.
    - e. Sunga lamulo ili: 6:13-16
      - (1) Lopanda chilema: 6:14
      - (2) Lopanda banga: 6:14
      - (3) Kufikira kubwera kwa Yesu: 6:14-16
    - f. Lamulira achuma ali pa dziko kuti: 6:17-19
      - (1) Kutu asakhale ndi malingaliro a pamwamba: 6:17
      - (2) Asakhulupirire zinthu zina koma mwa Mulungu: 6:17
      - (3) Chitani bwino: 6:18
      - (4) Khalani achuma mu ntchito zabwino: 6:18

- (5) Khalani okonzeka kupasa ena: 6:1
- (6) Funani kuyanjana: 6:18
- (7) Dzikundikireni maziko a muyaya: 6:19
- (8) Gwirani moyo osatha: 6:19

IV. Mawu otsiriza: 6:20-21

- A. Sungani chimene chaperekedwa kwa inu: 6:20
- B. Pewani zokamba zopanda pache: 6:20
- C. Pewani zotsutsana zimene ndi zooneka za mzeru zimene ena pozivomereza adalakwa  
ndi adataya chikhulupiriro: 6:21
- D. Chisomo chikhale ndi inu: 6:21

## TIMOTEO II

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**OMWE AMAWALEMBERA:** Timoteo

**CHOLINGA:** Paulo analemba bukuli ali ku ndende pofuna kumtsimikizira Timoteo kutenga udindo wa utumiki umene mtumwi amaupereka kwa iye chifukwa cha imfa yake inali pafupi. Paulo amadziwa kuti atha kuphedwa chifukwa cha chikhulupiriro chake.

**VESI LOTSOGOLERA:** II Timoteo 2:2

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Dongosolo la umulungu la kufalitsa uthenga wabwino ndiko “aliyense aphunzitse mmodzi kuti afikirensa mmodzi.”

**ANTHU OPEZEKA:** Paulo, Timoteo, Luka, Karpo, Marko, Tito, Humenayo, Onesiforo, Alesandro, Dema, Fugelo, Tukiko, Akula, Priska, Erasto, Yane, Yambre, Trofimo, Eubulo, Pude, Lino, Klaudiya.

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-2

A. Kuchokera kwa: Paulo: 1:1

1. Mtumwi.
2. Molingana ndi lonjezo la moyo limene ndi Yesu.

B. Kupita kwa: Timoteo: 1:2

1. Mwana mwa chikhulupiriro.
2. Chisomo, chifundo ndi mtendere zochokera kwa Mulungu ndi Yesu.

II. Mayamika: 1:3-5

A. Kuthokoza Mulungu: 1:3

B. Zifukwa zothokozerana: 1:3-5

1. Chikumbukiro chake cha Timoteo: 1:3
2. Khumbo lake la Timoteo: 1:4
3. Chikumbukiro chake cha kukhazikika kwa Timoteo muchikhulupiriro: 1:5

- III. Chilimbikitso pa utumiki wokhulupirika: 1:6-2:13
- A. Gwiritsa mphatso za mzimu: 1:6
- B. Khala ndi malingaliro olimbika: 1:7-8
1. Usaope: 1:7
  2. Khala ndi mzimu wamphamvu, chikondi ndi wodziletsa: 1:7
  3. Usachite manyazi ndi umboni wako: 1:8
  4. Khala omva nawo zowawa za uthenga wabwino molingana ndi mphamvu ya Mulungu: 1:8
- C. Zindikira mayitanidwe ako: 1:9-12
1. Ali wochokera kwa Mulungu: 1:9
  2. Mwa chipulumutso osati mwa ntchito: 1:9
  3. Kuti akwaniritse cholinga cha Mulungu: 1:9
  4. Mwachisomo cha Mulungu: 1:9
  5. Ndi okhazikika mwa Yesu: 1:10-11
  6. Adzabweretsa masautso: 1:12
  7. Ndi a muyaya: 1:12
- IV. Chilimbikitso ku chiphunzitso cholamitsa: 2:13-26
- A. Gwiritsitsa: 1:13-14
- B. Chifukwa cholimbikitsira: 1:15-18
1. Kupatuka ku chiphunzitso cholamitsa kwa iwo a ku m' Asiya: Fugelo ndi and Hermogene: 1:15
  2. Chifundo cha Onesiforo: 1:16-18
- C. Kutumiza chiphunzitso cholamitsa kwa ena: 2:1-2
1. Kwa iwo okhulupirika: 2:2
  2. Amene angathe kuphunzitsa ena: 2:2
- D. Kuteteza chiphunzitso monga msilikali: 2:3-4
1. Pilira mu zowawa: 2:3
  2. Osakodwa ndi zofuna za moyo uno wa dziko lapansi: 2:4
  3. Iye amene wasankha kukhala msilikali: 2:4
- E. Kufunafuna chiphunzitso ngati wochita mpikisano: 2:5
- F. Kugwirira ntchito chiphunzitso ngati mlimi: 2:6
- G. Ntchito yolabadira chiphunzitso: 2:7
- H. Kumva zowawa chifukwa cha chiphunzitso: 2:8-13
1. Mogwirizana ndi chitsanzo cha Yesu: 2:8
  2. Kumva zowawa sikuletsa chiphunzitso cholamitsa: 2:9
  3. Ngati tinafa ndi Iye, tidzakhanso ndi moyo ndi Iye: 2:10
  4. Ngati tivutika, tidzalamulira: 2:12
  5. Ngati timkana, Iyenso adzaticana: 2:12
  6. Ngati sitimkhulupirira, Iye akhalabe okhulupirika: 2:13

- I. Osalimbana ndi zinthu zopanda pache: 2:14
- J. Phunzirani chiphunzitso cholamitsa kuti: 2:15
  - 1. Uvomerezedwe ndi Mulungu.
  - 2. Usachite manyazi.
  - 3. Ulunjike nawo bwino mawu a choonadi.
- K. Koma pewa nkhani zopanda pake: 2:16-18
  - 1. Pakuti zimaonjeza chisapembedzo: 2:16
  - 2. Humenayo ndi Fileto adasochera nawo: 2:17-18
- L. Zikhazikitse wekha pa maziko owona: 2:19
  - 1. Mwa Yesu.
  - 2. Mu chilungamo.
- M. Khala chotengera cha ulemu: 2:20-21
- N. Thawa zilakolako za unyamata: 2:22
- O. Koma londola: 2:22
  - 1. Chilungamo.
  - 2. Chikhulupiriro.
  - 3. Chifundo.
  - 4. Mtendere.
  - 5. Makhalidwe a Umulumngu.
- P. Pewa mafunso opusa ndi opanda malango: 2:23-26
  - 1. Zimayambitsa ndewu: 2:23
  - 2. Mtumiki wa Mulungu sachita ndewu koma: 2:24-26
    - a. Wofatsa kwa anthu onse: 2:24
    - b. Wokwanitsa kuphunzitsa: 2:24.
    - c. Wopirira: 2:24
    - d. Wolangiza mkufatsa ndi mkulapa: 2:25-26
- V. Chilimbikitso cha masiku otsriza: 3:1-4:8
  - A. Kulengeza za zowawa zoopsa mmasiku otsiriza: 3:1
  - B. Zoipa za anthu mmasiku otsiriza: 3:2-7
    - 1. Odzikonda okha: 3:2
    - 2. Okonda ndalama: 3:2
    - 3. Odzitamandira: 3:2
    - 4. Odzikudza: 3:2
    - 5. Amwano: 3:2
    - 6. Osamvera akuwabala: 3:2
    - 7. Osayamika: 3:2
    - 8. Osayera mtima: 3:2
    - 9. Opanda chikondi cha chibadwidwe: 3:3

10. Osayanjanitsika: 3:3
  11. Akudierekeza: 3:3
  12. Osakhoza kudziletsa: 3:3
  13. Aukali: 3:3
  14. Osakonda abwino: 3:3
  15. Achiwembu: 3:4
  16. Aliuma olimbikira: 3:4
  17. Otukumuka mtima: 3:4
  18. Okonda zokonda anthu osati zokondweretsa Mulungu: 3:4
  19. Okhala nawo maonekedwe a chipembedzo koma mphamvu yake adaikana: 3:5
  20. Okwawira mnyumba nagwira akazi opusa: 3:6
  21. Osenza akatundu oipa: 3:6
  22. Otengedwa nazo zilakolako: 3:6
  23. Ophunzira nthawi zonse koma osazindikira: 3:7
- C. Monga Yane ndi Yambre ngati anthu oipa: 3:8
1. Anatsutsana ndi Mose.
  2. Anakana choonadi.
  3. Anthu ovutitsa mitima.
  4. Osatsimikizidwa pa chikhulupiro.
- D. Malire a anthu amenewa: 3:9
1. Sadzapitilira.
  2. Kupusa kwawo kudzaonekera pamaso pa anthu onse.
- E. Chizunzo cha masiku otsiriza: 3:10-12
1. Paulo ngati chitsanzo cha iwo anabadwa mmazunzo: 3:10-11
    - a. Chiphunzitso chake, moyo wake, cholinga chake chikhulupiro chake, Kuleza mtima, kukoma mtima ndi kudekha kwake anapilira mazunzo: 3:10
    - b. Mulungu anampulumutsa ku chizunzo cha ku m'Antiokeya, m'Ikoniya ndi m'Lustro: 3:11
  2. Onse ofuna kukhala moyo wopembedza adzamva zowawa: 3:12
- F. Nyengo zoipa mmasiku otsiriza: 3:13
1. Anthu oipa ndi onyenga adzaipa chiipire: 3:13
  2. Adzanyenga anthu ena: 3:13
  3. Adzanyengedwa okha: 3:14
- G. Zimene mtumiki angachite mu nyengo zoipa za masiku otsiriza: 3:14-4:5
1. Kukhalabe mu chiphunzitso cholamitsa: 3:14-15
  2. Kukhazikika mmalemba: 3:15-17
    - a. Pakuti akupatsa nzeru za kuchipulumutso mwa chikhulupiro cha Yesu: 3:15
    - b. Pakuti anauzilidwa ndi Mulungu: 3:16

- c. Ndipo ndi opindulitsa: 3:16
  - (1) Pa chiphunzitso.
  - (2) Pa chidzudzulo.
  - (3) Pa chikonzero.
  - (4) Pa chilangizo cha mchilungamo.
- d. Mau amabweretsa ungiwiro: 3:17
- e. Mawu amakonzeke retsa ntchito yabwino: 3:17
- H. Gwira chilamulo choyera: 4:1
- I. Lalikira mawu: 4:2
- J. Konzekera mu nyengo zonse: 4:2
- K. Tsutsa, dzudzula, Chenjeza ndi kuleza mtima ndi chiphunzitso: 4:2-4
  - 1. Izi ndizofunikira chifukwa ikudza nthawi imene sadzalora chiphunzitso cholamitsa: 4:3
  - 2. Adzadzifunira aphunzitsi a kumtima kwawo kuti adzawaphunzitse zimene akonda: 4:3
  - 3. Adzapatuka ku choonadi: 4:4
  - 4. Adzapatuka kutsata nthano: 4:4
- L. Khala mmaso mu zonse: 4:5
- M. Pilira mu zowawa: 4:5
- N. Gwira ntchito ya mlaliki wa uthenga wabwino: 4:5
- O. Kwaniritsa utumiki wako: 4:5

VI. Mawu otsiriza: 4:6-22

- A. Umboni wa Paulo: 4:6-8
  - 1. Ndi wokonzeka ngakhale kufa: 4:6
  - 2. Walimbana nako kulimbana kwabwino: 4:7
  - 3. Watsiriza ntchitoyo: 4:7
  - 4. Wasunga chikhulupiriro: 4:7
  - 5. Ndipo akuyembekezera kulandira mphoto: 4:8
  - 6. Ndipo palinso mphoto ya iwo anatsata chitsanzo chake: 4:8
- B. Apempha Timoteo abwere: 4:9-13
  - 1. Pempho loti abwere: 4:9
  - 2. Chifukwa chake: 4:10-12
  - 3. Malangizo pa zomwe atenge: 4:13

VII. Mayesero a Paulo: 4:14-18

- A. Zoipa zomwe adachita Alesandro: 4:14-15
- B. Paulo anayenera kuyima yekha poyamba: 4:16

- C. Koma Mulungu anayima naye mmayesero: 4:17
- D. Mulungu adzaima nayenso mmayesero akutsogolo: 4:18

VIII. Mawu otsiriza: 4:19-22

- A. Mawu otsiridza kwa Priska, Akula ndi a mnyumba ya Onesiforo: 4:19
- B. Nkhani yokhudza abwenzi a Paulo: 4:20
- C. Dandaulo lotsiliza loyitanitsa Timoteo: 4:21
- D. Moni wapadera: 4:21
- E. Nyimbo: 4:22



## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba mabuku a I ndi II Timoteo ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la I Timoteo.

---

3. Kodi buku la I Timoteo amalemba kwa yani?

---

4. TchuLani Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la I Timoteo.

---

5. Lembani Vesi lotsogolera la buku la I Timoteo kuchokera pantima.

---

6. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la II Timoteo.

---

7. Kodi buku la II Timoteo amalemba ndani?

---

8. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la II Timoteo.

---

9. Lembani vesi lotsogolera la buku la II Timoteo kuchokera pantima.

---

**(Mayankho a mafunso onsewa ali kumapeto kwa bukhu lino).**

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani mawu oti “ndikulamulira” mu I ndi II Timoteo. Ndipo ndi zinthu ziti zimene Paulo anamulamulira Timoteo kuti achite?
2. Werengani mawu oti “chikhulupiriro” amene agwiritsidwa ntchito mmabuku onse awiri. Kodi Paulo analankhula chiyani zokhudza chikhulupiriro?
3. Mabukuwa ali ndi zambiri zokhuza utumiki wa chiphunzitso. Werengani zonse zimene Paulo analemba zokhudza aphunzitsi, chiphunzitso ndi udindo wophunzitsa.
4. Werengani mawu ot “chipembedzo” mu I ndi II Timoteo. Lembani mwachidule zimene mawuwa akuphunzitsa.
5. Okhulupirira akufaniziridwa ndi zinthu zambiri mu buku la II Timoteo: Msilikali (2:3), Wothamanga (2:5), Mlimi (2:6), Wophunzira (2:15), Chotengera (2:21), ndi Mtumuki (2:24).
6. Lembani chidule ndi kawuniwuni wa utumiki wa Paulo. II Timoteo 4:6-8
7. Werengani zowayenerenza atumiki ndi akulu akulu zimene zikupezeka mu II Timoteo 3:1-13.
8. Phunzirani moyo wa Timoteo. Ndipo onjezerani zina zokhudza Timoteo mmabuku onse a I ndi II Timoteo. Werengani ndime izi:

-Machitidwe 13:5; 14:19-20; 16:1-3; 17:14; 19:22; 20:4

-I Akorinto 4:17; 9:20; 16:10

-II Akorinto 1:1,19

-I Atesalonika 3:2,6

-Afilipi 1:1; 2:19-23

-Akolose 1:1

-Filemoni 1:1

-Ahebri 13:23

## CHAPUTALA CHA 14

### TITO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Tito.
- Kudziwa amene amawalemba buku la Tito.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Tito.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Tito.
- Kutchula Moyo ndi Mfundo ya Utumiki ya buku la Tito.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**OMWE AMAWALEMBERA:** Tito, Mhelene wotembenuka mtima wogwira ntchito limodzi ndi Paulo

**CHOLINGA:** Kukonza mavuto ndi kukhazikitsa dongosolo labwino ku mipingo yopezeka pa chilumba pa Krete.

**VESI LOTSOGOLERA:** Tito 1:5

**ANTHU OPEZEKA:** Paulo, Tito, Artema, Tukiko, Apolo, Zena.

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-4

A. Kuchokera kwa Paulo: 1:1-3

1. Mtumiki wa Mulungu: 1:1
2. Mtumwi wa Khristu: 1:1-2
3. Mtumiki wochita kusankhidwa: 1:3

B. Kupita kwa Tito: 1:4

II. Cholinga: "Chifukwa cha ichi mnakusiya ku Krete": 1:5

A. Kuika zinthu mmalo mwake.

B. Kukhazikitsa ndondomeko za mpingo pansu pa Paulo.

III. Atsogoleri a mumpingo: 1:6-16

A. Zowayenereza zawo: 1:6-9:

1. Opanda banga: 1:6-7
2. Mamuna wamkazi mmodzi: 1:6
3. Osamalira banja lake mokhulupirika, ana ake omvera: 1:6
4. Woyang'anira wabwino: 1:7
5. Wosakwiya nsanga: 1:7
6. Wosaledzera naye vinyo: 1:7
7. Wopanda liuma: 1:7
8. Wosachita ndewu: 1:7
9. Wosasilira zonyasa (wosapeza ndalama mnjira zolakwika): 1:7
10. Wodziwa kuchereza alendo: 1:8
11. Wokonda anthu abwino: 1:8
12. Wodziweruza: 1:8
13. Wolungama: 1:8
14. Woyera: 1:8
15. Wodziletsa: 1:8
16. Wodziwa chiphunzitso: 1:9
17. Wodziwa mawu: 1:9

B. Kufunikira kwa kukhala ndi zowayenereza: 1:9-16

1. Kuti athe ukonza ndi kutsutsa otsutsana nawo: 1:9,13
2. Okhulupirira omwe olakwa ndi monga: 1:10-16
  - a. Osamvera: 1:10
  - b. Olankhula zopanda pake: 1:10
  - c. Onyenga: 1:10
  - d. Opasula mabanja: 1:11
  - e. Ophunzitsa chifukwa cha ndalama: 1:11
  - f. Abodza: 1:12
  - g. Zilombo zoipa: 1:12
  - h. Aumbombo: 1:12
  - i. Osakhwima mchiphunzitso: 1:13
  - j. Osamala malamulo a anthu amene amawachotsa pa choonadi: 1:14
  - k. Odetsedwa mmalingaliro ndi mchikumbumtima: 1:15
  - l. Osakhulupirira: 1:15
  - m. Ovomereza kuti adzimwa Mulungu, koma ntchito zawo zimkana Iye: 1:16
  - n. Onyasa: 1:16
  - o. Osamvera: 1:16
  - p. Osatsimikizika pa ntchito zonse zabwino: 1:16

IV. Magulu osiyana a mu mpingo: 2:1-3:2

Ichi ndi chiphunzitso chimene chikuyenera kuperekedwa kwa iwo (2:1,15)

A. Okalamba akhale: 2:2

1. Odzisunga.
2. Olemekezeka.
3. Odziletsa.
4. Olama mchikhulupiriro.
5. Achikondi.
6. Opilira.

B. Akazi okalamba akhale: 2:3-4

1. "Momwemonso": Akuyenera kukhala ndi makhalidwe ofanana ngati amuna okalamba: 2:3
2. A makhalidwe oyenera a anthu: 2:3
3. Osadzidierekeza: 2:3
4. Osakonda vinyo: 2:3
5. Ophunzitsa zokoma: 2:3
6. Olangiza akazi aang'ono: 2:4

C. Akazi aang'ono akhale: 2:4-8

1. Odzisunga: 2:4
2. Okonda amuna awo: 2:4
3. Okonda ana awo: 2:4
4. Odziletsa: 2:5
5. Odekha: 2:5
6. Osamalira bwino nyumba ywo: 2:5
7. Abwino: 2:5
8. Omvera amuna awo kuti mau a Mulungu asachitdwe mwano: 2:5

D. Anyamata: 2:6

1. "Momwemonso": Akhale ndi makhalidwe ofanana ndi akazi ang'ono: 2:6
2. Akhale odziletsa: 2:6

E. Wokhulupirira onse akhale: 2:7-8

1. Achitsanzo cha makhalidwe abwino: 2:7
2. Olama mchiphunzitso: 2:7
3. Olemekezeka: 2:7
4. Owona mtima: 2:7
5. Okhala ndi mawu olama ndi otsatsutsika: 2:8
6. Osakhala nako kanthu koyipa kowanenera: 2:8

F. Iwo akutumikira ambuye awo: 2:9-10

1. Amvere: 2:9
2. Akondweretse mbuye wawo: 2:9

3. Asakane mawu awo: 2:9
4. Asabe: 2:10
5. Awonetse chikhulupiriro chonse chabwino: 2:10
6. Akhale chitsanzo cha chikhulupiriro: 2:10

G. Okhulupirira onse: 2:11-3:2

1. Akane chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi: 2:12
2. Akhale odziletsa: 2:12
3. Akhale olungama: 2:12
4. Akhale opembedza: 2:12
5. Alindilire chiyembekezo kubwera kwa Yesu: 2:13
6. Akhale mmoyo owomboledwa: 2:14
7. Akhale mmoyo woyera: 2:14
8. Akhale molingana ndi anthu a Mulungu: 2:14
9. Amachawi pa ntchito zabwino: 2:14
10. Omvera ulamuliro: 3:1
11. Okonzeka kuchita ntchito yabwino: 3:1
12. Osalankhula zoipa za anthu ena: 3:2
13. Asakhale andewu: 3:2
14. Aulere: 3:2
15. A chifatso: 3:2

V. Malangizo oonjezera pa dongosolo la mpingo: 3:3-11

A. Kukhala ndi anthu molingana ndi mmene Mulungu anachita nanu: 3:3-7

1. Pamene kale munali: 3:3
  - a. Opusa.
  - b. Osamvera.
  - c. Onyengeka.
  - d. A kucitira ukapolo zilakolako ndi zokondweretsa za mitundu mitundu.
  - e. Okhalandi dumbo ndi njiru
  - f. Odedwa.
  - g. Odana wina ndi mnzache.
2. Koma Mulungu anakukuondani posatengera izi: 3:4-7
  - a. Munapulumsidwa mwa chisomo: 3:5
  - b. Munatsukidwa mkuyera: 3:5
  - c. Munabadwanso: 3:5
  - d. Munakonzedwa ndi Mzimu Woyera: 3:5-6
  - e. Munalungamitsidwa mwa chisomo: 3:7

f. Munapangidwa kukhala olandira cholowa cha moyo  
wosatha: 3:7

B. Khalani wabwino, wopindilitsa, ndi wofunika pa kubala chipatso: 3:8,14

C. Koma pewa izi chifukwa nzosapindulitsa ndi zopanda pake: 3:9

1. Mafunso opusa.
2. Mawerengedwe a mibadwo.
3. Ndewu.
4. Makani pa malamulo.

D. Mutamchenjeza munthu kamodzi kapena kawiri pa chiphunzitso: 3:10-11

1. Munkanize: 3:10
2. Mutadziwa kuti wasandulika: 3:11
3. Mutadziwa tchimo lake: 3:11
4. Dziwani kuti wadzitsutsa yekha: 3:11

VI. Mawu otsiriza: Malangizo ndi kupereka moni: 3:12-15

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Tito ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene analemba buku la Tito.

---

---

---

3. Kodi buku la Tito analemba kwa ndani?

---

---

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Tito.

---

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Tito kuchokera pamtima.

---

---

---

**(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa bukuli)**



## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Nkhani yokhuza ntchito zabwino yatchulidwa kwambiri mu buku la Tito. Werengani mavesiwa. Ndipo onetsani pa tchati zimene zikuphunzitsidwa zokhuza wokhulupirira ndi ntchito zabwino.

**Mavesi**

**Chidule**

2:7

2:14

3:1

3:4

3:5

3:8

3:14

2. Phunzirani zowayenereza atsogoleri a mpingo zimene zikupezeka mu buku la Tito.

3. Onani nthawi zitatu za chipulumutso mu 2:11-13:

-Kale Kubweretsa chipulumutso.

-Tsopano Kutiphunzitsa.

-Mtsogolo Keyembekedzera chiyembekezo chodala.

4. Kuti mudziwe zambiri zokhudzana ndi malo otchedwa Krete, onani I Samuele 30:14, Ezekiele 25:16, Machitidwe 2:11, ndi 27:17.

5. Dziwani ubale wa pakati pa I ndi II Timoteo ndi Tito:

I Timoteo: Teteza uthenga wabwino

II Timoteo: Lalikira uthenga wabwino

Tito: Chita molingana ndi uthenga wabwino

## CHAPUTALA CHA 15

### FILEMONI

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula amene analemba buku la Filemoni.
- Kudziwa yemwe amamulemba buku la Filemoni.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Filemoni.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Filemoni kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Filemoni.

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Paulo

**CHOLINGA:** Kudandaulira Onesimo, kapolo yemwe anathawa kwa Filemoni amene anasanduka kukhala wokhulupirira. Bukuli limaonetsa chitsanzo cha Chikhristu ku ma ubale osiyanasiyana. Limaonetsanso mfundo ya kukhululukirana, ndi utumiki wopembedzera.

**VESI LOTSOGOLERA:** Filemoni 1:10

**MOYO NDO MFUNDO YA UTUMIKI:** Mfundo za Chikhristu zikuyenera zionetedwe ku ma ubale athu osiyanasiyana.

**ANTHU OMWE ATCHULIDWAMO:** Paulo, Onesimo, Filemoni. Enanso monga Arkipo, Epafra, Dema, Luka ndi Aristarko.

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-7

A. Moni wa chisomo ndi mtendere: 1:1-3

1. Kuchokera kwa Paulo ndi Timoteo: 1:1

B. Kupita kwa: 1:1-2

1. Filemoni: 1:1

2. Apiya: 1:2

3. Arkipo: 1:2

4. Mpingo wa kunyumba kwa Filemoni: 1:2

C. Kuyamika chifukwa: 1:4-7

1. Chikondi: 1:5
2. Chikhulupiriro: 1:5
3. Chiyanjano cha chikhulupiriro: 1:6
4. Kutsitsimutsa oyera mtima: 1:7

II. Pempho: 1:8-21

A. Chidwi cha Paulo mwa Onesimo: 1:8-14

1. Anali kapolo wosapindulitsa: 1:11
2. Koma tsopano ndi wokhulupirira wopindulitsa: 1:11,13

B. Pempho la Paulo kwa Onesimo: 1:15-18

1. Mumkhululukire chifukwa cha iwe: 1:15
2. Mumkhululukire chifukwa cha iye: 1:16
3. Mumkhululukire chifukwa cha ine: 1:17-18

C. Cholinga cha pempho lake: 1:19-20

D. Kulimba mtima pa kumvera kwake: 1:21

III. Mawu otsiriza: 1:22-25

A. Paulo aganiza zochita ulendo: 1:22

B. Moni: 1:23-25

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi ndi ndani amene analemba buku la Filemoni?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la Filemoni.

---

---

---

3. Kodi buku la Filemoni amalemba kwa ndani?

---

---

4. Tchulani moyo ndi mfundoya utumiki ya buku la Filemoni.

---

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Filemoni kuchokera pamtima.

---

---

---

**(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa bukuli)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Nkhani zambrir zokhuza Filemoni zilikupezeka mu buku lalifupili. Werengani chidule cha zimene zukupezeka m'bukuli:
  - Filemoni adali bwenzi la
    - Paulo kwa Aroma: 1:2
    - Ku mpingo wa ku Kolose: 1:5,7
  - Adali munthu wachuma pokhala ndi akapolo (1:15-16) ndi zipanda zogona alendo (1:22).
  - Anakongoza moyo Paulo moyo wake: 1:9
  - Adali ndi mpingo ku nyumba kwake: 1:2
  - Adali ogwira ntchito limodzi ndi Paulo: 1:1
  - Adali ndi makhalidwe abwino a Chikristu monga:
    - Chikondi: 1:5
    - Chikhulupiriro: 1:5
    - Chiyanjano cha chikhulupiriro: 1:6
    - Kutsitsimutsa oyera mtima: 1:7
    - Kumvera: 1:21
    - Kupemphera: 1:22
  - Komanso amayendera iwo amene anali mu ndende, monga Paulo adampempha iye kuti amulankhule Epafra wandende mzake mu msinga mu mzinda: 1:23
2. Tingaphunzire zambiri zokhuza Paulo:
  - Anali wa mndende: 1:1
  - Anali munthu wa pemphero: 1:4
  - Amakhala wa chimwemwe mu nyengo zoipa: 1:7
  - Samazitenga cholanda Kamba ka maubale omwe analipo ngakhale anali nawo: 1:8-9,13-14,19
  - Amakhalabe wauzimu ngakhale mundende: 1:10
  - Anali osadzikonda: 1:13-14
  - Anali munthu wachikondi: 1:18-19
  - Anali munthu wachikhulupiriro: 1:22
  - Anali munthu amene amakonda maubale: Onesimo, Filemoni, ndi ena omwe atchulidwa mu chaputalachi.
3. Lembani mndandanda wa zinthu zimene mungaphunzire zokhuza Onesimo.

## CHAPUTALA CHA 16

### AHEBRI

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Ahebri.
- Kudziwa amene amamulemba buku la Ahebri.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Ahebri.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Ahebri.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Ahebri.

**WOLEMBA:** Paulo

**AMENE AMAWALEMBERA:** Ayuda okhulipirira

**VESI LOTSOGOLERA:** Ahebri 8:6

**MOYONDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Yesu ndi mkhalapakati wa pangano labwino lokhazikika pa malomjezano abwino.

**ANTHU AKUPEZEKAMO:** Paulo, Abrahamu, Mose, Aroni, Melikizedeki. Onaninso mayina mu Ahebri chaputala 11.

### MAGAWO

I. Ukulu wa Yesu: Yesu ndi wamkulu kuposa Angelo: 1:1-4

A. Vumbulutso cha Mulungu mwa aneneri cha Atate: 1:1

1. Nthawi zambiri.
2. Mu nyengo zambiri.

B. Vumbulutso la Mulungu mwa mwana wake: 1:2-4

1. Mulungu walankhula mwa Khristu: 1:2
2. Ulamuliro wonse wapatsidwa kwa Yesu: 1:2
3. Ntchito ya chiomboloya Yesu yakwaniritsidwa: 1:3-4

II. Mkhala pakati wamkulu: 1:3-2:18

A. Yesu ndi wamkulu kuposa Angelo: 1:3-4

1. Mwa cholowa.

2. Mwa dzina lake
- B. Ukulu wa Yesu oposa Angelo ukuonnetsedwa mu Chipango Chakale: 1:5-14
  1. Angelo: 1:5-7
  2. Mwana, Yesu Khristu: 1:8-12
  3. Angelo: 1:13-14
- C. (Koyamba) Ndime yochenjedza: 2:1-4
  1. Chenjedzo: 2:1
  2. Chitsanzo cha Chipangano Chakele: 2:2
  3. Lamulo latsopano mogwirizana ndi chenjezo: 2:3-4
- D. Ukulu wa Yesu woposa Angelo sutsutsana ndi umunthu: 2:5-8
  1. Angelo: 2:5
  2. Mwana: 2:6-8
- E. Ukulu wa Yesu woposa Angelo sutsutsana ndi masautso: 2:9-18
  1. Masautso anali wofunikira kuti analizitse kudzionetsera kwake ngati munthu: 2:9-13
  2. Masautso a kuimfa anali ofunikira kuti awononge Mdyerekezi: 2:14
  3. Masautso anali ofunikira kuti amasule anthu okhulupirira: 2:15-16
  4. Masautso anali ofunikira kuti amuyenereze Yesu ngati wansembe wamkulu wachifundo: 2:17-18

### III. Wamkulu woyambirira: Yesu ndi wamkulu woposa Mose: 3:1-4:13

- A. Yesu ndi Mose: Kusiyanitsa: 3:1-6
  1. Yesu ndi Mose anali okhulupirirka kwa Mulungu: 3:1-2
  2. Khristu anali womanga nyumba. Mose anali gawo limodzi la nyumba: 3:3-4
  3. Khristu ndi mwana wamkulu wa mnyumba. Mose anali mtumiki wa mnyumba: 3:5-6
- B. (Chachiwiri) Ndime yochenjeza: 3:7-4:13
  1. Chenjezo: 3:7-8
  2. Zimene Israyeli anakumana nazo mchipululu: 3:8-11
    - a. Malingaliro a Israyeli: 3:8-9
    - b. Mmene Mulungu anachitira: 3:10-11
  3. Chenjezo pa kusakhulupirira: 3:12-19
    - a. Chenjezo: 3:12
    - b. Zimene wokhulupirira achite pa chenjezolo: 3:13
    - c. Cholinga cha mmene achitira: 3:14
    - d. Chitsanzo cha Israyeli: 3:15-19
  4. Chenjezo pakusemphana ndi mpumulo wa Mulungu: 4:1-13
    - a. Chenjezo:

- b. Mpumulo: 4:3-5
- c. Kusowa mpumulo: 4:6-8
- d. Mpumulo wa Mulungu: 4:9-11
- e. Kutsimikiza chenjezo ndi Mawu a Mulungu ndi chidziwitso: 4:12-13

IV. Wansembe wamkulu. Yesu ndi wamkulu kuposa Aroni: 4:14-7:28

- A. Yesu ndi wamsembe wamkulu: 4:14-16
- B. Unsembe wa Aroni: 5:1-4
- C. Unsembe wa Yesu: 5:5-10
- D. (Kachitatu) Ndime yochenjeza: 5:11-6:20
  - 1. Chidzudzulo chifukwa chosakhwima muuzimu: 5:11-14
  - 2. Chilimbikitso chifukwa chokhwima muuzimu: 6:1-3
    - a. Kupita chitsogolo mopitilira maziko oyambirira: 6:1-2
      - (1) Kulapa ku ntchito zakufa: 6:1
      - (2) Chikhulupiriro mwa Mulungu: 6:1
      - (3) Chiphunzitso cha ubatizo: 6:2
      - (4) Kusanjika manja: 6:2
      - (5) Kuuka kwa akufa: 6:2
      - (6) Chiweruzo chamuyaya: 6:2
    - b. Khalanibe wangwiro: 6:1,3
  - 3. Chenjezo pa zotsatira za kukhala mu uchimo: 6:4-8
    - a. Kukhala mu chimo kulongoledwa: 6:4-6
    - b. Zotsatira zokhala mu uchimo: 6:4,6
    - c. Zifukwa za zotsatirazo: 6:6
    - d. Chitsanzo cha chilengedwe: 6:7-8
  - 4. Kukumbutsa kukhazikika kwa malonjezano a Mulungu: 6:9-20
    - a. Kukuopa: 6:9
    - b. Kukhulupirika kwa Mulungu: 6:10
    - c. Zimene okhulupirira ayenera kuchita: 6:11-12
    - d. Chitsanzo cha kukhazikika kwa malonjezano a Mulungu: 6:13-20
      - (1) Abrahamu: 6:13-15
      - (2) Lumbiro: 6:16-17
      - (3) Kutsimikizika kwa kukhulupirika kwa mawu a Mulungu: 6:18-20
- E. Unsembe wa Melikizedeki: 7:1-28
  - 1. Mnene zinalili: 7:1-3
  - 2. Melikizedeki ndi Abrahamu: 7:4-10
  - 3. Unsembe wa ku Levitiko: 7:11-13
  - 4. Unsembe watsopano: 7:14-17
  - 5. Unsembe wachilamulo: 7:18-21



6. Unsembe wachipangano chatsopano: 7:22-27
7. Chidule cha chiphunzitso: 7:28

V. Utumiki waukulu: Mapangano awiri: 8:1-10:18

A. Mawu oyamba: 8:1-6

1. Chidule cha phunziro la m'buyo: 8:1-2
2. Utumiki wa wansembe wamkulu: 8:3-5
3. Utumiki wapamwamba: 8:6

B. Mapangano awiri: 8:7-13

1. Pangano loyamba lakale: 8:7-8
2. Pangano lachiwiri latsopano: 8:8-12
  - a. Wolenga: 8:8
  - b. Pangano: 8:9-12
3. Kusiyana pakati pa chatsopano ndi chakale: 8:13

C. Magwiridwe ake ntchito a pangano chakale: 9:1-10

1. Chihema: 9:1-5
2. Utumiki wa wansemba wamkulu: 9:6-10

D. Magwiridwe ake ntchito a pangano latsopano: 9:11-10:18

1. Mmene zinzlili: 9:11-12
  - a. Chihema: 9:11
  - b. Utumiki wa wansembe wamkulu: 9:11-28
    - (1) Chochotsera machimo: 9:12-22
    - (2) Kumwamba: 9:23-28
2. Kusiyana pakati pa chakale ndi chatsopano: 10:1-18

VI. Zipangizo zazikulu za chikhulupiriro: Chidzudzulo chochitika: 10:19-13:17

A. Kukhala ndi mwayi wopita kwa Mulungu: 10:19-31

1. Kuyandikira kwa Mulungu: 10:19-22
  - a. Molimbika mtima: 10:19
  - b. Mwanjira yatsopano: 10:20
  - c. Kudzera mwa wansembe wamkulu (Yesu): 10:20-21
  - d. Ndi mtima wona: 10:22
  - e. Mu chitsimikizo chonse cha chikhulupiriro: 10:22
  - f. Ndi mitima yathu yowazidwa ndi mwazi kuchotsa chikumtima choipa: 10:22
  - g. Ndi matupi athu woyeretsedwa ndi madzi: 10:22
2. Khalani mu chikhulupiriro: 10:23
3. Limbikitsanani wina ndi nzake muchikhulupiriro: 10:24-25

- a. Tifulumizane ku chikondano ndi nchito zabwino: 10:24
- b. Musaleke kusunkhana kwanu pamodzi: 10:25
- c. Limbikitsanani wina ndi mzake: 10:25

B. (Lachianyi) Ndime yochenjeza: 10:26-31

- 1. Chenjezo: 10:26-27
- 2. Chitsanzo cha chipangano chatsopano: 10:28
- 3. Nyengo zatsopano: 10:29-31

C. Kumbukirani zimene munadutsamo kale: 10:32-34

D. Musataye chilimbikiro chanu: 10:35

E. Khalani opilira: 10:36-37

F. Khalani ndi moyo wachikhulupiro: 10:38-11:40

- 1. Lamulo lokhala ndi moyo wachikhulupiro: 10:38-39
- 2. Tanthauzo la chikhulupiro: 11:1
- 3. Ntchito ya chikhulupiro: 11:2-3
- 4. Zitsanzo za anthu achikhulupiro: 11:4-38
  - a. Abele: 11:4
  - b. Enoki: 11:5-6
  - c. Nowa: 11:7
  - d. Abrahamu and Sarai: 11:8-19
  - e. Isaki: 11:20
  - f. Yakobo: 11:21
  - g. Yosefe: 11:22
  - h. Mose: 11:23-29
  - i. Yoswa (Yeriko): 11:30
  - j. Rahabe: 11:31
  - k. Zitsanzo zina zachikhulupiro: 11:32-38

5. Olandira lonjezo la chikhulupiro mwa Yesu: 11:39-40

G. Kupilira masautso ndi chilango: 12:1-29

- 1. Zitsanzo za masautso: 12:1-3
  - a. Unyinji wa amene atizungulira (mboni): 12:1
  - b. Yesu: 12:2-3
- 2. Mmene amakhalira masautso: 12:4-11
  - a. Kukana kwa tchimo kopitilira: 12:4
  - b. Mulungu amakonda iwo amene awalanga ndipo akhala nawo ngati ana: 12:5-7
  - c. Okhawo amene sali ana salangidwa: 12:8
  - d. Kufannitsa ndi atate a dziko lapansi: 12:9-10
  - e. Zotsatira za chilango: 12:11
    - (1) Chilango cha nthawi yomweyo sichikoma.
    - (2) Kumapeto ake chimabala chipatso cha chilungamo cha mtendere.

3. Zimene okhulupirira angachite mmasautso: 12:12-17
  - a. Limbitsani manja ogooka, ndi maondo olobodoka: 12:12
  - b. Lambulani misewu yodutsamo: 12:13
  - c. Masautso onse achiritsidwe: 12:14
  - d. Londolani mtendere ndi anthu onse: 12:14
  - e. Londolani chiyero ndi anthu onse: 12:14
  - f. Yang'anitsitsani kuti wina asaperewere chisomo cha Mulungu: 12:15
  - g. Samalani kuti muzu oyipa ungabuke mkukuonongani: 12:15
  - h. Dzitsungeni kwa a chigololo ndi munthu woipa: 12:16-17

H. (Chachisanu) Ndime yochenjeza: 12:18-29

1. Mbali ya Israyeli pa phiri la Sinayi: 12:18-21
2. Mbali ya okhulupirira pa phiri la Sinayi: 12:22-24
3. Zimene okhulupirira angachite: 12:25-29

I. Chilimbikitso kuti akwaniritse udindo wakukhala Mkhristu: 13:1-17

1. Zoyenera kuchita anthu: 13:1-6
  - a. Zokhuza maubale: Chikondano chikhalebe: 13:1
  - b. Kuchereza alendo: 3:2
  - c. Kumbukirani iwo ali mumsinga ndi mmasautso: 13:3
  - d. Ukwati: Koma adama ndi achigololo Mulungu adzawaweruza: 13:4
  - e. Malankhulidwe: Musayankhule mosilira: 13:5
  - f. Chuma: Mukhutitsidwe ndi zimene mulinazo: 13:5
  - g. Kumbukirani kuti Mulungu ali nanu kuti akuthandizeni: 13:5-6
2. Zoyenera pa chipembedzo: 13:7-17
  - a. Kumbukirani iwo amene atsogolera inu: 13:7
  - b. Kumbukirani kuti Yesu sasintha: 13:8
  - c. Musatengeke ndi chiphunzitso chatsopano: 13:9
  - d. Musakodwe ndi chiphunzitso chachilamulo: 13:9-12
  - e. Musenze chitonzo chifukwa cha uthenga wabwino: 13:13
  - f. Funani mzinda umene uli mkuza: 13:14
  - g. Perekani nsembe za chiyamiko: 13:15
  - h. Chitani zokoma ndi kuyanjana: 13:16
  - i. Mverani atsogoleri anu ndi kuwagonjera: 13:17

VII. Malangizo ena: 13:18-25

A. Pempho la pemphero: 13:18-19

1. Kutu chikumbumtima ndi chokoma: 13:18
2. Kufuna kukhala ndi makhalidwe abwino: 13:18
3. Kutu kubwera kufulumize: 13:19

- B. Pemphero kwa owerenga: 13:20-21
  - 1. Amene akutchulidwa: 13:20
  - 2. Pempho: 13:21
- C. Chilimbikitso kuti asunge za mkalata: 13:22
- D. Ulendo wa Timoteo: 13:23
- E. Moni otsiriza: 13:24
  - 1. Kupita kwa: Iwo amene akukulamulirani ndi oyera mtima.
  - 2. Kuchokera kwa: Iwo aku Italiya.
- F. Nyimbo: 13:25

### **MAYESO ODZIYETSA NOKHA**

1. Kodi analemba buku la Ahebri ndi ndani?

---

2. Tchuani cholinga chimene analemba buku la Ahebri.

---

---

---

3. Kodi buku la Ahebri analemba kwa ndani?

---

---

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Ahebri.

---

---

---

5. Lembani Vesi lotsogolera la buku la Ahebri.

---

---

**(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukuli)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Buku la Ahebri limatchedwanso uthenga wachisanu. Mtaeyu, Marko, Luka ndi Yohane amakamba za ntchito za Yesu pa utumiki wake wa dziko lapansi, Imfa yake, ndi chiukitso chake. Koma Ahebri amafotokoza za ntchito ya Yesu kumwamba.
2. Mawu otsogolera powerenga buku la Ahebri ndi monga: Bwino, ungwiro, umuyaya, otenga nawo, Kumwamba, wansembe, ndi mkulu wansembe.
3. Buku la Ahebri limatuiza za kupitilira kwa mkambirano umene ndi wapakati pa Atate, Mwana, Yesu Khristu (Onani 1:5-13; 2:12-13; 10:5-9).
4. Ahebri chaputala 7-10 amalongsola za cholinga cha chihema cha chipangano chakale.
5. Ahebri chaputala 11 ndi chaputala chachikulu cha chikhulupiriro Mbaibulo.
6. Werengani Ahebri 4:12. Apa pali mfundo yofunikira kwambiri yokhuza Mawu a Mulungu opezeka Mbaibulo.
7. Werengani ma vesi awa otsimikizira ukulu wa Mesiya (Yesu) kwa Angelo: Masalmo 2:7; 104:4; 45:7-8; 102:26-28; 110:1; II Samueli 7:14; Deuteronome 32:43.
8. Werengani Ahebri 4:14-7:28. Siyanitsani unsembe wa Yesu ndi wa Aroni.
9. Werengani mapangano awiri opezeka mu Ahebri 8:1-10:18. Lembani mndandanda wa kusiyana pakati pa pangano lakale ndi pangano latsopano.
10. Pali machenjezo asanu mu kafukufuku wa mu gawo ili. Werengani machenjezowa. Ndipo muonetse mutu umene akufotokoza ndi zomwe akunena.
11. Werengani kusiyana pakati pa mbali ya Israyeli pa phiri la Sinayi ndi mbali ya okhulupirira paphiri ya Sinayi.

## CHAPUTALA CHA 17

### YAKOBO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziri ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Yakobo.
- Kudziwa kumene buku la Yakobo amalemba.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Yakobo.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku ya Yakobo.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Yakobo.

#### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yakobo

**AMENE AMAWALEMBERA:** Okhulupirira a mafuko khumi ndi awiri a Israyeli.

**CHOLINGA:** Kutonthoza Okhulupirira omwe chikhulupiriro chawo chikuyesedwa ndi masautso

**VESI LOTSOGOLERA:** Yakobo 2:26

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Chikhulupiriro ndiwo maziko a ntchito.

**ANTHU OMWE AKUPEZEKAMO:** Yakobo, Abrahamu, Isaki, Rahabe, Yobu, Eliya.

#### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1

- A. Kuchokera kwa: Yakobo, mtumiki wa Mulungu ndi Ambuye Yesu Khristu: 1:1
- B. Kupita kwa: Mafuko khumi ndi awiri obalalika: 1:1

II. Chikhulupiriro mmasautso: 1:1-18

- A. Zoyenera kuchita mmasautso: Chimwemwe: 1:2
- B. Ubwino wa masautso: 1:3-4
  - 1. Chipiriro: 1:3

2. Ungwiro: 1:4
  3. Umphuphu: 1:4
- C. Zoyenera kuchita mmasautso: 1:5
1. Kupempha nzeru kwa Mulungu: 1:5
    - a. Komwe nzeru zimachokera: kwa Mulungu.
    - b. Kupezeka kwa nzeru: Kudzera mpemphero ndi chikhulupiriro.
    - c. Kufunika kwa chikhulupiriro: Ndi anthu onse.
  2. Chikhulupiriro chokahazikaka: 1:6-7
    - a. Iye amene akayikayo ali ngati funde lotengeka ndi nyanja: 1:6
    - b. Wotereyi sadzalandira kanthu kwa Mulungu: 1:7
  3. Khalani ndi mtima umodzi: 1:8
  4. Tizichita bwino ngakhale takwezedwa kapena kutsitsidwa: 1:9-11
    - a. Mbale wapansi akondwere pamene wakwezedwa: 1:9
    - b. Mbale wapamwamba akondwere ngakhale watsitsidwa: 1:10
    - c. Pakuti milingo ya moyo imeneyo ndi yakanthawi. Zili ngati udzu ndi maluwa akuthengo amene amakula ndi kuuma kwa dzuwa: 1:10-11
- D. Madalitso pa masautso: 1:12
1. Ngati tipilira mmayesero tidzalandira kolona wamoyo, amene Ambuye analonjedza kwa iwo amkonda Iye.
- E. Kumene mayesero amachokera: 1:13-18
1. Osati kwa Mulungu: 1:13
    - a. Mulungu sayesedwa ndi choipa: 1:13
    - b. Mulungu sayetsa munthu ndi choipa: 1:13
  2. Timayedwa pamene: 1:14-15
    - a. Tikokedwa ndi chilakolako chathu ndi kunyengedwa: 1:14
    - b. Chilakolako, chikaima, chibala uchimo: 1:15
    - c. Uchimo ukaima, umabala imfa: 1:15
  3. Tikuyenera kumvetsetsa kuti: 1:16-18
    - a. Mulungu amapereka mphatso yabwino ndi yangwiro 1:17
    - b. Mulungu: 1:17-18
      - (1) Ali atate wa kuunika: 1:17
      - (2) Mwa Iye mulibe chisanduliko: 1:17
      - (3) Mwa Iye mulibe kusintha: 1:17
      - (4) Ndi Iye amene anatibala ife ndi mau a choonadi: 1:18
      - (5) Kuti tikhale ife zipatso zoundukula za chilengedwe: 1:18

### III. Chikhulupiriro cha ntchito: 1:19-4:12

- A. Chikhulupiriro chimene chimabweretsa kusintha: 1:19-21

1. Kodi tikhale otani: 1:19-20
    - a. Achangu pa kumvetsera: 1:19
    - b. Ochedwa pakulankhula: 1:19
    - c. Ochedwa pa mkwiyo: 1:19-20
  2. Kodi titaye chani: 1:21
    - a. Chinyanso chonse.
    - b. Chisefukiro choipa.
  3. Kodi tilole chani mmoyo wathu: Mawu: 1:21
- B. Chikhulupiriro pochita, osati pakumva: 1:22-25
1. Timadzinyenga tokha ngati tingomva mawu kokha: 1:22
  2. Chitsanzo cha munthu wodziyang'anira mkalilore: 1:23-25
    - a. Wokumva amangomva koma osachita kanthu: 1:23-24
    - b. Wochita amachita chimene mawu akunena: 1:25
- C. Chikhulupiriro chimaonekera pa kudziletsa kwa lilime: 1:26-27
1. Ngakhale timaoneka achipembedzo, koma ngati sitisamala lilime lathu tidzinyenga tokha ndipo kupembedza kwathu kuli chabe: 1:26
  2. Chipembedzo choyera pamaso pa Mulungu ndiko: 1:27
    - a. Kucheza ndi ana amasiye.
    - b. Kucheza ndi akazi amasiye.
    - c. Kudzisunga ku zoipa za dziko lapansi.
- D. Chikhulupiriro chilibe tsankhu kwa munthu: 2:1-13
1. Ulemu uwonetsedwe kwa onse mofanana osauka ndi olemera: 2:1-4
  2. Mulungu anasankha osauka a dziko lapansi, koma olemera mchikhulupiriro, kuti akhale cholowa mu Ufumu: 2:5
  3. Kulemekeza munthu ndi umboni wosakhala bwino pa dziki: 2:6-7
  4. Lamulo lachidumu: Uzikonda mzako monga uzikondera iwe: 2:8
  5. Kusamala maonekedwe a munthu ndi tchimo: 2:9
  6. Tchimo ndi lamulo: 2:10-13
- E. Chikhulupiriro chimene chimapulumsa: 2:14-26
1. Chikhulupiriro, chopanda ntchito, mchakufa: 2:14-17
  2. Ubale wa pakati pa chikhulupiriro ndi ntchito: 2:18
  3. Chitsanzo cha chikhulupiriro ndi ntchito: 2:20-25
    - a. Abrahamu: 2:21-24
    - b. Rahabe: 2:25
  4. Monga thupi lopanda mzimu ndi lakufa, momwenso chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa: 2:26
- F. Chikhulupiriro chimasamala lilime: 3:1-13
1. Lilime ndi chinthu chovuta kuchisamala: 3:1-2
  2. Chitsanzo cha zinthu zachilengedwe zimene timazisamala: 3:3-4
    - a. Zogwirira mkama mwa akavalo: 3:3



- b. Zombo zazikulu: 3:4
- 3. Mphamvu ya lilime: 3:5-12
  - a. Ngakhale ndi laling'ono koma lili ndi mphamvu yaikulu: 3:5
  - b. Lilime lili ngati moto limene limayaka ndi kuononga thupi lonse: 3:6
  - c. Mtundu uliwonse wa nyama umazoloweredwa ndi anthu koma lilime palibe amene angathe kulizolowera: 3:7-8
  - d. Lilime limatemberera komanso kudalitsa: 3:9
  - e. Kutemberera komanso kudalitsa kusatuluke mkamwa imodzi: 3:10-12
  - f. Kusamalira lilime ndi umboni wa chikhulupiriro ndi ntchito zabwino: 3:13
- G. Chikhulupiriro ndi magawano pakati pa okhulupirira: 3:14-4:12
  - 1. Magawano pamaso pa okhulupirira sizichokera kwa Mulungu: 3:14
  - 2. Mnzeru ya dziko: 3:15-16
    - a. Mmene imakhalira: 3:15
      - (1) Ya padziko.
      - (2) Ya chifuniro chachbadwidwe.
      - (3) Ya ziwanda.
    - b. Zotsatira zake: 3:16
      - (1) Kaduka.
      - (2) Ndewu.
      - (3) Chisokonezo.
      - (4) Zoipa zonse.
  - 3. Mzeru yochokera kwa Mulungu ili: 3:17
    - a. Yoyera.
    - b. Ya mtendere.
    - c. Yofatsa.
    - d. Yomvera bwino.
    - e. Yodzala chifundo.
    - f. Yobala chipatso.
    - g. Yopanda tsankhu.
    - h. Yopanda chinyengo.
  - 4. Chikhulupiriro chimabweretsa chilungamo ndi mtendere: 3:18
  - 5. Magawano ochokera ku zilakolako: 4:1-6
    - a. Zilakolakozi zimalempheretsa pemphero: 4:2-3
    - b. Zimalempheretsa ubale ndi Mulungu: 4:5-6
  - 6. Kukonza magawano: 4:7-12
    - a. Gonjerani Mulungu: 4:7
    - b. Kanizani mdierekezi: 4:7
    - c. Yandikirani kwa Mulungu: 4:8
    - d. Dziyeretseni nokha: 4:8
    - e. Khalani osautsidwa: 4:9

- f. Dzichepetseni nokha: 4:10
- g. Musalankhulire ena zoipa: 4:11
- h. Musaweruze ena: 4:11-12

#### IV. Chikhulupiriro ndi Tsogolo: 4:13-5:12

- A. Sitimadziwa za mtsogolo: 4:13-14
- B. Ndi Mulungu yekha amene amadziwa za mtsogolo: 4:15
- C. Tikamanyadira za mtsogolo, tikuchimwa: 4:16-17
- D. Tsogolo la olemera: 5:1-6
  - 1. Adzakumana ndi msautso: 5:1
  - 2. Chuma chidzatayika: 5:1-3
  - 3. Chinyengo chawo Mulungu akuchidziwa: 5:4
  - 4. Akhazikika mu zoipa: 5:5-6
    - a. Muzosangalatsa: 5:5
    - b. Mu njira za mumtima mwawo: 5:5
    - c. Kuweruza ndi kupha olungama: 5:6
- E. Kukonzekera tsogolo la okhulupirira: 5:7-12
  - 1. Dikirani mopilira kubwera kwa Ambuye: 5:7-8
  - 2. Khazikitsani mitima yanu: 5:8
  - 3. Osasunga mangawa: 5:9
  - 4. Onani aneneri ngati chitsanzo cha masautso anu: 5:10
  - 5. Pilirani mwa chimwemwe monga Yobu: 5:11
  - 6. Osalumbira koma chitani zimene mukunena: 5:12

#### V. Chikhulupirirondi maubale a Chikhristu: 5:13-20

- A. Zimene angachite osautsika: 5:13
- B. Zimene angachite omwe akusangalala: 5:13
- C. Zimene angachite odwala: 5:14-15
  - 1. Itanani akulu ampingo: 5:14
  - 2. Akudzodzeni ndi kukupemphererani: 5:14
  - 3. Pemphero la chikhulupiriro lidzachiritsa odwala: 5:15
  - 4. Ambuye adzamukitsa: 5:15
  - 5. Ngati anachimwa adzakhululukidwa: 5:15
- D. Zimene tingachite tikalakwirana: 5:16-18
  - 1. Vomerezani zolakwa zanu kwa wina ndi mzake: 5:16
  - 2. Pemphereranani wina ndi mzake kuti muchiritsidwe: 5:16
  - 3. Eliya ngati chitsanzo cha munthu amene anapemphera: 5:16-18
- E. Zimene tingachite kwa olakwa: 5:19-20

1. Mbwezeni: 5:19
2. Pulumutsani moyo wake ku imfa: 5:20
3. Kwirirani unyinji wake wamachimo: 5:21

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Yakobo ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la Yakobo.

---

---

---

3. Kodi buku la Yakobo amalemba ndani?

---

---

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Yakobo.

---

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Yakobo kuchokera pamtima.

---

---

---

**(Mayankho amafunso awa ali kumapeto kwa buku limeneli)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Buku la Yakobo ndi buku lokhalo mu chipangano chatsopano limene limakamba za mafuko khumi ndi awiri a ana a Israyeli: 1:1
2. Yakobo anagwiritsa ntchito mayina angapo a mchipango chakale polemba uthenga wake:

-Abrahamu: 2:21 Rahabe: 2:25 Eliya: 5:17  
-Isaki: 2:21 Yobu: 5:1

3. Yakobo anagwiritsa ntchito zitsanzo za chilengedwe polemba uthenga wake:
  - Mafunde otengedwa ndi mphepo ya nyanja: 1:6
  - Udzu wouma ndi maluwa oluluka: 1:10-11
  - Moto: 3:5
  - Kasupe wa madzi: 3:11
  - Mkuyu ndi Azitona: 3:12
  - Kufetsa ndi kututa: 3:18
  - Mvula yachangu ndi yochedwa: 5:7
  - Chilala: 5:17
4. Onani kubwerezadwa kwa mwu awa: “Chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa” mu 2:17,20,26.
5. Mwa mavesi onse 108 omwe ali mu buku La Yakobo, ndi mavesi 60 amene amakamba za malamulo moyo wa Chikhristu. Onanindi kuwerenga zimenezi.

6. Werengani moyo wa Yakobo, amene ndi m'bale wake wa Yesu amene analemba kalatayi. Onani mawu awa:

-Mateyu 12:46-50  
-Yohane 2:12; 7:1-9  
-Machitdwe 1:14; 12:17; 15:13; 21:18-26  
-I Akorinto 15:7  
-Agalatiya 1:18-19; 2:1, 9-10

7. Ziphunzitso za buku la Yakobo zimafanana ndi chiphunzitso cha paphiri cha Yesu. Malizitsani tchali ili:

### **Chiphunzitso cha pa phiri Yakobo Chidule cha Chiphunzitso**

Mateyu 5:48                      1:4

Mateyu 7:7	1:5
Marko 11:23	1:6
Mateyu 7:24,26	1:22
Yohane13:17	1:25
Luka 6:20	2:5
Luka 6:24-25	5:1
Mateyu 7:1	4:11-12
Mateyu 5:34-37	5:12
Mateyu 7:16-20	3:12

8. Fananitsani mitundu iwiri ya mzeru imene ikupezeka mu Yakobo 3:13-18:

**Mzeru ya kumwamba**

**Mzeru yosachokera kumwamba**

## CHAPUTALA CHA 18

### I NDI II PETRO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba mabuku a I ndi II Petro.
- Kudziwa omwe amawalemba mabuku a I ndi II Petro.
- Kutchula cholinga chimene amalemba mabuku a I ndi II Petro.
- Kulemba mavesi lotsogolera a mabuku onse a I ndi II Petro.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku lililonse.

### I PETRO

#### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Petro

**ANTHU OMWE AMAWALEMBERA:** A ku ukapolo omwe amazunidwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo

**CHOLINGA:** Kuchenjeza za chizunzo chimene chimachokera kunja kwa mpingo.

**VESI LOTSOGOLERA:** I Petro 4:12-13

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Zimene tingachite pozunzika Kamba ka chikhulupiriro chathu zigwirizane ndi malemba.

**ANTHU OMWE AKUPEZEKAMO:** Petro, Silvano, Maka

### MAGAWO

I. Moni: 1:1-2

A. Kuchokera kwa Petro, mtumwi wa Yesu: 1:1

B. Kupita kwa amene anabalalikana ku: 1:1

1. Ponto.
2. Galatiya.
3. Kapadokiya.
4. Asiya

## 5. Bituniya

### II. Chithonhozo ndi chitsimikizo mu masautso: 1:3-25

#### A. Chitsimikizo mu zoonadi za uthenga wabwino: 1:3-12

1. Gwero la chipulumutso: 1:3
  - a. Osankhidwa ndi Mulungu.
  - b. Owomboledwa ndi Ambuye Yesu.
  - c. Osambitsidwa ndi Mzimu.
2. Mmene chipulumutso chilili: 1:3-5
  - a. Moyo wa chiyembeko: 1:3
  - b. Cholowa chosaonongeka: 1:4
  - c. Chosadetsedwa: 1:4
  - d. Chosafota koma chamuyaya: 1:4
  - e. Chosungidwira kumwamba kwa iwo amene atetezedwa ndi mphamvu ya Mulungu mwa chikhululuiriro cha chipulumutso: 1:5

#### B. Chitsimikizo cha ubwino wa masautso: 1:6-12

1. Chimwemwe mkatikati mwa mayesero: 1:6
2. Mayamiko, ulemu ndi ulemerero: 1:7
3. Chimwemwe chifukwa cha ubale wa Yesu, osati pa zinthu zooneka za moyo: 1:8
4. Chitsimikizo cha chikhulupiriro: Chipulumutso cha moyo: 1:9-12
  - a. Ofunidwa ndi aneneri: 1:9-10
  - b. Gwero lawo: Khristu: 1:11
  - c. Chidule chawo: 1:11-12
    - (1) Adaloseza za kubwera kwake kwachiwiri ndi mazunzo: 1:11
    - (2) Adaloseza za kubweranso kwake kwachiwiri ndi ulemerero: 1:11
  - d. Ofunidwa ndi Angelo: 1:12

#### C. Chitsimikizo pa zimene adachita mmasautso: 1:14-17

1. Dzimangireni mchiuno mwanu za mtima wanu: 1:13
2. Khalani odziletsa: 1:13
3. Muziyembekeza chisomo chakukutengerani ku vumbulutso la Khristu: 1:13
4. Chitani ngati ana omvera: 1:14
5. Musadzifanidzire nokha ku zilakolako zakale: 1:14
6. Khalani oyera monga anakuitanani ali oyera: 1:15-16
7. Khalani aulemu ndi ochitachita: 1:17

#### D. Chitsimikizo pa chiombolo: 1:18-25

1. Sitinaomboledwe ndi zinthu zovunda: 1:18
2. Tinaomboledwa ndi mwazi wa Yesu wamtengo wapatali: 1:19-20
3. Chitsimikizo mu nthawi ya mazunzo chifukwa cha chiombolo ndi ubale wathu: 1:21-23



4. Chitsimikizo cha chiombolo chifukwa cha mawu amene ndi amuyaya ndipo ndi gwero la uthenga wathu wabwino: 1:24-25

### III. Zimene a Khristu angachite mmasautso: 2:1-3:13

- A. Ku uchimo: 2:1
- B. Ku mau a Mulungu: 2:2
- C. Kwa Mwana wa Mulungu: 2:3-10
- D. Kwa ife tokha: 2:11
- E. Kwa osapulumsidwa: 2:12
- F. Kwa atsogoleri adziko: 2:13-17
- G. Kwa olemba ntchito: 2:18-20
- H. Pa chitsanzo cha Khristu: 2:21-25
- I. Ku banja: 3:1-12
  1. Mkazi: 3:1-6
  2. Mamuna: 3:7
  3. Banja lonse: 3:8-12

### IV. Mwambo wa pa masautso: 3:13-4:19.

- A. Mazunzo chifukwa cha chilungamo amabweretsa chimwemwe ndi chikumbumtima chabwino: 3:13-17
- B. Mazunzo amalungamitsa ochimwa: 3:18-22
- C. Mazunzo amatifanizira ndi Yesu: 4:1-6
- D. Mazunzo amabweretsa chiyembekezo cha kubweranso kwa Ambuye: 4:7
- E. Mazunzo amaumba moyo wa uzimu: 4:8-11
  1. Chikondi: 4:8
  2. Chikhupiro cha machimo: 4:8
  3. Kuchereza wina ndi mzake: 4:9
  4. Kukhala adindo abwino a mphoto ndi utumiki: 4:10-11
- F. Mazunzo amachulukitsa mphoto yamtsogolo: 4:12-13
- G. Mazunzo amalemekeza Ambuye: 4:14-16
- H. Mazunzo amayeretsa oyera mtima: 4:17-19.

### V. Mawu achidule okhuza malingaliro a okhulupirira ku mazunzo: 4:19.

### VI. Pitilirani kutumikira, ngakhale mu masautso: 5:1-9

- A. Kutumikira ngati m'busa: Akuluakulu a mpingo: 5:1-4
  1. Dyetsani nkhoa za Mulungu: 5:2

2. Wetani gulu la Mulungu limene lili mwa inu osati mokakamiza: 5:2
  3. Osatumikira pofuna phindu la ndalama lonyasa: 5:2
  4. Khalani okonzeka mmaganizo: 5:2
  5. Khalani zitsanzo, osachita ufumu pa nkhusa: 5:3
  6. M'busa wamkulu wopereka mphoto: 5:4
- B. Tumikirani ngati atumiki: Kaya mwana kapena mkulu: 5:5-7
1. Mwana agonjere kwa akulu: 5:5
  2. Aliyense agonjere kwa mzake: 5:5
  3. Dzichepetseni: 5:5-6
    - a. Mulungu akaniza odzikweza koma apatsa chisomo kwa odzichepetsa: 5:5
    - b. Ngati tizchepetsa, tidzakwezedwa: 5:6
  4. Tayani nkhusa zanu pa Iye, chifukwa asamalira inu: 5:7
- C. Kutumikira ngati msikikali: 5:8-9
1. Mdani: Mdierekezi, ngati mkango wobuma, afuna wina amilikwire: 5:8
  2. Malingaliro a msikikali: 5:8
    - a. Tikhale odzisunga: 5:8
    - b. Khalani odikira: 5:8
  3. Njira zolimbana ndi mdani: 5:9
    - a. Timkanize mchikhulupiriro: 5:9
    - b. Podziwa kuti sitili tokha: Zowawazi zomwezinso abale ena akukumana nazo mdziko: 5:9

## VII. Mawu otsiriza: 5:10-14

### A. Nyimbo: 5:10-11

1. Phindu la masautso a Yesu. You will be: 5:10
  - a. Kupanda chilema.
  - b. Kukhazikika.
  - c. Upatsidwa mphamvu.
  - d. Kulimbikitsidwa.
2. Kwa Mulungu kukhale ulemerero ndi mphamvu: 5:11

### B. Kupereka moni kwa anthu: 5:12-14

1. Silvano: 5:12
2. Mpingo wa ku Babulo: 5:13
3. Marko mwana wanga: 5:13
4. Lankhulani wina ndi mzake ndi chipsompono: 5:14
5. Mdalitso ndi mtendere kwa iwo amene ali mwa Yesu: 5:14

## II PETRO

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Petro

**OMWE AMAWALEMBERA:** A Khristu a ku ukapolo, ofanana ndi omwe ali mu buku loyamba la I Petro.

**CHOLINGA:** Kuchenjeza zoopsa zochokera mkati mwa mpingo: Uchimo ndi ziphunzitso zonyenga

**VESI LOTSOGOLERA:** II Petro 3:1-2

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Zoopsa ziwiri zazikulu zochokera mkati mwa mpingo ndizo uchimo ndi aphunzitsi onyenga.

**ANTHU OMWE AKUPEZEKAMO:** Petulo, Paulo

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: 1:1-2

- A. Kuchokera kwa Petro, mtumiki wa Mulungu: 1:1
- B. Kupita kwa iwo amene apeza chikhulupiriro cha mtengo wapatali: 1:1
- C. Chisomo ndi mtendere zichuluke chifukwa cha chidziwitso cha Mulungu ndi Yesu: 1:2

II. Kulalikira mphamvu ya Mulungu pakati pa uchimo ndi aphunzitsi onyenga: 1:3

III. Malonjezo a Mulungu: 1:4

- A. Moyo.
- B. Chipembedzo.
- C. Chidziwitso.
- D. Ulemerero.
- E. Makhaliidwe abwino.

IV. Mfundo za Mulungu: 1:5-9

- A. Zikhazikitsidwe ndi khama: 1:5

B. Mfundo zake monga: 1:5-7

1. Chikhulupiro: 1:5
2. Ukoma: 1:5
3. Chidziwitso: 1:5
4. Kudzilesa: 1:6
5. Chipiliro: 1:6
6. Chipembedzo: 1:6
7. Chikondi cha pa abale: 1:7
8. Chikondi: 1:7

C. Kufunika kwa mfundo zimenezi. Zizakupanga iwe kukhala: 1:8

1. Ochuluka kuuzimu.
2. Obala chipatso ku chidziwitso cha Yesu.

D. Mavuto obwera Kamba kosowa mfundozi: 1:9

1. Kusowa masomphenya a uzimu.
2. Kusowa malingaliro a uzimu.

V. Maitanidwe a Mulungu: 1:10-12

- A. Khalani achangu kuti muwakhazikitse: 1:10
- B. Mukachita zimenezi simuzalephera: 1:10
- C. Muzatsimikizika kulowa mu ufumu wamuyaya: 1:11
- D. Muzakhazikika pa choonadi: 1:12

VI. Bvumbulutso kwa mtumwi wa Mulungu: Amene “adzachotsa msasa wa dziko lapanso”: 1:13-15

VII. Mawu a Mulungu: 1:16-21

- A. Sanakhazikike pa miyambo koma pa iwo amene anauona Iye: 1:16
- B. Okhazikika pa Umulungu wa Yesu Khristu: 1:17
- C. Okhazikika pa Mawu a chinenero: 1:19.
- D. Osati pa matanthauzo a anthu: 1:20
- E. Okhazikika pa kuuzila kwa Mzimu Woyera: 1:21

VIII. Chenjezo pa za aphunzitsi onyenga: Omwe apatuka pa mfundo zili mmwambazi (Mfundo II mpaka VII) ndi adani a Mulungu: 2:1-3:4

- A. Chizindikiro cha adani: 2:1-9
  1. Masiku alero: Aphunzitsi onyenga: 2:1-3
  2. Masiku akale: 2:1-9

- a. Aneneri onyenga: 2:1
  - b. Angelo oyipa: 2:4
  - c. Amene amakhala mu nthawi ya Nowa: 2:5
  - d. Amene amakhala mu nthawi ya Loti: 2:6-9
- B. Zokhudza adani a Mulungu (aphunzitsi onyenga): 2:1-3,10-19.
- 1. Adzadzitengera okha chitayiko pa chiphunzitso chawo: 2:1
  - 2. Amkana Ambuye: 2:1
  - 3. Adzatsata njira zonyasa: 2:2
  - 4. Adzapangitsa njira ya choonadi ilankhulidwe zamwano: 2:2
  - 5. Adzakhala osilira mmawu onyenga: 2:3
  - 6. Adzalankhula ndi mawu onyenga: 2:3
  - 7. Adzachita malonda ndi anthu a Mulungu: 2:3
  - 8. Adzachita malingana ndi zilakolako zonyasa: 2:10
  - 9. Adzapeputsa chilamulo: 2:10
  - 10. Adzakhala osaopa kanthu: 2:10
  - 11. Otsata chifuniro cha iwo eni: 2:10
  - 12. Adzalankhula za mwano kwa akulu: 2:10-13
    - a. Adzakana kuti ngakhale Angelo sanachita: 2:11
    - b. Amalankhula za zoipa zimene sadzidziwa: 2:12
    - c. Chifukwa cha ichi, adzawonongeka mu chivundi chawo ndipo adzalandira mphoto ya chosalungama: 2:12-13
  - 13. Amawanga ndi zilema: 2:13
  - 14. Achinyengo mu chiyanjano: 2:13
  - 15. A maso a chigololo: 2:14
  - 16. Osasiya uchimo: 2:14
  - 17. Onyengerera iwo amene ndi a moyo wosakhazikika: 2:14
  - 18. khumbo lonyasa: 2:14
  - 19. A ana otembereredwa: 2:14
  - 20. Oyiwala kuchita bwino monga anachitira Balamu: 2:15-16
  - 21. Zitsime zopanda madzi: 2:17
  - 22. Mitamboyokankhika ndi mkhutho: 2:17
  - 23. Mdimamwamuyaya ukuwasungikira: 2:17
  - 24. Alankhula mawu otukumuka opanda pake: 2:18
  - 25. Anyengerera pa zilakolako za thupi, ndi zonyansa, iwo amene adayamba kupulumukira a mayendedwe olakwawo: 2:18
  - 26. Amalonjeza ufulu ngakhale iwo ali mu ukapolo wa chivundi: 2:19.
- C. Tsogolo lawo la adaniwo: 2:20-22
- 1. Chitsiliziro chawo chidzaipa kuposa chiyambi: 2:20
  - 2. Zikanakhala bwino kwa iwo osadziwa cholungama kusiyana ndi kuchidziwa kenako mkupatuka: 2:21

3. Zili ngati galu wabwerera ku masanzo ake omwe ndi nkhumba yabwerera kukunkhulira m'thope: 2:22

IX. Chenjezo pa za nyengo ya uchimo: 3:1-18

A. Tanthauzo la nyengo uchimo: 3:1-4

1. Nthawi ya nyengo ya uchimo inaneneredwa ndi aneneri: 3:1-2
2. Uku ndi kunyoza lonjezano la kubera kwa Ambuye: 3:4

B. Yankho ku uchimo: Mulungu amatsogolera zakale, zatsopano ndi zakale: 3:5-13

1. Chiweruza pa dziko lakale chinadza ngakhale kunalo onyoza: 3:5-6
2. Chiweruzo cha mtsogolo pa dziko latsopano chidzabwera: 3:7-8,10
3. Mulungu ali ndi nthawi yake imene amachitira zinthu: 3:8
4. Chofunikira mu dongosolo la Mulungu ndi Chipulumutso kwa miyoyo yotaika, osati nthawi ya kukwaniritsidwa kwa zinthu za mtsogolo: 3:9
5. “Tsiku la Ambuye” limene lili mu dongosolo lake lidzafika mosayembekezera: 5:10
6. Dongosolo lake lidzafika ndi dziko latsopano: 3:13

C. Zimene okhulupirira angachite mu nyengo za uchimo: 3:14-18

1. Kupezedwa ndi Iye mumtendere: 3:14
2. Opanda banga: 3:14
3. Opanda zilema: 3:14
4. Kuzindikira kuti kuchedwa kukwaniritsa lonjezo la kubwera kwake ndi kuwonetsa chifundo kwa osapulumsidwa: 15-16
5. Chenjerani kuti mungatengedwe ndi kulakwa kwa iwo osaweruzika: 3:17
6. Kulani mu chisomo: 3:18
7. Kulani muchidziwitso cha Ambuye: 3:18

XI. Mawu otsiriza: 3:18

## MAYESO ODZIYETSA NOKHA

1. Kodi analemba mabuku a I ndi II Petro ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la I Petro.

---

3. Kodi buku la I Petro amalemba kwa ndani?

---

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la I Petro.

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la I Petro kuchokera pantima.

---

6. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la II Petro.

---

7. Kodi buku la II Petro amalemba kwa ndani?

---

8. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la II Petro.

---

9. Lembani vesi lotsogolera la buku la II Petro kuchokera pantima.

---

**(Mayanko amafunsowa ali kumapeto kwa bukuli)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani I ndi II Petro, ndipo lembani chilichonse chimene akuchinena kuti ndi chamtengo wapatali.
2. Werengani I Petro ndipo dulani mzere kungsi kwa mawu monga masautso ndo chisomo. Mawu awa ndi otsogolera.
3. Mu buku la I Petro okhulupirira akudziwika ndi mayina osiyanasiyana. Werengani mayinawa mundime zotsatirazi: 1:14; 2:2; 2:5; 2:9 (mayina anayi osiyana); 2:11; 4:16; 4:18; 1:2; 2:10; 4:11; 5:2.
4. Werengani moyo wa Petro mu mabuku a mauthenga ndi buku la Machitidwe.
5. Onani makhalidwe eni eni a moyo wa chikhristu:  
-Chiyembekezo cha moyo 1:3 -Mawu amoyo 1:23 -Mwala wamoyo 2:4
6. Mawu ena opezeka Muchipangano chatsopano agwiritsidwanso mu I Petro. Fananitsani awa:

### **Amene akupezeka mu chipangano chakale**

Yesaya 28:16

Masalmo 118:22

Yesaya 8:14

### **Amene akupezeka mu I Petro**

I Petro 1:6

I Petro 1:7

I Petro 1:8

7. Werengani I Petro 2:9-10. Fananitsani moyo wa okhulupirira mmene analili asanapulumsidwe ndi atapulumutsidwa.

### **Asanapulumsidwe**

### **Atapulumutsidwa**

Kutuluka ku\_\_\_\_\_ Kulowa mu ku\_\_\_\_\_

Sitinali \_\_\_\_\_ Koma pano tili\_\_\_\_\_

Tinalibe\_\_\_\_\_ Pano tili\_\_\_\_\_

8. Kuchokera mu buku la II Petro, lembani mndandanda wa chikhalidwe cha anthu osapembedza kapena aphunzitsi onyenga. Sungani mndandandawu ndipo mufanizire ndi umene ukupezeka mu buku la Yuda.



9. Kuchokera mu buku la II Petro 1:5-10, lembani makhalidwe amene okhulupirira ayenera kuonjezera ku moyo wawo.
10. Fananitsani pakati pa tsiku la Ambuye (II Petro 3:10) ndi tsiku la chiweruzo (II Petro 3:7)

## CHAPUTALA CHA 19

### I, II, NDI III YOHANE

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba mabuku a I, II ndi III Yohane.
- Kudziwa komwe buku lililonse amalemba.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku lililonse.
- Kulemba vesi lotsogolera la buku lililonse kuchokera pamtima.
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya mabuku onse.

#### CHITHUNZITHUNZI CHABE

Mu chaputala ichi, muphunzira mabuku atatu: I, II ndi III Yohane. Mabuku onsewa analembedwa ndi Yohane mwana wa Zebedayo (Mateyu 4:21) amene anali mtumwi wa Yesu (Mateyu 10:2). Yohaneyi ndi amenenso analemba buku la uthenga wabwino wa Yohane ndi buku la Chibvumbulutso. Mwaphunzira kale uthenga wa Yohane. Pomwe buku la Chibvumbulutso muliphunzira komalizira mu maphunzirowa. Mabuku amene analembedwa ndi Yohane amalowerana mu dongosolo lofuna kuchulukitsa vumbulutso.

#### MABUKU OLEMBEDWA NDI YOHANE

##### Uthenga wa Yohane

Amalankhula za chipulumutso

Amakamba za kale

Amamuonetsera Yesu ngati Mneneri

Amakamba za mtanda mu moyo wa okhulupirira

##### Makalata a Yohane

Amalankhula za chiyeretso

Amakamba zatsopano

Amamuonetsera Yesu ngati wansembe

Amakamba za chiyanjano cha okhulupirira

##### Chibvumbulutso

Amalankhula za ulemerero

Amakamba za mtsogolo

Amamuonetsera Yesu ngati Mfumu

Amakamba za kolona amene okhulupirira adzavekedwa<sup>1</sup>

---

<sup>1</sup> Dziwani: Mabuku a II ndi III Yohane alibe magawo a machaputala mu Baibulo. Choncho, ndi vesi okha amene akupezekamo.

## **I YOHANE MAWU OYAMBA**

**WOLEMBA:** Yohane

**KOMWE AMALEMBERA:** A Khristu amene amagwa mumsampha wa chinyengo cha Satana chimene chimaononga ubale wawo ndi Mulungu komanso ndi okhulupirira ena.

**CHOLINGA:** Kulongosola muyeso wa chiyanjano chenicheni ndi Yesu Khristu.

**VESI LOTSOGOLERA:** I Yohane 1:8-9

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Chiyanjano chenicheni ndi Mulungu ndi okhulupirira ena chakhazikika pa Mawu a Mulungu ndipo chimasungika ndi mfundo za kuvomereza machimo.

**ANTHU OMWE ATCHULIDWAMO:** Wolembe, Yohane. Palibenso ena atchulidwamo mayina.

### **MAGAWO**

I. Mawu oyamba: 1:1-4

- A. Yohane akulemba za zinthu zimene anaona ndi maso ake, zimene anazipenya, ndipo chimene anachigwira ndiwo mawu a moyo. Akulemba za zinthu zimene anakumana nazo: 1:1
- B. Chiyanjano cha chimene analemba ndi chiyanjano chenicheni cha okhulupirira ndi Mulungu komanso wina ndi mnzake: 1:2-3
- C. Cholinga chimene amalemba pa mutu uwu ndi chakuti chimwemwe chawo chikwanire pa kukhazikika mu chiyanjano: 1:4

II. Mmene chiyanjano chilili mwa Yesu Khristu: 1:5-10

- A. Kufanana ndi muyeso wa mawu Mulungu: 1:5-7
- B. Chivomerezo cha machimo: 1:8-10

III. Khalidweloyenera la chiyanjano chenicheni cha okhulupirira: 2:1-29

- A. Chikhalidwe cha khalidwe loyenera ndiko kutsatira moyo wa uzimu umene adawuonetsera Yesu Khristu: 2:1-11

1. Mfundo ya kutsatira: 2:1-2
  2. Dongosolo la kutsatira: 2:3-6
  3. Chitsimikizo cha kutsatira koyenera: 2:7-11
- B. Lamulo la khalidwe ndiko kusiyana: 2:12-17
1. Lamulo likuperekedwa kwa okhulupirira amene kukula kwawo mu uzimu kuli kosiyana: 2:12-14
  2. Lamuloli ndi kusiyana ndi dziko lapansi: 2:15-17
- C. Chikhulupiriro cha makhalidwe anthu: 2:18-29
1. Kufunika kwa chikhulupiriro: 2:18-21
  2. Chikhalidwe cha chikhulupiriro: 2:22-29
- IV. Makhalidwe enieni a chiyanjano cha Akhristu: 3:1-24
- A. Chiyero: 3:1-3
  - B. Chilungamo ndi chikondi: 3:4-18
  - C. Kulimba mtima: 3:19-21
  - D. Kumvera: 3:22-24
- V. Adani a chiyanjano cha okhulupirira: 4:1-21
- A. Aneneri onyenga: 4:1-6
    1. Mmene tingawadziwire: 4:2-3
    2. Mmene tingawagonjetseni: 4:4
    3. Ndi a dziko lapansi: 4:5
    4. Ife ndi ake a Mulungu: 4:6
  - B. Chivomerezo chonyenga cha mzimu wa chikondi: 4:7-21
    1. Za chikondi cha ngwiro: 4:7-17
    2. Chikondi cha ngwiro chimasiyana ndi chivomerezo chonyenga cha mzimu wa chikondi: 4:18-21
- VI. Chifukwa chosungira chiyanjano chenicheni: 5:1-21
- A. Chikhulupiriro mwa Yesu chimaonekera mu makhalidwe amene tikuonetsa: 5:1-5
  - B. Chkhulupiriro mwa Yesu chimaonekera mmaudindo amene tikuonetsa: 5:6-12
    1. Umboni wa zimene tikuonetsa: 5:6-8
    2. Zotsatira za zimene tikuonetsa: 5:9-12
  - C. Chikhulupiriro mwa Yesu chimaonera mu kulimbika mtima kwathu: 5:13-15
  - D. Chikhulupiriro mwa Yesu chimaonekera pa kugonjetsa tchimo: 5:16-21

## II YOHANE

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yohane

**OMWE AMAWALEMBERA:** “Mkazi wosankhidwa ndi ana ake” kutanthauza kuti mpingo ndi ziwalo zake (mpingo nthawi zonse umadziwika ndi dzina la mkazi chifukwa umatchedwa mkwatibwi wa Yesu.

**CHOLINGA:** Kulimbikisa okhulupirira kuti akhale okhulupirika ku chiphunzitso

**VESI LOTSOGOLERA:** II Yohane 1: 9

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Tikuyenera kudziyang’anira tokha kwa aphunzitsi onyenga amene amatichotsera makhalidwe athu a uzimu amene tilinawo ndi kutipanga kukhala ochita zoipa.

**MUNTHU YEMWE AKUTCHULIDWAMO:** Yohane

### MAGAWO

I. Mawu oyamba: Moni: 1-3

- A. Kuchokera kwa: Wamkulu, Yohane: 1
- B. Kupita kwa: Mkazi osankhidwa ndi ana ake amene Yohane anawakonda mchoonadi: 1-2
- C. Watumiza kuchokera kwa Atate Mulungu ndi Mwana: 3
  - 1. Chisomo.
  - 2. Chifundo.
  - 3. Mtendere.

II. Chilimbikitso pa chikondi: 4-6

- A. Yendani mu choonadi: 4
- B. Yendani mu chikondi: 5
- C. Yendani mu malamulo ake: 6

III. Chenjezo pa ziphunzitso zonyenga ndi aneneri onyenga: 7-11

- A. Chivomerezo cha aphunzitsi oyenga: 7
- B. Kuipa kokhulupirira aphunzitsi onyenga: 8-9
  - 1. Umataya makhalidwe a uzimu amene udawapeza poyamba: 8
  - 2. Kuchimwa pakulephera kukhala mu chiphunzitso cha Yesu: 9
  - 3. Umachita nawo ntchito zawo zoipa: 10-11

IV. Mawu otsiriza: 12-13

- A. Yohane anali ndi chikondi chachikulu powalembera ndipo amayembekezera kuwayendera: 12
- B. Yohane akutumiza moni kuchokera ku ziwalo za mpingo oyandikana nawo: 13

### **III YOHANE**

#### **MAWU OYAMBA**

**WOLEMBA:** Yohane

**OMWE AMAWALEMBERA:** Bukuli amalembera kwa munthu wotchedwa Gayo. Amalemberanso osati kwa mpingo umene iye amasonkhana. Panalibe chifukwa chomudziwa munthuyi kuti anali ndani, pakuti ngakhale Baibulo silikambapo zambiri zokhudza iye. Choonadi cha kalatayi ndi chofunikira kwa okhulupirira onse.

**VESI LOTSOGOLERA:** III Yohane 1:11

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Moyo wathu ndi chitsanzo cha ntchito zabwino kapena zoipa kwa anthu amene timakhala nawo.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Yohane, Gayo, Diotrefe ndi Demetriyo.

#### **MAGAWO**

I. Mawu oyamba: 1-2

- A. Kuchokera kwa: Mkuluyo, Yohane: 1
- B. Kupita kwa: Wokonedwa Gayo: 1
- C. Khumbo la Yohane pa iye: Kuti alemere kuthupi monganso mzimu wake ali wolemera: 2

II. Ubale wa okhulupirira ndi choonadi: 3-4

- A. Ukuyenera ukhazikike mwa iwo: 3
- B. Akuyenera kuyenda mu choonadi: 3
- C. Tikamayenda mu choonadi, timabweretsa chimwemwe kwa atsogoleri athu a kuuzimu: 4

III. Ubale wa okhulupirira ndi akhristu ena: 5-8

- A. Ayenera kutumikira abale ndi alendo: 5
- B. Ayenera kudziwika kumpingo pa zachikondano chawo pa abale: 6
- C. Ayenera kuthandiza anzawo pa choonadi: 8

IV. Ubale wa okhulupirira ku zabwino ndi zoipa: 9-12

A. Diotrefe ngati chitsanzo choipa: 9

1. Adayesera kukhala malo otsogolera.
2. Adakana kumulandira Yohane, mtsogoleri osankhidwa ndi Mulungu.
3. Adalankhulira atumwi mwano (utsogoleri).
4. Osakhutitsidwa.
5. Adapatula okhulupirira ena (gulu la anthu ochepe).
6. Adayesera kuchotsa mu mpingo okhulupirira amene samagwirizana ndi utsogoleri wa mpingo wosankhidwa ndi Mulungu.

B. Zoyenera kuchita pa zoipa izi: 11

1. Londolani chimene si choipa, chifukwa amene achita zoipa sanaona Mulungu: 11
2. Londolani chimene ndi chabwino, pakuti iye amene achita chabwino ali wa kwa Mulungu: 11

C. Demetriyo: Chitsanzo cha munthu wabwino: 12

1. Anthu ambiri anamuchitira umboni.
2. Amayenda mogwirizana ndi Mawu a Mulungu.
3. Anali ndi mbiri yabwino ya utsogoleri wosankhidwa ndi Mulungu.

V. Mawu otsiriza: 13-14

A. Yohane anali ndi zinthu zambiri zoti alembe, koma adayembekezera kuwayendera: 13-14

B. Akutumiza: 14

1. Mtendere.
2. Mawu otsiriza kuchokera kwa abwenzi kupita kwa Gayo ndi mpingo.

C. Akumfusa Gayo kuti apereke moni kwa abwenzi ake mu dzina lake: 14



## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba mabuku a I, II ndi III Yohane ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la I John.

---

---

---

3. Kodi buku la I Yohane amalemba kwa ndani?

---

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la I Yohane.

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la I Yohane kuchokera pamtima.

---

---

---

6. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la II Yohane.

---

7. Kodi buku la II Yohane amalemba kwa ndani?

---

8. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la II Yohane.

---

---

9. Lembani vesi lotsogolera la II Yohane kuchokera pantima.

---

---

---

10. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la III Yohane.

---

---

11. Kodi buku la III Yohane amalemba kwa ndani?

---

12. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la III Yohane.

---

---

13. Lembani vesi lotsogolera la buku la III Yohane kuchokera pantima.

---

---

---

**(Mayankho onse a mafunsowa ali kumapeto kwa bulkuli)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Phunzirani zinthu zonse zimene mukuyenera kudziwa molingana ndi I Yohane. Pofuna kuphunzira koyamba werengani I Yohane ndi kudula mzere mawu oti “dziwa” ndi “kudziwa” mmene agwiritsidwira ntchito. Keneko bwererani mmbuyo ndipo pa zimene mwadula mzerezo lembani mndandanda wa zinthu zimene tiyenera kuzidziwa.
2. Lembani zinthu zimene alembera anthu awa mu I Yohane 2:12-14
  - Ana
  - Atate
  - Achinyamata
  - (Iyi ndi milingo ya kukula mu uzimu)
3. Werengani I Yohane ndipo onetsetsani mmene agwiritsira ntchito mawu monga chikondi ndi choonadi. Lembani mwachidule za zimene mawuwa akuphunzitsa.
4. Lembani mndandanda wa zikhalidwe zoipa za Diotrefe zimene zikupezeka mu III Yohane 9-10.
5. Phunzirani zikhalidwe za okhulupirira obadwa mwatsopano: I Yohane 2:29; 3:9; 4:7; 5:1,4,18
6. Phunzirani mayesero asanu ndi awiri amene okhulupirira enieni amakumana nawo: I Yohane 1:6,8,10; 2:4,6,9; 4:20
7. Magawo osavuta a buku la I Yohane ndi:
  - Chaputala 1-2      Mulungu ndiye kuunika
  - Chaputala 3-4      Mulungu ndiye chikondi
  - Chaputala 5      Mulungu ndiye Moyo
8. Werengani kusiyana kwa zinthu izi mu I Yohane:
  - Kuunika ndi mdima: 1:5-2:11
  - Atate ndi dziko: 2:12-17
  - Khristu ndi wokana Khristu: 2:18-28
  - Chabwino ndi choipa: 2:29-3:24
  - Mzimu Woyera ndi cholakwa: 4:1-6
  - Chikondi ndi kuyerekeza: 4:7-21
  - Kubadwa mwa Mulungu ndi zina: 5:1-21

## CHAPUTALA CHA 20

### YUDA

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Yuda.
- Kudziwa amene amawalemba buku la Yuda
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la Yuda
- Kulemba vesi lotsogolera la buku la Yuda kuchokera pamtima
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Yuda

### MAWU OYAMBA

**WOLEMBA:** Yuda (mbale wake wa Yesu)

**OMWE AMAWALEMBERA:** Akhristu onse, ngakhale amalemba anthu a ku mpingo wa ku M Asiya.

**CHOLINGA:** Kuchenjeza za aphunzitsi onyenga

**VESI LOTSOGOLERA:** Yuda 1:3

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Tikuyenera kukhala tcheru ndi aphunzitsi onyenga amene apezeka mosayembekezera ndi cholinga chofuna kuchotsa okhulupirira pa choonadi cha Mulungu.

**ANTHU OMWE ATCHULIDWAMO:** Yuda, Kaini, Balamu, Kole, Enoki, Mngelo Mikaye.

### MAGAWO

Dziwani: Buku la Yuda lilibe ma chaputala mu Baibulo. Choncho ndi mavesi okha amene akupezekamo.

I. Mawu oyamba: Moni: 1-2

A. Kuchokera kwa: Yuda: 1

1. Mbale wa Yakobo.
2. Kapolo wa Yesu Khristu.

- B. Kwa iwo amene: 1
  - 1. Ayeretsedwa ndi Mulungu.
  - 2. Osungidwa mwa Khristu.
  - 3. Oitanidwa.

II. Cholinga: 3

- A. Cholinga chochokera pa chiyambi: Chipulumutso cha aliyense.
- B. Cholinga china: Chilimbikitso cha kuti ayenera kulimbana ndi chikhulupiriro chawo chifukwa cha mtundu wa anthu umene unalowa mu mpingo.

III. Makhalidwe a "anthu achilendo" (aphunzitsi onyenga): 4

- A. Analowa mosadziwika.
- B. Adalandira chitsutso.
- C. Anthu osapembedza.
- D. A. kusandutsa chisomo cha Mulungu ndi chonyasa
- E. Okana Ambuye Yesu Khristu.

IV. Mitundu iwiri ya mbiri: 5-7

- A. Israyeli: Atatha kupulumutsidwa, ataonongedwa: 5 (Numenti 13-14 ndi I Akorinto 10:5-10)
- B. Angelo: Adasiya malo awo a poyamba, adawasunga mundende: 6 (II Petro 2:4)
- C. Sodomu and Gomora: Chifukwa cha chilakolako ndi dama adalangidwa ndi moto: 7 (Genesis 18-19)

V. Mmene aphunzitsi onyenga analili: 8-10 (akuwalongosola mpakana vesi 4)

- A. Olota zonyasa: 8
- B. Odetsa matupi awo: 8
- C. Opeputsa ufumu: 8
- D. Ochitira mwano ulemerero: 8-10
  - 1. Koma Mikayeli Mngelo sadafune kulankhula zoipa za Mdierekezi: 9
  - 2. Anthuwo amalankhula za zoipa zimene samazidziwa: 10
- E. Ataika mu zinthu za chibadwidwe: 10

VI. Zitsanzo za anthu oipa: 11

- A. Adapita: Monga njira ya Kaini: Adakana mwazi ngati njira yokhululukira machimo:

(Genesis 4)

- B. Adathawa: Atangolakwa Balamu: Utumiki wofuna ndalama: (Nomeri 22-24)
- C. Adatayika: Mu chitsutsano cha Kole: Kukana utsogoleri woikidwa ndi Mulungu: (Nomeri 16)

VII. Kuipa kwa anthu pofanizira ndi zinthu zina (kufanizira ndi zitsanzo za chilengedwe): 12-13

- A. Mawanga: Kutanthauza kuti "miyala" mmaphwando anu; mwala mu chakudya: 12
- B. Mitambo yopanda madzi: Kulonjeza zambiri koma osachita kanthu; kutengeka mosavuta: 12
- C. Mitengo yakufa: Yopanda zipatso, Yopanda mitsitsi mkukhazikika; okufa kawiri: koyamba mu uchimo ndi mu chinyengo: 12
- D. Mafunde oopsa: Aphokoso, opokosera, koma osachita kanthu: 13
- E. Nyenyezi zosokera: zooneka zowala, koma zopereka mdima: 13

VIII. Chiweruzo cha mtsogolo: 14-15 (Genesis 5:18-24)

- A. Mnthenga: Enoki: 14
- B. Uthenga: 15
  - 1. Oweruzidwa ndi Ambuye ndi oyera mtima zikwi makumi: 14
    - a. Pa ntchito zawo zosapembedza zimene anachita: 15
    - b. Pa mawu ao onse analankhulira Mulungu: 15

IX. Makhalidwe a anthu oipa: 16

- A. Odandaula.
- B. Owilingula.
- C. Akutsata zilakolako zawo.
- D. Pakamwa pawo polankhula zotukumuka.
- E. Ochitira ulemu anthu, poganiza kuti ena ndi abwino kuposa ena chifukwa cha chuma, maudindo ndi zina.

X. Kumbukirana: Yesu adawachenjeza kale anthuwa: 17-19

- A. Onyoza azadza mmasiku otsiriza: 18
- B. Adzachita molingana ndi zilakolako zawo: 18
- C. Adzadzisiyanitsa okha (mmagulu ang'ono): 19
- D. Adzakhala ndi makhalidwe a chibadwidwe: 19
- E. Sadzakhala ndi Mzimu wa Mulungu: 19

XI. Njira zinayi zopewera chinyengo cha anthu oipawa: 20-21

- A. Kudzimangira nokha mu chikhulupiriro: 20
- B. Pempheperani mu mzimu: 20
- C. Mudzisunge nokha mu chikondi cha Mulungu: 21
- D. Yembekezerani kubwera ka Ambuye Yesu Khristu: 21

XII. Zimene tingachite kwa anthu oyipawa: 22-23

- A. Ena muwachitire chifundo: 22
  - 1. Onetsani kusiyana pakati pa ofooka ndi iwo amene achita choipa mwachifuniri chawo (onani vesi 23).
- B. Ena muwapulumutse ndi mantha: 23
  - 1. Muwakwatule ku moto wa uchimi/gehena, Akwatuleni, musakhale nawo mmachimo awo.
  - 2. Danani nawo Malaya awo a mawanga ndi thupi.

XIV. Nyimbo yotsiriza: 24-25

- A. Zimene atichitira tsopano: Ndi wokutha kutisunga kuti tisagwe: 24
- B. Zimene adzachita mtsogolo: Kutipereka kuti tikhale opanda banga: 24
  - 1. Pamaso pa ulemerero wake.
  - 2. Ndi chimwemwe chachikulu.
  
- B. Kwa Mulungu yekha, wanzeru ndi mpulumutsi, tsopano ndi masiku onse kukhale: 25
  - 1. Ulemerero.
  - 2. Ukulu.
  - 3. Ulamuliro.
  - 4. Mphamvu.

## MAFUNSO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Yuda ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la Yuda.

---

---

---

3. Kodi buku la Yuda amalemba kwa ndani?

---

---

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la Yuda.

---

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Yuda kuchokera pamtima.

---

---

---

**(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa bukuli)**



## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Lembani chikhalidwe cha aphunzitsi onyenga omwe akupezeka mbuku la Yuda
2. Werengani zitsanzo za muchipangano chakale zomwe zikupezeka mu buku la Yuda:
  - Israyeli adatuluka mu Aigupto kenako adaonongedwa: Numeri 13-14; I Akorinto 10:5-10; Ahebri 3:17
  - Angelo amene sadasunge malo awo oyamba: II Petro 2:4
  - Sodomu ndi Gomora: Genesis 18:1-19:24
  - Kaini: Genesis 4
  - Balamu: Numeri 22-24
  - Kola: Numeri 16
  - Enoki (Mbadwo wa chisanu ndi chiwiri wochokera kwa Adamu): Genesis 5:18
3. Werengani Yuda 20-23. Lembani mndandanda wa zinthu zimene mungazitetezere kwa aphunzitsi onyenga malingana ndi buku la Yuda.
4. Werengani malamulo akupezeka mbuku la Yuda:
  - Chitani nkondo ndi chikhulupiro chaanu: 3
  - Kumbukirani mawu a atumwi: 17
  - Dzimangireni nokha mu chikhulupiro: 20
  - Pempheperani mu mzimu
  - Yang'anirani chifundo cha Yesu
  - Dzitsungeni nokha mu chikondi cha Mulungu
  - Bweretsani kusintha
  - Chitirani ena chifundo
  - Pulumutsani ena ndi mantha
  - Akwatuleni pa moto
  - Danani ndi chovala cha kuthupi
5. Mawu amodzi ofunikira omwe akupezeka mu buku la Yuda ndi “osapembedza”. Anagwiritsa ntchito mawuwa pofuna kukamba za anthu, zilakolako, ntchito, kudzipereka, ochimwa ndi zolankhula.
6. Onani ubale umene ulipo pakati pa Yuda ndi II Petro:

<b>Jude</b>	<b>II Peter</b>
4	2:1-3
6	2:4
7-10	2:6-12
11	2:15
12-13	2:13-17
16	2:18
17-18	3:1-3

## **MAWU OYAMBA A BUKU LA UNENERI**

Chibvumbulutso ndi buku lokhalo la uneneri mu Chipangano Chatsopano. Limapereka chithunzithunzi cha mtsogolo mu dongosolo la Mulungu, kuphatikizapo za chimaliziro cha nthawi monga mmene tikudziwira, za kulengedwa kwa kumwamba kwatsopano ndi dziko latsopano, za chiweruzo, ndi chiyambi cha umuyaya.

## CHAPUTALA CHA 21

### CHIBVUMBULUTSO

#### ZOLINGA:

Pakutha pa phunziro ili muyenera:

- Kutchula yemwe analemba buku la Chibvumbulutso.
- Kudziwa komwe buku la chibvumbulutso amalemba.
- Kutchula cholinga chimene amalemba buku la chibvumbulutso
- Kulemba vesi lotsogolera la chibvumbulutso kuchokera pamtima
- Kutchula moyo ndi mfundo ya utumiki ya buku la chibvumbulutso

#### MAWU OYAMBA

#### WOLEMBA: Yohane

**OMWE AMAWALEMBERA:** Mipingo isanu ndi iwiri ya m Asiya ndi okhulupirira onse

**CHOLINGA:** Kuulula dongosolo la Mulungu la dziko

**VESI LOTSOGOLERA:** Chibvumbulutso 1:19

**MOYO NDI MFUNDO YA UTUMIKI:** Kumapeto kwa zonse, chabwino chidzagonjetsa choipa. Nthawi zonse Mulungu amakwaniritsa madongosolo ndi zolinga zake zokhazikika.

**ANTHU OMWE AKUTCHULIDWAMO:** Yohane, Wokana Khristu, Mneneri onyenga, Yesu Khristu.

### MAGAWO

#### Gawo Loyamba: Zakale: “Zinthu zimene wazona”

I. Mawu oyamba: 1:1-3

II. Kupereka moni: 1:4-6

III. Mutu waukulu wa Chibumbulutso: 1:7-8

IV. Wolembe: Yohane 1:9-10

IV. Masomphenya a Yohane a Ambuye: 1:10-18

- A. Umunthu wake: Alefa and Omega, Ambuye: 1:11
- B. Malo ake: Pakati pa mipingo (zoikapo nyali): 1:12-13
- C. Chikhalidwe chake: 1:13-16
- D. Uthenga wake: 1:17-20

**Gawo Lachiwiri: Zatsopano: "Zinthu zimene zilipo"**

I. Mauthenga ku mipingo: 2:1-3:22

- A. Efeso: 2:1-7
- B. Smurna: 2:8-11
- C. Pergamo: 2:12-17
- D. Tiyatira: 2:18-29
- E. Sarde: 3:1-6
- F. Filadelfeya: 3:7-13
- G. Laodikaya: 3:14-22

Gawo Lachitatu: Mtsogolo: "Zinthu zimene zidzachitike mtsogolo"

I. Mmene zidzachitikira zinthu mu nthawi yotsiriza: 4:1-5:14

- A. Mpando wa chifumu wa Mulungu: 4:1-11
- B. Buku lolembedwa: 5:1-5
- C. Mwana wa nkhosa: 5:6-14

II. Mkwiyu wa mwana wa nkhosa: 6:1-19:21

A. Zosindikiza zisanu ndi ziwiri za chiweruzo: 6:1-11:19

- 1. Chosindikiza choyamba: 6:1-2
- 2. Chosindikiza chachiwiri: 6:3-4
- 3. Chosindikiza chachitatu: 6:5-6
- 4. Chosindikiza chachinayi: 6:7-8
- 5. Chosindikiza chachisanu: 6:9-11
- 6. Chosindikiza chachisanu mchimodzi: 6:12-17
- 7. Nyengo ya zochitika: 7:1-17
  - a. Pa dziko lapansi: Kusindikiza chizindikiro cha akapolo a Mulungu: 7:1-8
  - b. Kumwamba: Kuimba nyimbo kwa akapolo a Mulungu: 7:9-17

8. Chosindikiza cha chisanu ndi chiwiri: 8:1-11:19. Chosindikiza ichi chinali ndi malipenga asanu ndi awiri:

- a. Lipenga loyamba: 8:7
- b. Lipenga lachiwiri: 8:8-9
- c. Lipenga lachitatu: 8:10-11
- d. Lipenga lachinayi: 8:12-13
- e. Lipenga lachisanu: 9:1-12
- f. Lipenga lachisanu mchimodzi: 9:13-21
- g. Nthawi ya zochitika: 10:1-11:14.

Zinthu zisanu ndi ziwiri zikuchitika pakati pa chinthu cha chisanu ndi chimodzi ndi malipenga asanu ndi awiri.

- h. Lipenga lachisanu ndi chiwiri: 11:15-19

III. Ulamuliro wa Satana pa dziko lapansi: 12:1-13:18

A. Satana ndi Israyeli: 12:1-17

B. Satana ndi dziko: 13:1-18

IV. Mbale zisanu ndi ziwiri za chiweruzo: 14:1-16:21

A. Zochitika zina zisanabwere chiweruzo: 14:1-15:8

B. Mbale za chiweruzo: 16:1-21

1. Mbale yoyamba ya chiweruzo: 16:2
2. Mbale yachiwiri ya chiweruzo: 16:3
3. Mbale yachitatu ya chiweruzo: 16:4-7
4. Mbale yachinayi ya chiweruzo: 16:8-9
5. Mbale yachisanu ya chiweruzo: 16:10-11
6. Mbale yachisanu mchimodzi ya chiweruzo: 16:12-16
7. Mbale yachisanu mchimodzi ya chiweruzo: 16:17-21

V. Kupasuka kwa chipembedzo cha padziko lapansi: 17:1-18

A. Za mu mbiri: 17:1-6

B. Zamtsogolo: 17:7-18

VI. Kupasuka kwa maulamuliro ndi chuma cha dziko: 18:1-24

VII. Kugonjetsedwa kwa adani a Mulungu pa nkondo ya Halmagedo: 19:1-21

A. Chisangalalo cha Mmwamba: 19:1-10

B. Kubwera pa dziko lapansi: 19:11-21

VIII. Chiweruzo cha anthu amitindu: 20:4-15

A. Ku moyo: 20:4-10

B. Ku imfa: 20:11-15

IX. Miyamba kwatsopano ndi dziko latsopano: 21:1-22:5

A. Maonekedwe ake: 21:1-8

B. Mmene Yerusalemu watsopano alili: 21:9-22:5

X. Machenjezo ndi malonjezo: 22:6-21

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kodi analemba buku la Chibvumbulutso ndi ndani?

---

2. Tchulani cholinga chimene amalemba buku la Chibvumbulutso.

---

---

---

3. Kodi buku la Chibvumbulutso amalemba ndani?

---

---

4. Tchulani moyo ndi mfundo ya utumiki ua buku la Chibvumbulutso.

---

---

---

5. Lembani vesi lotsogolera la buku la Chibvumbulutso kuchokera pamtima.

---

---

---

**(Mayankho a mafunsowa ali kumapeto kwa phunziroli)**

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

1. Mu buku la Chibvumbulutso muli madalitso asanu ndi awiri amene akutchulidwamo:
  - Wodala iye amene awerenga chinenero: 1:3
  - Wodala ndi iwo amene akufa mwa Ambuye: 14:13
  - Wodala iye amene adakilira za kubwera kwake: 16:15
  - Wodala ndi iwo amene aitanidwa ku phwando la ukwati wa mwana wankhosa
  - Wodala ndi iye amene achita nawo pa kuuka koyamba
  - Wodala ndi iye amene asunga mau a chinenero cha bukuli
  - Wodala ndi iwo amene atsuka miinjira yawo.
  
2. Werangani mmene ziwanda azilongosolera mu Chibvumbulutso chaputala cha 19.
  
3. Werangani mkumano waukulu wa mapemphero a anthu osapulumsidwa mu mbiri: 6:15-17
  
4. Mawu omaliza amene Yesu analankhula ku mpingo akupezeka mu chaputala 2 ndi 3.
  
5. Yohane amene analemba buku la Chibvumbulutso, ndi amene analembanso uthenga wabwino wa Yohane, ndi I, II ndi III Yohane. Werangani zina zimene analemba. Yohaneyi anali wophunzira wa Yesu. Mukhoza kuwerenga zambiri zokhuza iye mu uthenga wake wabwino.
  
6. Mukuyenera kumaonako buku la Danieli pamene mukuwerenga Chibvumbulutso. Dziwani zina mwa zimene zikupezeka ku Danieli:
  - Zokhuza Israyeli: Danieli 3 ndi 6, ndi Chibvumbulutso 12
  
  - Zokhuza okana Khristu: Danieli 3:1-7; 7:7,8,24,25; 8:9-12, 23-25; 9:27; 11:36-45; ndi Chibvumbulutso 13
  
  - Zokhuza chitsautso chachikulu: Danieli 9:24-27; Chibvumbulutso 11:2, 12:6,14; 13:5
  
  - Danieli anali buku lotsekedwa: Danieli 12:9. Kutanthauza kuti chilichonse chokhudza tsogolo sichimayenera kuululika pa nthawi imeneyo.
  
  - Chibvumbulutso ndi buku losatsekedwa (Chibvumbulutso 22:10). Linalembedwa kuti likwanilitse vumbulutso la munthu mu dongosolo la Mulungu.



7. Baibulo limatchulapo za akolona osiyasiyana amene adzapatsidwe kwa okhulupirira

- Kolona osonongeka: I Akorinto 9:25
- Kolona wa chimwemwe: I Atesalonika 2:19-20
- Kolona wa chilungamo: II Timoteo 4:8
- Kolona wa ulemerero: I Petro5:2-4
- Kolona wa moyo: Chibvumbulutso 2:10

8. Werengani mauthenga amene amapita ku mipingo isanu ndi iwiri mu Chibvumbulutso chaputala 2 mpaka 3. Pezani pepala ndi lembani izi zokhuza mipingoyo:

Dzina la mpingo: Kumene uthenga umapita. Mpingo uliwonse watchulidwa  
Zimene amafotokoza: uthenga uliwonse umafotokoza zokhuza Ambuye Yesu Khristu.  
Kuchita bwino kwawo: Lembani makhalidwe abwino amene Ambuye analankhula.  
Lamulo: Mu uthenga uliwonse, Ambuye amawapatsa lamulo ndi populumukira pa mavuto a mpingo  
Lonjezo: Lonjezo likuperekedwa ku mpingo uliwonse ndi cholinga chofuna kulimbikitsa mmachitidwe ake.

9. Buku la Chibvumbulutso lili ndi mayina ambiri a Yesu kuposa mabuku ena onse a Mbaibulo. Mayinawa ndi awa ali mmusimu. Kodi mungathe kupezako ena?

- Yesu Khristu: 1:1
- Mboni yokhulupirika: 1:5
- Wobadwa woyamba wa akufa: 1:5
- Mkulu wa mafumu a dziko lapansi: 1:5
- Alefa ndi Omega: 1:8
- Woyamba ndo wotsiriza: 1:17
- Mwana wa munthu: 1:13
- Mwana wa Mulungu: 2:18
- Wosunga mafungulo a Davide: 3:7
- Wosunga mafungulo a imfa ndi hade: 1:18
- Mkango wa a yuda: 5:5
- Muzu wa Davide: 5:5
- Mwana wankhosa wophedwa: 5:6
- Mwanawankhosa wamkwiyo: 6:16-17
- Mwanawankhosa oweta: 7:17
- Ambuye wathu: 11:8
- Mwana wa mamuna: 12:5
- Mfumu ya oyera mtima: 15:3
- Wokhupirika ndi woona: 19:11

- Mawu a Mulungu: 19:13
- Mfumu ya mafumu: 19:16
- Mbuye wa ambuye: 19:16
- Woyamba ndi wotsiriza: 22:13
- Nyenyenzi yonyezimila ya nthanda: 22:16

10. Tchati lili mmusimu lingakuthandizeni kumvetsa nkhondo zokhazikika zitatu zimene Baibulo limatiuza.

Ochita nkhondo	Nthawi yake	Zotsatira zake	Mabuku ake
1 Rusa ndi anzawo	Chisanafike chitsautso Kapena chilimkati. Zikhoza Kuchitika nthawi iliyonse	Mulungu adzalowelera ndipo asilikali a Rusa adzaonongedwa	Ezekieli 38:1-39:16
2 Asilikali a mmaiko Amene sadziwa Mulungu	Kumapeto kwa zaka zisanu ndi ziwiri za chisautso	Yesu atsika mkuononga adani onse	Yoweli 3:9,12 Zakaliya 14:1-4 Chibvu. 16:13-16, 19:11-21 Chibvu. 20:7-10
3 Satana ndi Mulungu Chikwi za ufumu	Patatha zaka	Satana ndi a minthenga Aponyedwa Mnyanja Ya moto	

11. Werengani kusiyana pakati pa chiyambi ndi chitsiridzilo cha dziko:

**Chiyambi (Alefa)**  
**Genesis chaputala 1 mpaka 3**

Mulungu analenga kumwamba  
ndi dziko lapansi 1:2  
Kukhale kuwala: 1:3-5  
Madzi anatchedwa nyanja: 1:10  
Mtengo wa moyo: 2:8-9  
Mtsinje wotuluka mu Edeni: 2:10  
Imfa ya ku mtengo: 2:17  
Padaikidwa themberero: 3:17  
Zowawa: 3:17

**Chitsirizilo (Omega)**  
**Chbumbulutso chaputala 20 mpaka 22**

Ndinaona miyamba yatsopano ndi  
ndi dziko latsopano: 21:1  
Mzinda sunafune kuwala: 21:23; 22:5  
Kunalibe nyanja: 21:1  
Mtengo wa moyo: 22:2  
Mtsinje woyera wa moyo: 22:1  
Moyo wochokera ku mtengo: 22:2  
Kunalibe Themberero: 22:3  
Kopanda zowawa: 21:4

Khoma lidatsekedwa: 3:24  
Adayenda nawo limodzi: 3:8  
Imfa idaikidwa: 2:17  
Satana adanyenga: 3:4-6  
Satana adamasulidwa: 3:4  
Chisoni: 3:17  
Dziko ndi kumwamba zikhala: 1:1  
Mphamvu ya Mulungu yolenga: 1:1  
Kubisala pamaso pa Mulungu: 3:8  
Zinayamba: 1:1

Khomo lotsekula: 21:25  
Adakhala nawo limodzi: 21:3  
Imfa idachotsedwa: 20:14  
Satana sadanyenge: 20:3  
Satana adamangidwa: 20:2  
Kopanda chisoni: 21:4  
Dziko ndi kumwamba zopanda kanthu: 20:11  
Mphamvu ya Mulungu yoononga: 20:9  
Kuimirira pamaso pa Mulungu: 20:12  
Zachitika: 21:6

### **PAMETHERO**

Baibulo limaulula dongosolo lalikulu la Mulungu. Koterokuti Chipangano Chakale ndi chikonzekero cha dongosololi. Mabuku a uthenga wabwino amaonetsera dongosololi, ndipo Machitidwe ndi Makalata ndi amene amakwaniritsa dongosololi. Pomwe Chibvumbulutso akuonetsera chimaliziro chake cha dongosolo la Mulungu.

## **MAYANKHO A MAYESO ODZIYESA NOKHA**

### **CHAPUTALA 1**

1. Mateyu
2. Kupereka utumiki wa Yesu, makamaka ngati mfumu ya Ayuda
3. Kwa okhulupirira onse ngakhala amalemba kwa a Chiyuda kumene amafuna kumuonesta Yesu ngati Mesiya, Mwana wa Davide.
4. Lamulo lotsiriza la Yesu kwa ophunzira ake linali kupita kwa anthu amitundu yonse kukalalikira uthenga wabwino.
5. Chifukwa chake mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira chimariziro cha nthawi ya panso pano. (Mateyu 28:19-20).

### **CHAPUTALA 2**

1. Marko
2. Kuonetsera utumiki wa Yesu, potsindika ntchito yake ngati mtumiki ndi Mwana wa munthu.
3. Kwa okhulupirira onse, ngakhale oyambirira anali Achiroma kumene Yesu anamudziwa ngati mtumiki.
4. Moyo ndi Mfundo ya Utumiki: Tifunefune kutumukira osati kutumikidwa.
5. Pakuti ndithu, Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la kwa anthu ambiri (Marko 10:45).

### **CHAPUTALA CHA 3**

1. Luka
2. Izi zikupezeka mu Luka 1:1-4. Cholinga kunali kulemba tsatanetsatane wa zokhuza utumiki wa Yesu.

3. Okhulupirira onse, ngakhale koyambirira anali a Helene kumene aanawaonetsera Yesu ngati munthu wangwiro. Komanso akulemba kwa okhulupirira wina wotchedwa Teofilo.
4. Ntchito yathu ya utumiki ndi yofanana ndi ya Yesu. Ndiko kulalikira uthenga wabwino kwa otayika.
5. Pakuti Mwana wa munthu anadza ndi kufunafuna chotaikacho (Luka 19:10).

#### **CHAPUTALA CHA 4**

1. Yohane
2. Kufuna kutsimikiza kuti Yesu anali Mesiya, Mwana wa Mulungu, ndipo kudzero nu chikhulupiriro anthu apeze moyo osatha.
3. Okhulupirira onse, amene Yohane anawaonetsera Yesu ngati Mwana wa Mulungu.
4. Yesu ndi Khristu, Mwana wa Mulungu wa moyo, ndiye amene ali chiyambi cha chipulumutso ndi njira yak u moyo wosatha.
5. Koma zalembedwa izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace (Yohane 20:31).

#### **CHAPUTALA CHA 5**

1. Luka.
2. Izi zikupezeka mu Machitidwe 1:12. Bukuli limakamba za zimene Yesu anapitiliza kuchita ndi kuphunzitsa atangokwera mwa thupi lake la uzimu, ndiwo mpingo.
3. Okhulupirira onse, ngakhale analemberanso kwa munthu wotchedwa Teofilo.
4. Chizindikiro chooneka cha Mzimu Woyera ndi mphamvu yopatsidwa: Mphamvu yotha kukhala mboni ndi cholinga chofuna kufalitsa uthenga wabwino kudziko lapansi.
5. Komatu mudzalandira mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ache a dziko (Machitidwe 1:8).

## **CHAPUTALA CHA 6**

1. Paulo.
2. Amafunu kupereka tanthauzo lenileni la uthenga wabwino mogwirizana ndi chilamulo, uneneri, ndi chosowa cha anthu onse pa kulungamitsidwa mwa chikhulupiriro.
3. Okhulupirira a kwa Aroma.
4. Okhulupirira adzakhala ndi moyo mwa chikhulupiriro.
5. Pakuti Uthenga Wabwino sundichititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu ali yense wakukhulupira; kuyambira Myuda, ndiponso Mhelene. Pakuti m'menemo chaonetsedwa chilungamo cha Mulungu chakuchokera kuchikhulupiriro kuloza kuchikhulupiriro: monga kwalembedwa, Koma munthu wolungama adzakhala ndi moyo ndi chikhulupiriro (Aroma 1:16-17).

## **CHAPUTALA CHA 7:**

1. Paulo.
2. Paulo amathana ndi mavuto amene anampeza ndi mafunso amene anthu a ku Akorinto anafunsa.
3. Okhulupirira a ku Akorinto.
4. Chikondi ndi chifungulo chachikulu cha chipambano pa moyo wa uzimu ndi utumiki.
5. Ndipo tsopano zitsala chikhulupiriro, chiyembekezo, chikondi, zitatatu izi; koma chachikuru cha izi ndicho chikondi (I Akorinto 13:13).
6. Kukhazikitsa ulamuliro wa utumwi wake chinali cholinga chachikulu, komanso panali zinthu zina zofunikira.
7. Okhulupirira a ku Akorinto.
8. Chifooko cha umunthu chimapereka danga kuti mphamvu ya Mulungu iwonekere.

9. Ndipo ananena kwa ine, Chisomo changa chikukwanira; pakuti mphamvu yanga ithedwa m'ufoko. Chifukwa chache makamaka ndidzadzitamandira ndi kukondweratu m'maufoko wanga, kuti mphamvu ya Kristu ikhale pa ine (II Akorinto 12:9).

#### **CHAPUTALA CHA 8:**

1. Paulo.
2. Kukonza ziphunzitso zolakwika za Chiyuda za chilamulo mu mpingo.
3. Okhulupirira a ku Agalatiya.
4. Yesu anatimasula ku chilamulo mkukhala afulu.
5. Kristu anatisandutsa mfulu, kuti tikhale mfulu; chifukwa chache chirimikani, musakodwensho ndi mgori la ukapolo (Agalatiya 5:1).

#### **CHAPUTALA CHA 9:**

1. Paulo.
2. Kudziwitsa okhulupirira za chuma chawo mwa Khristu ndi kuwalangiza za mayendedwe awo mwa Khristu.
3. Kwa okhulupirira a ku Efeso.
4. Okhulupirira ali cholowa cha madalitso (chuma) ndi udindo (mayendedwe) okhuza mayitanidwe awo.
5. Wolemekezeka Mulungu ndi Atate wa Ambuye wathu Yesu Kristu, amene anatalitsa ife ndi dalitso lonse la mzimu m'zakumwamba mwa Kristu (Aefeso 1:3).

#### **CHAPUTALA CHA 10:**

1. Paulo.
2. Kupempha umodzi mu Chikhristu.
3. Mpingo wa ku Filipo.

4. Umodzi mwa Khristu umabweretsa chimwemwe.
5. Kwaniritsani chimwemwe changa, kuti mukalingalire mtima zomwezo, akukhala nacho chikondi chomwe, a moyo umodzi, olingalira mtima umodzi (Afilipi 2:2).

#### **CHAPUTALA CHA 11:**

1. Paulo.
2. Amalimbana ndi nkhani ya ziphunzitso za mu mpingo.
3. Okhulupirira a ku Akolose amene amagawana kalata yawo ndi okhulupirira a ku Laodikaya.
4. Yesu ali zonse mu zonse.
5. Chifukwa chache ngati munaukitsidwa pamodzi ndi Kristu, funani zakumwamba, kumene kuli Kristu wokhala pa dzanja lamanja la Mulungu. Lingalirani zakumwamba osati za padziko ai. Pakuti munafa, ndipo moyo wanu wabisika pamodzi ndi Kristu mwa Mulungu (Akolose 3:1-3).

#### **CHAPUTALA CHA 12:**

1. Paulo.
2. Kutsimikiza kuti Ambuye akubweranso posachedwa: Kuyamikira ndi kuwadandaulira pa chikhulupiriro chawo ndi kukonza ziphunzitso zolakwa. Paulo amayankhaponso za umboni wonama okhuza utumiki wake.
3. Mpingo wa ku Atesalonika.
4. Chitonthozo chikahale pa chiyembekezo chodala cha kubweranso kwa Yesu Khristu.
5. Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka; pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse. Chomwecho, tonthozanani ndi mau awa (I Atesalonika 4:16-18).



6. Kulangiza okhulupirira pamene akudikira kubweranso kwa Ambuye.
7. Mpingo wa ku Atesalonika.
8. Pakuti padzakhala kugwa kwakukulu lisanafike tsiku la Ambuye, choncho ndikofunikira kuphunzitsa ndi kukhala mu chiphunzitso cholama.
9. Munthu asakunyengeni konseko; kuti silifika, koma chiyambe chifike chipatukocho, nabvumbulutsike munthu wosayeruzika, mwana wa chionongeko (II Atesalonika 2:3).

### **CHAPUTALA CHA 13:**

1. Paulo.
2. Paulo amalemba kwa wogwira naye ntchito limodzi Timoteo amene amatumikira ngati mbusa oyembekezera ku mpingo wa ku Efeso. Bukuli limakamba za mavuto ndi zosowa zina zimene mpingo unakumana nawo.
3. Timoteo.
4. Tikuyenera kukhala moyo wa chitsanzo umene tinayitanidwirako.
5. Munthu asapeputse ubwana wako; komatu khala chitsanzo kwa iwo okhulupira, m'mau, m'mayendedwe, m'chikondi, m'chikhulupiriro, m'kuyera mtima (I Timoteo 4:14).
6. Paulo analemba akadali kundende ndi cholinga chofuna kumsimikizira Timoteo kuti atenge udindo wa utumiki umene mtumwi amaupereka kwa iye pamene amayandikira kufa. Paulo amadziwa kuti wasala pang'ono kuphedwa chifukwa cha chikhulupiriro chake.
7. Timoteo.
8. Dongosolo la Umulungu la kuchukitsa uthenga wabwino ndi “aliyense aphunzitse kufikira mmodzi.”
9. Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso (II Timoteo 2:2).

#### **CHAPUTALA CHA 14:**

1. Tito.
2. Kukonza mavuto ndi kukhazikitsa dongosolo la mu mpingo umene unali pa chilumba cha Krete.
3. Tito, Mhelene wotembenuka mtima ndi wogwira ntchito limodzi ndi Paulo.
4. Kuchita ntchito zabwino kokha sikukwanira. Ntchitozo zikuyenera kukhazikika ndi kumangirika pa mfundo za mau a Mulungu.
5. Chifukwa cha ichi ndinakusiya iwe m'Krete, kuti ukalongosole zosowa, nukaike akuru m'midzi yonse, monga ndinakulamulira (Tito 1:5).

#### **CHAPUTALA CHA 15:**

1. Paulo.
2. Kudandaulira Onesimo, kapolo amene anathawa kwa Filemoni koma anasanduka wokhulupirira. Bukuli limatiphunzitsa za umoyo wathu watsiku ndi tsiku za mmene tikhallira ndi anthu. Limaphunzitsa za kukhululukira ndi utumiki wopembedzera.
3. Filemoni, Mkhristu amene amakhala ku Akolose.
4. Mfundo za Chikhristu zikuyenera zizigwiritsidwa ntchito ndi mmene timakhallira ndi anthu ena.
5. Ndikudandaulira chifukwa cha mwana wanga, amene ndambala m'ndende, Onesimo (Filemoni 1:10).

#### **CHAPUTALA CHA 16:**

1. Paulo.
2. Kumuonetsa Yesu ngati wamkulu ndi woposa onse.
3. Okhulupirira a Chiyuda.

4. Yesu ndi mkhalapakati wa pangano labwino lokhazikika pa malonjezano.
5. Koma tsopano iye walandira citumikiro chomveka choposa, umonso ali Nkhoswe ya pangano labwino loposa, limene likhazikika pa malonjezano oposa (Ahebri 8:6).

#### **CHAPUTALA CHA 17:**

1. Yakobo.
2. Kulimbikitsa okhulupirira amene amadutsa mu mayesero chifukwa cha chikhulupiriro chawo.
3. Okhulupirira omwe ena mwa iwo ndi mafuko khumi ndi awiri a Israyeli.
4. Chikhulupiriro ndiwo maziko a ntchito.
5. Pakuti monga thupi lopanda mzimu liri lakufa, koteronso chikhulupiriro chopanda ntchito chiri chakufa (Yakobo 2:26).

#### **CHAPUTALA CHA 18:**

1. Petro.
2. Kuwachenjeza za kuopsa kwa chizunzo chochokera kunja kwa mpingo.
3. A ku ukapolo amene anazunzidwa chifukwa cha chikhulupiriro chawo cha Khristu.
4. Mayankho athu a pachizunzo achokere mu mfundo za zimene mau a Mulungu akunena.
5. Okondedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale chakukuyesani, ngati chinthu chachilendo chachitika nanu: koma popeza mulawana ndi Kristu zowawa zache, kondwerani; kutinso pa bvumbulutso la ulemerero wache mukakondwere kwakukurukuru (I Petro 4:12-13).
6. Kuchenjeza za kuopsa kwa uchimo ndi ziphunzitso zonyenga zochokera mkati mwa mpingo.
7. A Khristu amene anali ku ukapolo, amene akutchulidwa mu I Petro.

8. Zoopsa ziwiri zomwe zinali mu mpingo ndi makhalidwe a uchimo ndi aphunzitsi onyenga.
9. Okonedwa, uyu ndiye kalata wachiwiri ndilemba kwa inu tsopano; mwa onse awiri nditsitsimutsa mtima wanu wooka ndi kukukumbutsani; kuti mukumbukile mau onenedwa kale ndi aneneri oyera, ndi lamulo la Ambuye ndi Mpulumutsi, mwa atumwi anu (II Petro 3:1-2).

### **CHAPUTALA CHA 19:**

1. Yohane
2. Kulongosola makhalidwe a chiyanjano chenicheni mwa Yesu Khristu.
3. A Khristu amene amagwa mumsampha wa chinyengo cha Satana chimene chimaononga chiyanjano chawo ndi Mulungu ndi okhulupirira ena.
4. Chiyanjano chenicheni ndi Mulungu ndi okhulupirira ena chakhazikika pa mawu a Mulungu ndipo chimasungidwa ndi mfundo ya kuvomereza tchimo.
5. Tikati kuti tiribe uchimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe choonadi. Ngati tibvomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire machimo athu, ndi kutasambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse (I Yohane 1:8-9).
6. Kulimbikitsa okhulupirira kuti akhale okhulupirika ku ziphunzitso zolama, ndi kuwachenjeza za za aphunzitsi onyenga.
7. Kwa “Mkazi osankhidwa ndi ana ake,” zimene zikutanthauza mpingo ndi ziwalo zake.
8. Tikuyenera kudziyang’anira kwa aphunzitsi onyenga amene amatichotsera makhalidwe a uzimu amene tawapeza ndi kutipanga kukhala ochita nawo zoipa zawo.
9. Yense wakupitirira, wosakhala m'chiphunzitso cha Kristu, alibe Mulungu; iye wakukhala m'chiphunzitso, iyeyo ali nao Atate ndi Mwana (II Yohane 1:9).
10. Kuyamikira Gayo ndi Demetriyo pa umboni wawo monga Akhristu ndi kudzudzula makhalidwe omwe si a Khristu a Diotrefe.

11. Bukuli amalemba kwa munthu wotchedwa Gayo. Ndipo analemberanso kwa iye ndi mpingo umene amasonkhana nawo. Choonadi cha kalatayi ndi choyenera kwa okhulupirira onse.
12. Moyo wathu umakhala chitsanzo cha ntchito zabwino kapena zoipa kwa anthu amene timakhala nawo.
13. Wokonedwa, usatsanza chiri choipa komatu chimene chiri chokoma. Iye wakuchita chokoma achokera kwa Mulungu; iye wakuchita choipa sanamuona Mulungu (III Yohane 1:11).

#### **CHAPUTALA CHA 20:**

1. Yuda.
2. Kuwachenjeza za aphunzitsi onyenga.
3. Kwa a Khristu onse, ngakhale anthu a munthawi imene amalemba anali a mpingo wa ku m'Asiya.
4. Tikuyenera kukhala tcheru ndi aphunzitsi onyenga amene akwawira pakati pathu mosadziwa ndi cholinga chofuna kupotoza okhulupirira ku choonadi cha Mulungu.
5. Okonedwa, pakuchita changu chonse chakukulemberani za chipulumutso cha ife tonse, ndafulumidwa mtima ine kukulemberani ndi kudandaulira kuti mulimbanetu chifukwa cha chikhulupiriro chapatsidwa kamodzi kwa oyera mtima (Yuda 1:3).

#### **CHAPUTALA CHA 21:**

1. Yohane.
2. Kuvumbulutsa dongosolo la Mulungu la padziko lapansi.
3. Mipingo isanu ndi iwiri yak u m'Asiya ndi okhulupirira onse.
4. Kumapeto a zonse, chabwino nthawi zonse chimagonjetsa choipa. Mulungu nthawi zonse amakwaniritsa dongosolo ndi cholinga chokhazikika.
5. Chifukwa chache lembera zimene unazona, ndi zimene ziripo, ndi zimene zidzaoneka m'tsogolomo (chibvumbulutso 1:19).